

CHIBVUMBULUTSO, MUTU FORO GAWO II



Wokondwa kwambiri kukhalanso muno mmawa uno. Ine ndimangoganiza za momwe kuti chipale ichi... Tsopano, ndipo ngati ife tikanakhala mu Colorado, chipale ichi chikanakhala chofewa kwenikweni ndi chosalala, ndi kukhala pafupifupi forte pansi pa ziro, ndipo inu mukhoza, *phew*, kuwuzira monga choncho, ndi kupita mpaka pansi ku fumbi. Ndipo izo zimakhala choncho nthawi yonse yachisanu. Koma tsopano, monga kuno, mu iyi... yokhala ngati ya pakatikati, pakati pa chigawo, tsopano kumakhala konyowa kwenikweni ndi koterera ndi koyipa, ndipo—ndipo izo zimangowoneka ngati ine—ine ndimakhumba nditangowulukira kutali, ku Arizona, ndi kukadikirira mpaka chilimwe chifike ndipo kenako nkubwerera.

² Umo ndi momwe ife tonse timakhalira ndi chimfine, majeremusi ndi zinthu tsopano zimangokhala pa nthaka ndipo kumaundana kenako kusungunuka, ndipo kenako kuundana kenako kusungunuka. Ndipo izo zimakwera m'mwamba ndipo ife timazipumira izo mkati, ndi kukhala ndi zilonda zapakhosi, kupweteka kwa mutu, ndi ululu ndi kupweteka. Ndipo, mai, mai, ndi nthawi yotani, malo otani.

Koma kuli Dziko kutsidya la mtsinje,
Lomwe amalitcha lokoma nthawizonse lija,
Ndipo ife timangofikira ku Gombe limenero
mwa lamulo lachikhulupiro;
Mmodzi ndi mmodzi ife tikuyandikira
chipatacho,
Kumeneko kuti tikakhale ndi achisavundi,
Tsiku lina adzaliza mabelu agolide amenewo
kwa inu ndi ine.

³ Ndiko kumene ife tikupita Kwathu kuti tikakhale ndiye, sichoncho izo? Ndilo tsiku limene ife tikuliyembekezera.

⁴ Tsopano, usiku wathawu ine ndithudi ndinasangalala nawo maulaliki odabwitsa amenewo ndi zinthu zimene ine ndinazimva kuchokera kwa abale anga. Kodi Pat Tyler ali kuti, iye ali muno mmawa uno? Pat, oh, sindinakuwone iwe utakhala pamenepo uli wamkulu ngati moyo komanso wachirengedwe mochulukitsa kawiri. Ndipo—ndipo ine—ine sindinakuwone utakhala pamenepo. Nthawi yoyamba yomwe ine ndinakhala ndi Pat...ndinamumva Pat akuyankhula;

Ine ndithudi ndinasangalala nazo, ndikutsimikiza kuti tonse tinatero.

⁵ Ndipo kenako m'bale wamng'ono yemwe anapereka umboni wamoto uwo wa ulaliki pano izo ndithudi zimamveka ngati mfuti ya makina ikuwombera. M'bale wina, ine ndinakumana naye, wochokera ku Ohio. Kodi iye ali pano mmawa uno? Penapake muno? M'bale Neville ananenapo za iye kukhala wowombera mofulumira kwambiri.

⁶ Kenako M'bale J. T. Parnell. Ndipo—ndipo ine ndikuganiza iwo sanafike kwa M'bale Beeler. Ndipo kodi iye, M'bale Parnell ali pano? M'bale Parnell, M'bale Beeler? Sindiri wotsimikiza, ine ndimaganza kuti ndinamuwona M'bale Beeler.

⁷ Magetsi awa, awa ndi a... Pamene iwo amanga kachisi watsopano, Ine ndikuyembekeza kuti iwo akonza chinthucho mosiyana, mosiyana pang'ono. Uyu ndi wathu woyamba, woyeserera. Ndipo kotero ife tipeza watsopano, bwanji, ife tikufuna wosiyana pang'ono ndi uyu; inu simungathe kuwona; Ine ndimakonda kachisi kuti amangidwe mokhala ngati motsetserekera pansu munga *chonchi*, omvetsera. Inu mukuyang'ana molunjika kwa omvetsera anu nthawi zonse. Ndiyeno makamaka m'misonkhano ya kuzindikira zamumtima, inu mukhoza kumangopita mozungulira. Mwaona, kumawatenga iwo mozungulira munga *chonchi*, mmbuyo momwe ndi mtsogolo. Ndiyeno, ngakhale inu mukuyenera mutakhala ndi khonde laling'ono loti lituluke, ndi zabwinoko.

⁸ M'bale Littlefield, ngati Billy ali pano, anandiyimbira ine usiku wathawu ndipo iye akutumiza zofotokozera a kachisi amene ine ndinamudalitsa kumeneko, amene amisiri... M'bale Wood, izo zinatengera, ine ndikukhulupirira, madola faivi handiredi basi kuti m'misiri azijambule izo. Ndipo iye—iye akutumiza izo ndi mtengo ndi chirichonse cha zipangizo zonse ndi thuu mwa foro aliyense ndi zakuti mwa zakuti zomwe zimapita mmenemo. Ndipo iye akuzitumiza izo kwa iye, ndipo akufuna kuti abwere; ndipo anati iye apita kwa anthu ocheka matabwa ndi zina zotero ndi kukawona ngati iye sangakhoze kuwapeza iwo kuti apange ku—kucheka munga iwo anachitira pa wake. Kachisi wokongola kwambiri, osati wamkulu kwambiri, koma ndi chimango chokongola.

⁹ Kotero ine ndinamuza iye, ndinati, “Ine—ine ndizipereka izo kwa matrastii ndi madikoni mwamsanga inu mukangozitimiza kwa Billy ndipo—ndipo kenako ife tiwalola iwo kuti awone kuchuluka kwa zomwe akuyenera kuti akhale nazo kuti ayambe kumanga kwawo.”

¹⁰ Iye anati, “Inu mukatero, ine ndikubwera, ndidzavala ovololo ndipo ndidzangokhala nanu pomwepo pa nthawi imeneyo.” M'bale Littlefield ndi munthu wachisomo wotero, munthu wachisomo, wabwino kwambiri.

¹¹ Tsopano, kodi inu nonse mukumverera bwino za zimenezo, kuti muyambe Chaka Chatsopano tsopano? Ameni! Kupita uko mu Chaka Chatsopano. Ife tikufuna kuti tiziziyamba izo bwino, kutumikira Ambuye. Ndi angati amene anadzuka mmawa uno ndi kumuthokoza Iye chifukwa cha chaka chakale ndi zonse zomwe izo zimatanthauza, ndipo anamufunsa Iye, “Muyiwale zammbuyo”? Koteru, ife tinatero pambali pa bedi pamene ife tinadzuka, ndiyeno nkubwera ku gome ndipo kumene kawirikawiri guwa laling’ono la banja, iwo amasonkhana mozungulira gome ndi kupemphera.

¹² Ndipo koteru ife nthawizonse timayesera kuchipanga icho kukhala chizolowezi chomapemphera usiku ife tisanakagone. Ine ndakhala nazo, zimenezo, kuyambira pamene ine ndinatembenuka mtima poyamba. Kudzuka mmawa, ndipo kuli mdima kwambiri komanso kwankhungu kwambiri kuti ine ndiyende, ine—ine sindikudziwa komwe ine ndikupita. Koma ngati ine ndingangomupempha Iye kuti agwire dzanja langa ndi kundilondolera ine tsiku lonse.

¹³ Ndiye ine ndikukumbukira, kutsidya kwa msewu kuno, pamene ine ndinali mnyamata chabe, Billy Paul anali pafupifupi usinkhu wa zaka zitatu, kapena zinayi, ndipo ife tinkakhala kutsidya lina la msewu. Ndipo usiku wina iye ankafuna kumwa madzi, ndipo iwo anali kunja mu khitchini, choviyikira mu chidebe. Ndipo ine ndinati. . . Oh, ine ndinali wotopa kwambiri, ndinali nditagwira ntchito molimba usana wonse ndi kulalikira theka la usiku. Ndipo—ndipo iye anati, “Adadi, ine—ine ndikufuna akumwa.”

¹⁴ Ndipo ine ndinati, “Billy, ingopita mu khitchini momwemo, iwo ali pa tebulo laling’ono.” Ine ndinati. . .

¹⁵ Iye ananyamuka, anatikita mmaso mwake, anayang’ana pamenepo, iye anati, “Adadi, ine ndikuwopa kuti ndipite.” Mukuona?

¹⁶ Ndipo ine ndinati, “Chabwino, ndizo. . . zonse ziri bwino.” Ndinati, “Ingothamanga, wokondedwa, ndi kukamwa. Adadi atopa kwambiri.” Kamtunda pang’ono chabe, pafupifupi ku zenera limenero.

Ndipo iye—iye anati, “Koma ine ndikuwopa kuti ndipite, adadi.” Mukuona?

¹⁷ Chabwino, ine ndinadzuka ndi munthu wamng’onoyo. Ndipo anatambasula ndipo anadzandigwira dzanja langa, ndipo icho chinali chinthu chabwino; ife tinali tisanayende masitepe anayi kapena asanu mpaka iye anagunda chiguduli pamene Meda anali atapaka pansu, ndi pa chidutswa cha matayilosi, ndipo inu mukudziwa momwe izo zimakhallira. Ndipo iye anangokhwekhwereka, koma ine ndinali nditagwira dzanja lake, ndiyeno iye anangondifinya ine molimba chotero. Ndipo kenako ine ndinayima pamenepo pang’ono, ndipo

ine ndinaganiza, “Mulungu, ndiko kulondola.” Mukuona? “Ine sindikufuna kuti ndipange sitepe imodzi popanda Inu kundigwira dzanja langa, chifukwa ine sindikudziwa pamene ine nditi nditerereke.” Inu mukuona? “Ndipo bola ngati ine ndikukhoza kumverera dzanja Lanu lalikulu, lamphamvu litagwira langa, ine ndikudziwa kuti Inu mudzandigwira ine mu nthawi zanga za . . .” Mukuona?

¹⁸ Kotero ine ndimayesera kupanga chizolowezi cha zimenezo, kuti—kuti ndisunge dzanja langa mu Lake. Ndipo nthawi zina ndachitapo zinthu zomwe zimawoneka zachipongwe pamaso panga pomwe, zinthu zotero zimene zimaoneka zosakhala zachirengedwe ku malingaliro a munthu; koma ngati ife tingangozisiya izo zokha, ndimapeza kuti chinali chinthu chokhacho chomwe chikanakhoza kuchitidwa kuti chikhale cholondola.

¹⁹ Inu mukudziwa, zinthu zomwe sizimaoneka zolondola kuno, ngati Mulungu akutsogolerani inu mu zimenezo, izo zidzakhala zolondola kuno kwina kwake, inu mukuona, chifukwa Iye amadziwa momwe angatsogolere. Kotero, powona kuti Iye ndiye chisomo chathu chokwanira mu zonse, ndipo zonse zomwe ife tikuzisowa kapena kuzisamalira ziri mwa Iye, ndiye tiyeni tisiye pambali china chirichonse pambali pa Iye ndi kugwira dzanja la Mulungu losasintha.

²⁰ Ife tinkakonda kuyimba nyimbo pano, ine sindinaimve iyo ikuyimbidwa kwa nthawi yayitali. Tsopano, sindimatha kuyimba ndipo alipo . . . ine sindikuganiza kuti pali alendo alionse limodzi nafe. Kotero ine . . . Nchifukwa chake ine ndimayesera nyimbo zazing’ono izi, inu mukudziwa, chifukwa ine ndimangozikonda izo. Ndipo Gene, ngati iwe utazilola izi zipite kudzera mu tepi imeneyo kunjira kugulu! Tinkakonda kuyimba nyimbo yaying’ono apa:

Nthawi yadzaza ndi kusandulika kwachangu,
Palibe padziko lapansi chosasanthika chomwe
chingayime.

Manga ziyembekezo zako pa zinthu Zamuyaya,
Gwira pa dzanja la Mulungu losasintha!

Ndi angati omwe munayimvapo nyimboyi? Oh,
ndimayikonda iyo, sichoncho inu? Tiyeni tiyesere ndime
yake:

Gwira pa dzanja la Mulungu losasintha!
Gwira pa dzanja la Mulungu losasintha!
Manga ziyembekezo zako pa zinthu Zamuyaya,
Gwira pa dzanja la Mulungu losasintha!

Tiyeni tiyesere ndime:

Pamene ulendo wathu udzatha,
Ndipo kwa Mulungu takhala owona,
Kokongola ndi kowala kwanu mu Ulemerero,

Moyo wako wokwatulidwa udzawuona!
 Gwira pa dzanja la Mulungu losasintha!
 Gwira pa dzanja la Mulungu losasintha!
 Manga ziyembekezo zako pa zinthu Zamuyaya,
 Gwira pa dzanja la Mulungu losasintha!

²¹ Tiyeni tiyime tsopano miniti yokha kwa pemphero, ngati inu mungatero, pamene ife tikukwezera limodzi la manja athu kwa Mulungu ndi kuyimba iyo kachiwiri:

Gwira pa dzanja la Mulungu losasintha!
 Gwira pa dzanja la Mulungu losasintha!
 Manga ziyembekezo zako pa zinthu Zamuyaya,
 Gwira pa dzanja la Mulungu losasintha!

Usasilire chuma chachabe cha dziko lapansi,
 Chomwe chimavunda mwamsanga kwambiri,
 Manga ziyembekezo zako pa zinthu Zamuyaya,
 Izo sizidzatha konse!

²² Atate Akumwamba, pamene ife tikuyima, Ambuye, ife timangokonda kuyimba nyimbo zakale zimenezo, izo zimapita pansu kwambiri mu zigawo za mkati mwa mtima wathu ndi kutulutsa chiwonetsero cha chikondi chathu kwa Inu, Mulungu wamoyo. Ndipo pamene ife tinakweza manja athu, Ambuye, mmawa uno, chinali chikumbutso chaching'ono kuti “Gwirani manja athu, Ambuye.” Pamene ine ndinali kunena za Billy Paul, momwe iye anagwirira pa dzanja langa, iye akanagwa ngati ine ndikanakhala kuti sindinamugwire iye. Ndipo, O Mulungu, ndi nthawi zingati zomwe ife tikanagwa ngati Inu mukanapanda kutigwira dzanja lathu! Kuganiza momwe kuti iye, wopanda amake, monga khanda laling'ono . . . ndi momwe izo . . . momwe kudutsa m'moyo, kuti njira zomwe iye anali atatenga, akanakhala ataphedwa kalekale, koma panali Dzanja lalikulu limene limakhoza kufikira kumene langa silikanakhoza kufikirako, ndi kugwira. Tsopano, ndife oyamikira kwambiri chifukwa cha zimenezo.

²³ Wokondwa kwambiri kudziwa, Ambuye, kuti pamene ife timverera moyo wathu ukulekana ndi thupi ili, kuti pakadali dzanja lomwe ife tikanakhoza kulifikira ndi kuligwira, litilondolera ife kutsidya kwa mtsinjewo. Ife tikukuthokozani Inu chifukwa cha zinthu izi, chitsimikizo ichi, chitsimikizo chodala ichi chimene ife tiri nacho, Nangula wa moyo, zomwe zimatipangitsa ife kukhala okhazikika pamene ife tikuyenda pa ulendo uwu kapena kuyenda ulendo wofunikira kwambiri wamoyo.

²⁴ Ndipo ife tikupemphera, Atate, kuti monga wolemba ndakatulo ananena, “M'bale wokhumudwa, ndi wosweka, powona kukhazikika kwathu (pa muyeso), kuziwona izo, tidzalimbikitsidwanso kachiwiri, kapena kulimba mtima kachiwiri ndi kuyesetsanso”; kudziwa kuti Mulungu wokwanira

mu zonse, ngati ife tipunthwa kapena kugwa, dzanja Lake lalikulu liri pamenepo kuti litithandize ife. Chisomo chake ndi chokwanira.

²⁵ Tsopano ife tikupemphera, Mulungu, kuti ife titero, mmawa uno, tiyambe Chaka Chatsopano mu nyimbo ndi kuyimba ndi kusangalala, ndipo podziwa kuti Mulungu adzatitsogolera ife kudutsa mu ulendo wa moyo ndi kuwoloka mtsinje wa imfa, kupita ku Dziko lolonjezedwalo. Maso athu akuyang'ana kupyola mitsinje yosefukira ya Yordano mmawa uno, kupita kumene minda ya—ya zipatso ndi minda yobiriwira ikukula, ndipo ife tikupemphera, Mulungu, kuti miyoyo yathu igwire masomphenya amenewo ndi kusawalola iwo kuti achoke. Tsiku lina pamene ife tidzayenera kubwera ku mtsinje umenewo kumene iye amawoloka, kuti, monga Eliya wakale, Mwinjiro wa Mulungu udzakantha mitsinje ya imfa ndipo ife tidzayenda popanda mantha. Perekani izi, Ambuye.

²⁶ Tithandizeni ife pamene tikuyandikira Mawu Anu. O Ambuye, ine ndikupemphera kuti Mzimu Wanu Woyera uwadzoze Mawu awa. Ndife kwenikweni osakwanira kuti tiwaphunzitse iwo, posakhala m'phunzitsi. Ife tikudziwa kuti njira yokhayo yomwe ife tingadziwire Iwo ndi kwa M'phunzitsi wamkuluyo kuti abwere ndi kudzatenga Ake—malo Ake okhalamo m'mitima yathu, ndi—ndi kugonjetsa maganizo athu mwa njira yotero (ndi malingaliro athu) mpaka tidzatero... Iye adzamasulira Malemba Opatulika kwa ife. Ife mwaulemu tikudalira pa zimenezo.

²⁷ Ndipo taganizani za zimenezo, Mulungu, Oh, ndi zodabwitsa bwanji kuti Atate wamoyo monga choncho, amene anachokera...ndiko kubadwa komwe kwa Umuyaya, umene ukanadzatsikira kwa anthu achivundi ndi kutithandiza ife, ndipo akanadzabweretsa Mawu Ake ndi kuwapereka Iwo mkamwa mwathu ndi m'mitima ndi m'makutu kuti ife tikhoze kuwamva Iwo ndi kukhala moyo, kuti atiwohole ife ku themberero lomwe ife tinalibe nalo chochita ndi kubwera kwake, Atate, chifukwa izo zinkachitika ndi mtundu wa anthu ndipo ndife mbadwa za limenero—banja loyamba limenero. “Ndipo timabadwira mu tchimo, kuwumbidwa mu kusaeruzika.” Koma Mulungu wolungama ndi wamoyo amadziwa kuti ife tinalibe chochita ndi zimenezo, koma wapanga njira yopulumukirapo ndi kutipatsa ife mwayi wobwera. Ndife okondwa bwanji kuti tabwera ku Nyumba ya Atate!

²⁸ Ife tikupemphera tsopano, kuti Inu mudalitse mpingo wathu kuno, M'bale Neville, wathu—m'busa wathu wolimba, wantchito Wanu wodzichepetsa. Ife tikupempherera madikoni athu ndi matrastii athu, kuti Inu muwapatse iwo chaka chopambana kwambiri chomwe anayamba akhalapo nacho. Perekani izi, Ambuye. Apatseni iwo moyo wautali. Alimbitseni iwo, Ambuye, iwo ndi antchito Anu. Mulole iwo nthawizonse azikhala olimba

pa malo antchito. Dalitsani osonkhana, ma—mamembala, Ana anu okondedwa amene amabwera ku nyumba ino. Mulungu, ife tikutenga moyo wa aliyense wa iwo amene adutsa pakhomo la nyumba iyi. Ife tikuzitenga izo chifukwa cha Inu, Ambuye. Tithandizeni ife kuti tikhale atumiki otero amene angabweretse Mawu mophweka kwambiri ndi moona kwambiri, mwa Mzimu Woyera, kuti iwo adzakhumba kukhala monga Inu, Ambuye. Perekani izi. Chiritsani odwala ndi osautsika amene alowa muno. Ndipo kuzungulira dziko lonse lapansi, perekani izi mu nyumba iliyonse ya Mulungu.

²⁹ Potsiriza, pamene Inu mwatsiriza, Ambuye, mulole ife tilowe mu zipata Zanu, tikhale pansi pa gome lolandiridwa la Mulungu, ndi kudya ndi kukhala pamodzi kupyola m'mibadwo yosatha. Mpaka nthawi imeneyo, mulole tikhale ndi thanzi ndi mphamvu, chisangalalo, chimwemwe, mphamvu ndi nyonga, ndi madalitso a Mzimu Woyera kuti utitsogolere. Ife tikupempha mu Dzina la Yesu. Amen. Mukhoza kukhala pansi.

³⁰ Ine ndikuyamikira nyimbo zabwino izo mmawa uno. Izo. . . Ine ndinangolowa, mu nthawi, ndimayankhula kwa mzanga wabwino, M'bale Skaggs, ndi—ndi M'bale Gene kumbuyo uko, ndi m'bale wina pakhomo; mpaka ine ndinangomva gawo la izo, koma zinali zikubwera pa chojambulira mokongola kwambiri.

³¹ Kodi inu nonse mukusangalala ndi Chivumbulutsolo? Chabwino? Ine ndikukhulupirira mochuluka monga msungwana wanga wamng'ono, Sarah, kumbuyo uko, izo zakhala “zosintha” kwa ine, ndizo basi—ndizo zosintha zikumangochitika mobwerezabwereza. Inu mukudziwa, ndikukhumba ife tikanakhala nawo tsopano mpaka pafupifupi Marichi kapena Epulo, kungoyika lona yayikulu kwambiri kudutsa kumbuyo kuno ndi kumangobwera masana ndi kujambula zithunzi zimenezo ndi tchati chonsecho, ndi kungozikweza mmwamba ndi pansi ngati zotchinga za zenera, inu mukudziwa, monga ine ndakhala ndikulota nthawiyina za kukhala ndi kachisi wamkulu kwinakwake kumene ine ndingakhoze kufikira pansi ndi kukokera chinsalu ichi pansi, kuchokera komwe ku nsanja; ndipo mavumbulutso ndi matanthauzo amene Ambuye andipatsa ine, ndi kutenga cholozera ndi kuyamba kudutsa pamene ndi kuyibweretsa mibadwo iyi kutsika. Ndiye ife tikathana nazo zimenezo, nkuyikweza imodziyo m'mwamba, nkukokera inayo pansi monga *chonchi* ndi kuyamba pa zimenezo, ndi kuziphunzitsa kudzera mu zimenezo. Oh, uko kukanakhala ngati kumwamba pang'ono, sichoncho izo? Kungokhala nyengo yachisanu yonse, kungokhala ndi Ambuye.

³² Zabwino kwambiri kukhala nokhanokha ndi Iye! Inu mukudziwa, ife tinkakonda kuyimba nyimbo, “Pali nthawi zomwe ine ndimakonda kukhala ndekha ndi Khristu Ambuye wanga, ine ndikhoza kumuza Iye mavuto anga onse ndekha.” Mwaona, ndiyo njira yoti muzipezere. Iwo anakonda

kuyimba, Roy Davis, anakonda kuyimba nyimbo yaying'ono, *Kuzemba Kumbali ndi Kukapemphera ndi Yesu*. Chirichonse chimangolozera. . .chirichonse chimene inu mungakhoze kuchiyang'ana nthawizonse chimagwera mmbuyo momwe mu mzere wa Yesu Khristu, sichoncho izo?

³³ Tsopano, pa mibadwo ya mpingo imene ife tinayikamba, masiku eyiti apitawa mu msonkhano. . .Ndiye usiku watha ine ndikuganiza ife tinafika ku ndime ya 2 ya mutu wa 4 wa Chivumbulutso. Ndipo ine ndikuganiza nonse a inu munali pano usiku watha kuti—kuti mumve izo. Ndipo kotero ine. . . mwinamwake ngati ine ndingawerenge ndime kapena ziwiri za izo mmawa uno, ndi. . .Kapena motalika mmene Ambuye adzanditsogolera, ine sindikudziwa. Ine ndatsika mpaka ku ndime ya 6 kapena ya 7 apa, nkhani yaying'ono chabe yomwe ndinalemba pamene ine ndingakhoze kubwerera mmbuyo mu magawo osiyanasiyana a Malemba ndi kuzibweretsa zinthu zimenezo, ndi pamene ine ndinawerenga dzulo.

³⁴ Ndipo tsopano, ife tikupeza, ife tinalekezera usiku watha, ine ndikukhulupirira, pa ndime ya 2, kuyambira pa ya 3, ine ndikuganiza iyo inali. Ndipo ife tinangotsala ndi “Liwu la Lipenga.” Sizinali zolondola izo, “Kuwomba kwa Liwulo”? Ndiloleni ine ndiwerenge zonse kuti ife tibwererenso tsopano:

Zitatha izi ine ndinapenya, ndipo, taonani, khomo linatseguka kumwamba: ndipo liwu loyamba limene ine ndinalimva linali ngati la lipenga likuyankhula ndi ine; limene linati, Kwera kuno, ndipo Ine ndidzakusonyeza iwe zinthu. . . ziyenera kukhalapo kuchokera pano.

Ndipo pomwepo ine ndinali mu mzimu: ndipo, taonani, mpandowachifumu unakhazikitsidwa kumwamba, ndi mmodzi anakhala pa mpandowachifumuwo.

Ndipo iye amene anakhala pa mpando wachifumu. . . iye wokhalapo anali wowoneka ngati. . . yaspi ndi. . . mwala wa sardiyo: ndipo panali utawaleza wozinga mpandowachifumuwo, wowoneka ngati mwala wa emarodi.

³⁵ Tsopano, ili lokongola, oh, phunziro lokongola! Ndipo mmawa uno, basi ine ndisanabwere kuno, ine ndinafika pansa apa mu ndime ya 6, Ine ndinaganiza, “Oh, mai, ine sindingathe kuzipitirira izo, chifukwa apa pali chinachake mu ndime ya 6 iyi Ine ndikufuna anthu onse azimve bwino kwenikweni, ife tikafika ku *zirombo* izi.” Matanthauzo osiyanasiyana a zirombo izi apa, kuyang'ana mmbuyo mu choyambirira, chimodzi chiri mtundu wina wa chirombo, ndipo zirombo zina zinayizo ndi winanso. Chimodzi ndi wa nyama, mu Chigriki, monga “nyama yakuthengo.” Chimodzi chinachi sichinamasuliridwe molondola mu King James, pakuti izo si *zirombo*, ndi “Zolengedwa

zamoyo.” Ndipo momwe Zolengedwa zimenezo, chomwe izo zinali, sanali munthu ngakhalenso sanali Mngelo. Koteru ndi “Zolengedwa zamoyo,” ndi momwe zinali nazo nkhope zinayi ndi zinayi. . . Oh, mai, ife tikubweretsa izo mpaka ku Uthenga, ndi kuzibweretsanso izo ndi kuziyika izo lero mwangwiro basi monga izo ziliri apa. Ndipo, kumbukirani, *foro* ndi nambala yapadziko lapansi. Mukuona? Ndipo ndi phunziro lokongola basi pamenepo, ndipo koteru ine—ndine wotsimikiza ndithu kuti ife sitifika mu zimenezo; mwinamwake ife titero. Koma ndizodabwitsa kwambiri!

³⁶ Ndiye, Ambuye akalola, ndiye ngati ife tiri kuno, mwinamwake Lamlungu likudzali ife tikhoza kudzayesera izo kachiwiri; kuyesera, kutsika, kuwona ngati ife tingamalize mutu wa 4 uwu tisanachoke. Ife sitikudziwabe kwenikweni malo omwe kuyamba koyambirira kudzakhale.

³⁷ Tsopano, ife tikupeza kuti *zitatha*, “Zitatha zinthu izi.” *Zitatha* ankatanthauza kuti “Mibadwo ya mpingo itatha.”

³⁸ Kenako Yohane anayitanidwa kuti akwere pamwamba, “bwera pamwamba pano,” zimene zikutanthauza “kwera kuno.” Iye anamuwonetsa zonse zimene zidzachitike mu dziko la m’ba—m’badwo wa Mpingo. Ndiye itatha mibadwo ya mpingo, ife tikupeza ndiye kuti Yohane anali choyimira cha wokhulupirira woona aliyense amene adzayitanidwa ndi Khristu Kumwamba. Kulondola uko? Kuyitanidwa, “Kwera kuno.”

³⁹ Ndipo ife tikupeza kuti Liwu limene linayankhula kwa iye linali Liwu la lipenga, lomveka, momveka bwino, ndipo linali Liwu lomwelo limene linayankhula kwa iye pano pa dziko lapansi. Mwaona, nthawi yonse pamene Iye anali pakati pa zoyikapo nyali zisanu ndi ziwiri zagolide, Iye ankayankhula kwa . . . kapena *kuchokera*. Oh, ine ndikuzikonda zimenezo, “kuyankhula kuchokera pa zoyikapo nyali.” Mwaona, Iye anali mu zoyikapo nyali, akuyankhula kuchokera kwa izo ku Mpingo Wake. Ndiye pamene m’badwo wa mpingowo unatha, Iye anachoka padziko lapansi ndipo anakwera kupita Kumwamba ndipo Iye anayitana Owomboledwa Ake akwere ndi Iye. Oh, kodi izo sizokongola? Ine—ine. . . Oh, izo zimangopangitsa mtima wanga kulumpha.

⁴⁰ Ndipo kumbukirani, pamene ife tikubweretsa zinthu izi, ine ndikufuna makamaka otembenuka mtima achichepere monga Mlongo Ina pano, kapena, ndi Ina, kani, ndi mwamuna wake, ndi Rodney ndi—ndi mkazi wake, ndi Charlie ndi iwo, kuti mumvetse kuti zinthu izi, ndipo ambiri a inu achinyamata omwe mwangobwera kumene mwa Ambuye, amene simunapite patali kwambiri mpaka panobe, mwangomulawa kumene Iye ndi kuona kuti Iye ndi wabwino ndi wachisomo. Tsopano, zindikirani ichi, kuti zinthu izi zomwe ife tikuziyankhula, zomwe ife tikuyesetsa kuti tichite ndi kuti mukhazikitse

chikhulupiroro chanu, kuti pamene Mulungu anena chirichonse icho chimayenera kuti chichitike. Izo sizingalephere basi! Ziribe kanthu... Zitha kuwoneka ngati ziri mamailosi miliyoni... ndipo sizingakhoze kuchitika, koma Mulungu adzazisuntha izo mozungulira ndi kuzipangitsa izo kuchitika. Ndipo Iye amachita zimenezo kuti akuyeseni inu.

⁴¹ Tayang'anani zimene Iye ananena kwa Abrahamu. "Umutengere mwana wako kuno pamwamba pa phiri ndipo umuphe iye," atatha kumuyembekezera iye kwa zaka twente faivi. Ndipo Iye anati, "Umutengere iye kuno ndipo umuphe iye." Ndipo bwanji...? "Ndidzakupanga iwe tate wa mafuko."

⁴² Ndipo Abrahamu, wa zaka handiredi; mkazi wake, nainte; ndipo mwana wawo yekhayo... Abrahamu anali pafupifupi handiredi ndi fifitini pamenepo. Kotero iye anati, "Kodi iye adzakhala bwanji, bwanji—izo zitheka bwanji? Ngati ine, bambo wokalamba, wachikulire monga ine ndiri, ndipo ndinayembekezera kwa zaka twente fayivi... Inu munandipatsa lonjezo pa sevente faivi, ndipo pano ine ndiri handiredi. Ndipo Sara anali sikisite faivi, ndipo tsopano iye ali nainte. Bwanji? Titabereka mwana uyu... Ndipo Inu munandiuzwa ine komwe kumbuyo uko, zaka twente faivi zapitazo pamene ine ndinali usinkhu wa zaka sevente faivi zakubadwa, Ine ndinali 'kudzakhala ndi mwana' nditatha kukhala ndi Sara zaka zonsezi, ndinali wosabala ndipo iye anali chumba. Kotero motani ndiye? Komabe, Inu munandipangitsa ine wachonde ndipo munamupangitsa iye kukhala wachonde, ndiyeno nkubwera motsatira ndi kudzatipatsa ife mwana uyu. Ndipo ife tamulera iye pano mpaka zaka fifitini, ndipo kudzera mwa mwana uyu Inu munati Mukanadza 'Dalitsa Amitundu ndi mtundu uliwonse wa padziko lapansi,' ndi kundipanga ine tate mpaka wa Amitundu, kundipanga ine tate. Ndiye m'mibadwo imene ikudzayo, Ambuye, kuti Inu mundipange ine tate wa mafuko onse pansu pa thambo kudzera mwa mwana ameneyu. Ndipo kudzera mwa mwana uyu pakanadzabwera Muwomboli, ndipo kudzera mwa Muwomboli ameneyo mukanadzawombola mtundu wonse wa anthu. Inu mudzachita chotani izo, Ambuye?" Limenero silinali lingaliro la Abrahamu, limenero silinali funso la Abrahamu. Kumvera! Sanati, "Inu mudzachita chotani izo?"

⁴³ "Si ntchito yanga. Inu munanena izo, kotero ine ndikudziwa Mawu Anu ndi olondola, ngati Inu mungakhoze kusunga Mawu Anu kwa ine ndipo mukhoza kundiwonetsa ine kuti pamene ndinali usinkhu wa zaka sevente faivi; pamene munandiyitana ine ndi kuti, 'Dzipatule wekha ndipo upite ku dziko lachirendo,' Ine ndakhala mu dziko lino kwa zaka twente faivi. Ndinachoka, bambo wokalamba, ndikukhala ndi mkazi amene ine ndakhala naye kuyambira ali mtsikana, ndi mlongo wanga watheka. Ndiyeno ine ndina-... nthawi yonseyi. Ndipo Inu munandipatsa ine mwana uyu amene Inu munandilonjeza; Ine ndinamulandira

iyе ngati mmodzi wochokera kwa akufa. Ndipo ngati Inu mukuti ‘umuphe iye,’ Ndinu wothekera kumuwukitsanso iye kwa akufa kachiwiri.” Oh, mai! Ndiyo njirayo, ndi zimenezo. Ndipo Iye anatero.

⁴⁴ Ndipo mwamsanga pamene iye anamvera Mulungu mwathunthu, anachotsa tsitsi la Isake pa nkhope yake, anasolola mpeni kuti amuphe mwa...mwana wake yemwe, mwana wake wobadwa yekha. Mulungu anali kutionetsa dongosolo, kutionetsa ife. Kodi Iye anachita zimenezo chifukwa chiyani? Iye sankasowekera kutero. Koma Iye anachita zimenezo kotero kuti inu ndi ine, kuti ife tikakhoze kuyang’ana pa zinthu zimenezi mu tsiku la mdima lowopsya lino kumene mitima ya anthu ili yodzazidwa ndi zoyipa, kuti ife tikhoze kudziwa kuti Mulungu amasunga lonjezo Lake. Ziribe kanthu momwe zikuwonekera kukhala zosakwanira, zingakhale zosatheka bwanji, Mulungu akadaliwe Mulungu ndipo Iye amasunga lonjezo lirilonse limene Iye analipanga.

⁴⁵ Ndicho chimene ine ndikuyesetsa kuti ndinene kwa inu pamene ife tiyima pano mu msonkhano wa machiritso. Kuyima pano, inu mumati, “Ndikudwala.” Ndipo inu... Ndi zosakayikitsa, inu mukudwala. Koma Mulungu amasunga lonjezo Lake! Ndiye Iye atsika pansi. Tsopano, onani, Iye anapanga chitetezero apa kuti Iye—kuti Iye akuchizeni inu. Ndizimene Iye anachita. Tsopano, chinthu chokhacho chimene Iye amakufunsani inu kuti muchite ndi kukhulupirira izo, kugwiritsitsa kwa izo monga momwe Abrahamu anachitira.

⁴⁶ “Chabwino, adokotala akuti ine—ine ndikhala moyo tsiku limodzi lowonjezera.”

⁴⁷ Ine sindikusamala. Ndi zabwino, ndizo zonse zomwe munthu amadziwa, ndizo zopambana zomwe iye amadziwa. Abrahamu akanamulandira bwanji mwana uyu atatha kumugoneka kale iye pamwamba apa, ndipo Mawu a Mulungu anamuza iye kuti “apite akaphe mnyamatayo”? Kodi iye adzazichita bwanji zimenezo? Funsolo si limenero. Mulungu anati chita zimenezo ndipo izo chikukhazikitsa zimenezo. “Kodi ine ndikhala bwino bwanji ndipo adokotala akuti sindingakhale bwino?” Ine...izo si zanga...ine kuti ndifunse; ndi kutenga Mawu a Mulungu. Ndipo mwamsanga pamene izo zawululidwa kwa inu kuti mukhala bwino, ndiye inu—inu mungokumbukira kuti inu mukhala bwino. Palibe chimene chingakulepheretseni inu zimenezo. Uko nkulondola. Mukuona?

⁴⁸ Kotero pamene Abrahamu anamvera kwathunthu...Kodi Iye azichita motani izo? Mphindi yotsiriza, maminiti faivi otsiriza anafika, maminiti atatu otsiriza, maminiti awiri otsiriza, miniti imodzi yotsiriza, masekondi sarte otsiriza, sekondi yotsiriza inafika, pamene dzanja linali kale mmwamba kuti litenge moyo wa mnyamatayo, Mulungu anati, “Imitsa izo

pomwepo. Imitsa izo pomwepo, mwaona. Ine ndaona kuti iwe umandikhulupiriradi Ine. Tsopano, ine ndangochita izi, Abrahamu, kuti ndimuwonetse Branham Tabernacle m’masiku ali mkudzawo, mwaona, za zomwe zikuchitika, kuti iwo akuyenera kundidalira Ine. Iwo sakuyenera kundikaikira Ine konse. Andikhulupirire Ine!”

⁴⁹ Pafupifupi nthawi imeneyo, iye. . . Apa panali nsembe, iye sanayipange iyo pachabe. Ayi, iye sanachite izo pachabe, pakuti pomwepo mwa—mwanawankhosa analira, kankhosa kakang’ono kanali katakodwa m’chipululu mmenemo ndi nyanga. Ndipo ndikangati kamene ife tadutsa mu zimenezo. Kodi mwanawankhosayo inafika bwanji kumeneko? Motani, kudutsa zirombo zonse zakuthengo? Mailosi handiredede kutali ndi chitukuko, pakati pa mikango, nkhandwe, mimbulu, mtundu uliwonse wa nyama zakuthengo kumbuyo uko, pomwe pamwamba pa phiri pamene panalibe madzi kapena udzu, kodi anakachita chiyani kumeneko? Mulungu anamulenga iye, anangomuyika iye kumeneko.

⁵⁰ Ndipo kuti timuwone Iye m’masiku athu amene ife tikukhalamo! Tsopano, mmawa uno ine ndiyenera kuchita zochulukwa kwambiri za—za zinthu zanga kuti ndizinene, kuti ndifike ku chimene ine ndikufuna kuti ndinene. Nchifukwa chake ndikuyikira kumbuyo izi momwe ine ndikuchitira, ndisanayambe pa izi. Ine ndikufuna kuti mumvetse kuti zinthu izi zomwe zimamveka ngati zandekha, izo sizimatanthauza kuti ndi zandekha. Izo zimangobweretsedwa kuti zipereke chitsanzo kwa inu kuti chikhulupiriro chanu chikhale chokhazikika mu chikhulupiriro chimene chiri mwa Khristu, inu mukhoza kupumira pa lonjezo Lake. Chifukwa Mulungu amasunga lonjezo Lake mwangwiro basi monga lingakhoze kukhalira, tsopano kutionetsa ife.

⁵¹ Ndipo tayang’anani pa *Yehova-yire*, yemweyo, amene Abrahamu anamutcha Iye, lomwe mu Chihebri limatanthauza “Mulungu adzadziperekera Yekha nsembe.” Mulungu akhoza kuchita zimenezo. Iye anapanga njira Yake. Ngati Iye anati. . . Iye anamuza Nowa. . .

⁵² Inu munati, “Chabwino, ameneyo anali Abrahamu basi.” Ayi. Iye anawauza onse kudutsa mu m’badwowo, ndipo Iye akunenabe.

⁵³ Iye ananena kwa Nowa kumbuyo uko, kuti, pamene ife tikufika m’mawa uno, “Bwanji, mvula igwa.” Chifukwa panalibe. . . kunalibe konse mtambo mu mlengalenga. Mtsinje wawukulu kwambiri wa madzi unali nthambi kumene Mulungu ankathirira nthaka, kasupe wamng’ono penapake. Umenewo unali mtsinje wawukulu kwambiri wa madzi umene unalipo.

⁵⁴ Tsopano, anthu amati, “Kodi mu dziko madzi adzatsika bwanji kuchokera kumwamba uko? Ndisonyezeni ine kumene

iwo ali kumwamba kumeneko mu dzuwa lonse lotentha ilo, ngati kulibe aliwonse pamwamba apo.”

55 “Ngati Mulungu anati, ‘manga chombo, kuti iyo ikudza,’ ndi ntchito yanga kuti ndimange chombo ndi kukonzekera, chifukwa iyo ikubwera. Iye ndi Yehova-yire, Iye akhoza kupereka madzi kumeneko.”

56 Ndipo chinthu chokhacho chimene Iye anachita chinali kumulola munthu, wopusa, munthu wopusa, kuti azichita ndendende ndi sayansi yake, kuti akwaniritse zomwe Iye ankadziwa kuti zikanadzabwera. Mulungu sanawonongepo konse dziko; munthu amawononga dziko. Mulungu samawononga kalikonse, Mulungu amayetsa kusunga chirichonse. Munthu amadziwononga yekha ndi chidziwitso chake, monga iye anachitira m’munda wa Edeni pa mtengo, ndi zina zotero. Ndipo kotero wotentheka wina anagwira mphamvu ina ya atomiki, kwinakwake, yomwe iwo anali nayo.

57 Iwo—iwo ankakhoza kugwira nazo ntchito pa nthawiyo, chifukwa iwo ankakhoza kuchita zinthu pa nthawiyo ndi zimenezo zomwe ife sitinaziphunzirepo panobe. Ife sitinapite patsogolo kwambiri chotero. Mwinamwake zitenga zaka zitanu kapena foro apobe, kapena kupitirirapo, ife tisanachite izo, kuti tichite zomwe iwo anachita. Iwo anamanga mapiramidi ndi zosema ndi zina zotero. Ife sitingathe konse kuchita zimenezo. Ife sitingathe kuzibweretsanso izo, palibe njira yoti ife tingachitire zimenezo, pokhapokha titapeza mphamvu ya atomiki. Mphamvu ya petulo, mphamvu yamagetsi, sitikanakweza umodzi mwa miyala imeneyo, sitikanawusuntha iwo kuchoka pa nthakha. Ndipo zina za izo ndi zotalika ngati mdadada umodzi wa mu mzinda, mmwamba mu mlengalenga, ndipo zolemera matani biliyoni. Kodi iwo ankaikweza bwanji pamenepo? Mwaona, iwo ankadziwa.

58 Ndipo iwo amawusiya iwo, winawake amalola limodzi la mabomba a atomiki amenewo kuwulukira pa chotchinga cha ena, mmasiku am’mbuyo, chifukwa, “Monga momwe zinaliri m’masiku a Nowa,” monga zinaliri, mtundu umenewo wa chitukuko, mtundu umenewo wa anthu anzeru; “monga zinaliri m’masiku a Nowa, momwemonso zidzakhala, momwemonso zidzakhala mu kudza kwa Mwana wa munthu.” Kubwerezedwa kwa zomwe zinali! Mukuona?

59 Kuno osati kale kwambiri iwo anakumba chosungiramo madzi chamakono, chinali pansi—pansi kuno mu Mexico kusefukira koyamba kusanachitike. Inu munaziwona izo? Izo zinali mu pepala, kumene zosungiramo madzi zamakono monga ife tiri nazo tsopano, zomwe zinamira pansi pa nthaka; chinachake cha atomiki chinachiphimba icho. Iye anangophulika ndipo anapita monga choncho. Mukuona?

⁶⁰ Tsopano, “monga zinaliri m’masiku a Nowa,” amuna anzeru, amuna anzeru ndi mphamvu zawo za atomiki ndi chirichonse, amakhoza kumanga mapiramidi ndi zosema ndi zina zotero. “Monga zinaliri mu tsiku limenero, momwemonso zidzakhala.” Koma ntchitoyo ifupikitsidwa mu tsiku lino, chifukwa payenera kudzakhala anthu Okwatulidwa kutulutsidwa kunja. Monga Enoki, payenera kukhala anthu oti adzatengedwe. Ife tiri mu kalasi imeneyo mmawa uno, anthu amene atengedwera mmwamba monga Nowa anachitira kudzera mu chigumula.

⁶¹ Koma kumbukirani, zisanachitike...Musayiwale izi! Dontho limodzi la mvula lisanagwe, musanakhale chinthu chimodzi mu mlengalenga, Nowa asanakhale konse—asanamalize chombocho, Enoki anategedwera Kwawo. Enoki anakwatulidwa popanda imfa, anangoyamba kuyenda tsiku lina, ndipo—ndipo mphamvu yokokera pansu inasiya kumugwira iye. Ndipo iye anapeza phazi limodzi m’mwamba pang’ono, ndi linalo m’mwamba pang’ono, ndi phazi lina m’mwamba pang’ono, ndipo chinthu choyamba inu mukudziwa, iye anati, “Tsala bwino, dziko lapansi.” Anangoyenda kupita ku Ulemerero.

⁶² Ndipo pamene Nowa anayang’ana pozungulira ndipo sankakhoza kumupeza Enoki kulikonse, iye anayang’ana pozungulira ndipo sankadziwa kumene Enoki anapita, ndiye iye anati, “Yakwana nthawi yomanga chombo tsopano.” Mukuona? Ndipo iye anapita kukamanga chombo kuti chidzanyamule otsala.

⁶³ Ndi chinthu chomwecho chimene chikuchitika pomwe pano. Mpingo unategedwa kupita Kumwamba, ndipo Yohane tsopano akubweretsedwapo ndi Izo monga choyimira cha owukitsidwa, monga ife tinazitengera izo usiku watha. Ndipo tinapeza kuti Liwu lomwelo limene linamuyitana iye kuti ayang’ane mmbuyo pa dziko lapansi, linali Liwu lomwelo limene linamuyitana iye kuti akwere mmwamba.

⁶⁴ Oh, Mkhristu aliyense! Liwu lomwelo, Charlie, limene linakuyitana iwe tsiku lina kumusi uko mu Kentucky, kuti “Tembenuka,” ndi Liwu lomwelo limene lidzakuyitana iwe, “Kwera kuno!” Kodi sindinu wokondwa nazo izo, M’bale Evans? Liwu limene linati, “Tembenuka,” Liwu lomwelo linati, “Kwera kuno!” Oh, mai! Kumeneko, kuyitanidwa kotani! Zenizeni bwanji! Lomveka bwino, lomveka ngati lipenga, “Tembenuka, unditumikire Ine! Bwera kuno kumene Ine ndiri.”

⁶⁵ Pamenepo ife tinamuona iye akuyimira iwo amene anafa, Mose kuyimira oyerantima akufa; anauka. Eliya, ndi gulu lake pa tsiku lotsiriza, ndi gulu lake Lokwatulidwa litayima pamenepo. Onse pamaso pa Ambuye Yesu! Yohane anaziwulula izo... Yesu anawauza iwo kuti iye—iye sadzafa, ndipo zinali

chiyani kwa iwo ngati iye akanati akhale moyo mpaka iye atawona kudza Kwake. Ndipo ophunzira anatulutsa mawu.

⁶⁶ Oh, ine ndikanakonda ndikanapita kwenikweni, mwakuya kwenikweni pakali pano, kwa maminiti pang’ono, kwa mpingo. Aliyense amadziwa... Ndipo aliyense amakhala moyo wawamseri ndi Mulungu. Ndi chochitika cha pawekha, zinthu za Mzimu zomwe zimakutengera iwe ku malo amene iwe sungayerekeze nkomwe kuyankhula za iwo.

⁶⁷ Ine ndazindikira izi mu wanga womwe waung’ono, utumiki wodzichepetsa, kuti pali nthawi zambiri zimene ine ndimanena chinachake ndipo osadziwa chifukwa chomwe ndinanenera zimenezo, ndipo izo sizimawoneka zolondola (Komabe, winawake adzanena chinachake.), koma ine ndimayang’ana ndipo chinthu chimenecho chimadzabwera mwangwiro basi mozungulira kwa icho momwe chingakhoze kubwerera. Mulungu adzachipangitsa icho kuchitika! Ine ndikangofuna kunena chinachake, ine ndimati, “Chabwino, tsopano, dikirani miniti. *Munthu uyo, wakuti ndi wakuti, izi* kuti zichitike chakuno, tsopano izo—izo ziyenera kukhala mwanjira imeneyo basi.” Chabwino, kwenikweni, ine—ine sindimadziwa chifukwa chimene ine ndinanenera zimenezo. Ndipo chinthu choyamba inu mukudziwa, ziri mwanjira imeneyo basi. Mulungu amachita izo!

⁶⁸ Tsopano, pamene ophunzira awa anati, “Oh, Yesu anati ‘munthu uyu sangafe.’” Yesu sananene zimenezo.

Yesu anati, “Kodi inu mudzati chiyani ngati iye angadzakhale ndi moyo kufikira Ine nditabwera?”

⁶⁹ Koma kuwaona ophunzira akupanga maneno a izo, ndiye Yesu anatsika pansi ndipo anadzamutenga Yohane ndipo anadzamubweretsa iye ndipo anamulola iye kuti abwereze chinthu chonsecho, awone kubwereza kwa Kudza kwa Ambuye. Yohane anawuwona Mpingo, iye anawona mapeto a m’badwo wa Mpingowo, iye anawona mapeto a Ayuda, iye anawona Kudza Kwachiwiri, iye anawona dongosolo lonse.

⁷⁰ Ndipo taonani chimene Mulungu anayenera kuti achite; kumuwiritsa iye m’mafuta kwa pafupifupi maora twente foro kumusi uko, kuti aone kuti iye anali Waumulungu, kuti Mzimu Waumulungu unali utawadzoza cha—cha solo... (chakunja chija, chadothi, kapena chirichonse chimene inu mumachitcha icho, thupi la munthu), linali litakhathamira Mwaumulungu kwambiri mpaka mafuta oyaka otentha kwa maora twente foro sanamuwauale nkomwe iye. Kuyesera kuwiritsa Mzimu Woyera kuchoka mwa munthu; simungathe kuchita zimenezo. Ndiye anamuyika iye pa chisumbu cha Patmo, ndipo iye analemba Bukhu, ndipo anabwerera ndipo analalikira zaka zingapo. Hmm. Hmm.

⁷¹ Ndithudi, tsopano, iye amayenera kunyamula dzina loyipa, “Iye anali wam’bwebwe, iye anali mfiti.” Ndi angati akudziwa kuti Yohane ankatchedwa mfiti? Mwamtheradi! Yesu anatchedwanso choncho, nayenso. Mukuona? Mwaona, dziko silidziwa kanthu za zinthu izi. “Iye anali wowerenga maganizo.” Mukuona? Iwo ananena kuti “Iye anali mfiti kuti mpaka iye anawalodza mafuta aja, kuti mafutawo sakanatha kumuwothcha chifukwa iye anali atawalodza iwo,” chifukwa chakuti iye sanagwirizane ndi malingaliro awo Achikatolika. Ndizo zonse.

⁷² Iye anali wantchito wa Mulungu amene . . . wodzichepetsa, anali ndi ntchito yaying’ono kumeneko yomwe iye ankayisunga. Iye sakanalekerera ndi zinthu zakale zazikulu zimenezo, ndipo kotero Mulungu anangomusunga iye ndi kumusamalira iye. Momwemonso Iye anatero: Marteni Woyera ndi—ndi Ireniyasi, ndi onse kudutsa mu m’badwo.

⁷³ Ndipo Iye akuchita chinthu chomwecho lero, akubwera mpaka mmusi. Tsopano, musati muyiwale izi, kuti Mulungu analonjeza kugwedeza kwakukulu, ndi ntchito zazikulu, zamphamvu. Tsopano, lembani izi pa zolembe zanu zomwe mukulemba (Mukuona. Mukuona?), chimene munthu amachitcha “champhamvu ndi chachikulu,” Mulungu amachitcha “Chopusa!” Ndipo chimene munthu amachitcha “chopusa,” Mulungu amachitcha “Chachikulu!” Musayiwale zimenezo, mwaona, musayiwale zimenezo. Izo zikuthandizani mu zaka zikubwerazi, chifukwa ife tikufunafuna chinachake chachikulu nthawi zonse. Ndipo ife tikulandira zokulirapo nthawi zonse, koma anthu a mdziko sakudziwa izo. Ngakhalenso iwo sankadziwa zimenezo m’masiku a Nowa, ngakhalenso iwo sankadziwa zimenezo m’masiku a Yohane, m’masiku a Yesu, m’masiku a atumwi, m’masiku a Ireniyasi, lililonse la masiku amenewo, iwo sankadziwa konse zimenezo.

⁷⁴ Ngakhale Joan waku Arc, iye anali woyera, mkazi wamng’ono. Pamene iye sanali kanthu koma msungwana, Mulungu anayankhula kwa iye m’masomphenya, ndipo Mngelo anayankhula kwa iye. Inu mukudziwa zomwe mpingo wa Katolika unanena? “Iye ndi mfiti.” Ndipo iwo anamuyika iye pa nkhu ni ndi kumuwothcha iye mpaka kufa, ansembe Achikatolika anatero; anamupha iye, anagamula imfa yake monga “mfiti,” ndipo Joan waku Arc anafa monga mfiti. Pafupifupi zaka thuu handiredi pambuyo pake, iwo anadzapeza kuti iye sanali mfiti, iye anali wo—wophunzira wa Khristu.

⁷⁵ Iwo anachita chinthu chomwecho kwa oyeramtima onse. Yesu anati, “Ndi ndani wa inu amene makolo anu sanamuzunze? Ndi ndani wa aneneri amene anabwerapo amene iwo sanamukane?” Anati, “Inu makoma oyeretsedwa.” Anati, “Inu—inu mumapite pansu ndi—ndi kukayika zokongoletsa pamwamba pa manda a aneneri, ndipo ndinu nomwe amene munawayika iwo mmenemo.” Hmm! Mai! Mai! Mukuona? Iye

sanabweze nkhonya zirizonse pa iwo. Hmm! Iye anangowauza iwo.

⁷⁶ “M’badwo uwu wa njoka,” Yohane anati, “ndani wakuchenjezani inu kuthawa mkwiyo womwe ulinkudza? Musayambe kunena kuti muli ndi Abrahamu kwa atate wanu.” “Ndife a mabungwe enaake, aakulu.”

“Kodi ndinu Mkhristu?”

⁷⁷ “Oh, ndine wa Methodist. Ndine wa Presbateria. Ndine wa Chipentekoste.” Izo siziri mmenemo nkomwe. Izo ziribe chirichonse chochita kuposa—kuposa—kuposa—kuposa—kuposa momwe chipale chimachitira ndi kuwala kwa dzuwa. Mukuona? Izo ziribe kanthu kochita ndi izo. Ngati ndinu Mkhristu, ndinu wantchito wa Mulungu wobadwa kachiwiri.

⁷⁸ Tsopano, tsopano, pamene Yohane anabwera, ife tinali ndi zimenezo usiku wathawu. Tsopano, kumbukirani, pamene inu mufika ku izi... Pa nkhani ya chinthucho, ine—ine ndinakuuzani inu pamenepo. Kumbukirani, dziko likukhala ndi kugwezezeka kolimba kwambiri komwe linayamba lakhalapo nako, pakali pano, dziko la mpingo.

⁷⁹ Tsopano, kumbukirani, mosakayikira, m’masiku a—a Yohane, masiku a Yesu, kunali zikondwerero zopambana ndi oyankhula opambana m’masiku awo, amuna aluntha opambana, ndipo iwo anakoka mateni a zikwi kuchulukitsa zikwi za anthu. Kodi Kayafa akanachita chiyani ngati iye akanayitanitsa m—msonkhano pamodzi? Akanabweretsa Yerusalemu yense, akanabweretsa Israeli yense pamodzi, kuchokera msanamira mpaka ku mzati. Ndipo onse a iwo amati, “Oh,”

“Tsopano, ngati Kayafa anganene zinthu *zakuti-zakuti*, izo zikhala zopambana.”

“Oh, kodi inu mumawakhulupirira Malemba, Rabbi, M’busa, Dokotala, Bishopu? Kodi inu mumawakhulupirira Malemba?”

“Ndithudi, ine ndimawakhulupirira Malemba, ndine sikolala wodziwika!”

⁸⁰ “Chabwino. Tsopano, Baibulo linanena apa kuti idzafika nthawi yomwe padzakhale, ‘Mapiri onse adzadzumpha ngati tiana tankhosa, masamba onse adzawomba m’manja, ndipo malo onse okwera adzatsitsidwa pansu ndi kusalazidwa, malo onse otsika adzakwezedwa mmwamba ndi kukhala okwera. Ndipo izo zidzachitidwa ndi liwu la iye wofuula m’chipululu.’ Kodi inu mukukhulupirira zimenezo, Rabi, M’busa, Dokotala, M’busa?”

“Ndithudi, ine ndikukhulupirira zimenezo!”

“Kodi izo zidzachitika bwanji?”

⁸¹ “Oh, Mulungu adzatumiza munthu wamphamvu pa dziko lapansi tsiku lina. Oh, iye adzakhala wamkulu. Iye adzakhala liwu la iye wofuula mu chipululu, kapena iye adzatsogolera

Mesiya wakudzayo. Ndipo pamene iye adzabwera, mulibe kukaikira m'malingaliro anga koma chimene adzatsike kuchokera Kumwamba ndi kubwera pansu ku kachisi. Iye adzabwera kumusi konkuno ku kachisi, ndi kunena, 'Tsopano, ife titenga Aroma onse ndi kuwamenya iwo mpaka kufa. Ndizo zonse. Ife tidzagonjetsa Aroma onse.' Ndipo—ndipo kenako iye adzanena, "Tsikani pansu pano, Mesiya!" Ndipo Mesiya adzatsika pansu, ndipo ife tiwumbamo zikwakwa zathu zonse kukhala. . . kapena malupanga athu akhale zolimira ndi zikwakwa, ndipo sipadzakhalanso nkondo." Ndipo, uh-huh, ndiko kutanthauzira kwawo.

⁸² Koma chinachitika ndi chiyani pamene izo zinabwera? Kodi chinachitika ndi chiyani? Kunalibe chiwonetsero cha Kumwamba, chimene iwo anayamba achiwonapo; chinalipo chimodzi, koma iwo sanachione icho. Iwo sanachione icho. Mwaona. Ndi liti pamene mapiri onse analumpha ngati tiana tankhosa? Kodi ndi liti pamene malo okwera onse anakhala otsika ndi malo otsika kukwera? Mlaliki wa nkhope yachikale anabwera akuyenda kuchokera ku chipululu ndipo sankadziwa nkomwe ma ABC ake. Malingana ndi mbiri yakale, iye anapita kuchipululu ali ndi zaka naini ndipo sanawonekerenso mpaka iye anali sarte. Iye anakhala moyo kuchokera mu dzombe ndi uchi wa mtchire. Dzombe ndi ziwala, ziwala zazitali zija.

⁸³ Iwo amazidya izo nthawi zonse. Chabwino, inu mukhoza kugula izo konkuno mu. . . Musaganize kuti ndizoyipa, chifukwa inu mukhoza kuzigula izo kuno mu sitolo yayikulu ngati inu mukuzifuna, njuchi za m'maluwa, njuchi za uchi, dzombe, njoka, chirichonse chimene inu mukufuna.

⁸⁴ Koteru anakhalira moyo pa dzombe ndi uchi wa mtchire. Ndi chakudya chotani! Koma iye ankasungidwa ndi mphamvu ya Mulungu. Iye sankavala ndi kolala yake yotembenezidwa; monga winawake ananena usiku wathawu, M'bale Parnell kapena ena a iwo. Iye sankavala chikhotho cha chipsyepsye, ndi zonse zokhudza izo. Anatuluka mu chipululu ndi chidutswa chachikulu, chachikale cha chikopa cha nkhoza chitakulungidwa momuzungulira iye. Monga ine ndanena, mwinamwake. . . Ife timayenera kusamba tsiku lililonse, ndipo mwinamwake iye sanasambe kamodzi pa miyezi itatu kapena foro iliyonse, kunja uko mu chipululu. Ine sindikudziwa. Iye sanali mochuluka kwambiri woti nkuyang'anapo. Iye analibe guwa. Iye sanapite m'mizinda ikuluikulu iliyonse ndi kukakhala ndi misonkhano yokopa anthu yayikulu. Iye anayima kunja uko pa magombe a Yordani, matope mpaka m'mawondo ake, ndipo anati, "Inu m'badwo wa njoka, wakuchenjezani inu ndani kuti muthawe mkwiyo womwe ulimkudza?" Hmm. Ndi pamene malo okwera anatsitsidwa, mwaona, ndipo malo otsika anapangidwa kukhala okwera. Uh-huh. Inde, bwana.

⁸⁵ Ndiye, chinthu choyamba inu mukudziwa, iwo anali

kuyembekezera Mesiya kuti adzabwere pansi ndi Angelo ndi zinthu, ndi kudzakhazikika mu mlengalenga kunja uko ndi kachisi kumene iwo anamumanga kuti Iye adzabwereko (monga ife tikumangira malo aakulu kwambiri lero kudutsa mafuko ndi zina zotero). Mukuona? Ndipo Iye anabwera liti? Iye analambalala alionse a ma sunagoge awo, lirilonse la mabungwe amenewo, ndi kubwera mpaka ku khola. Iwo anamukakamiza Iye kulowamo.

⁸⁶ Ndi zomwe ziri lero. Iye amakakamizika kulowa mu zinthu, kukakamizidwa kuti achite izo, kukakamizidwa kuti akhale pakati pa zipembedzo, chifukwa Uthenga Wake sumagwirizana ndi chipembedzo. Uthenga Wake lero, wolalikidwa ndi atumiki Ake, ndi wa zipembedzo zosiyanasiyana chifukwa zipembedzo zinamuthamangitsira Iye kunja. Baibulo linanena chomwecho. Iye anali kunja, akugogoda, akuyesera kuti alowe mkati, (Mukuona?), mu mpingo Wake Womwe. Ndipo pamene izo ziri. Mwaona, ziri chimodzimidzi basi lero.

⁸⁷ Kotero, kumbukirani, chimene chimawoneka chachikulu kwa munthu, ndi chaching'ono pamaso pa Mulungu. Tsopano, ndicho chifukwa chake simusowa kuti mukhale ndi maluwa ochuluka. Ndipo pamene Mulungu abwera kachiwiri, pamene Yesu adzabweranso, inu mudzadabwa, mkazi wamng'ono wotsukambale uja kumbuyo mu khwalala. Uh-hum. Inu mudzadabwa, munthu ameneyo amene samanena kalikonse, akusunga zinsinsi zake kwa iyemwini ndi kuyenda mozungulira pamaso pa Mulungu, wodzichepetsa. Inu mudzadabwa. Izi zidza- . . .

⁸⁸ Ine ndinalalikira osati kale kwambiri, pa chiweruzo. . . *Zodabwitsa pa Chiweruzo*. Sizidzakhala zodabwitsa kumuwona wogulitsa mowa kumeneko, iye akudziwa kuti akupita. Ndithudi. Sizidzakhala zodabwitsa kumuwona wabodza, wachigololo, chirichonse pamenepo, chimene panalibe. Koma chodabwitsa chidzakhala, ndipo chokhumudwitsa chidzakhala, amene akuganiza kuti akupita; uh-huh, eya, ndiyeno nkudzakanidwa. Iwo amene anati, “Chabwino, dikirani miniti, amayi anga anali a mpingo uno, bambo anga anali a mpingo uno, agogo anga aamuna ndi agogo aakazi. Ndakhala membala kumeneko moyo wanga wonse.”

⁸⁹ “Chokani kwa Ine, inu ochita kusaeruzika, Ine sindinakudziweni nkomwe inu.”

⁹⁰ Tayang'anani m'masiku pamene Simeoni wamng'ono, wokalamba, munthu wosadziwika, wopanda mbiri, ife sitimadziwa kalikonse za iye mu Baibulo. Koma Baibulo linati, “Izo zinawululidwa kwa iye ndi Mzimu Woyera,” (Ndi uyo apo; ndi inu apo.) “kuti iye sadzafa mpaka atamuwona a—Khristu wa Ambuye.”

⁹¹ Ndiye yang'anani pa yemwe Yohane Mbatizi anali, mtundu wina wa munthu wosamvetsetseka, munthu wakuthengo uko mu nkhalango. Izo zinawululidwa kwa iye. Iye anabwera akulalikira Uthenga. Tayang'anani pa zimenezo!

Kodi Anna wamng'ono anali ndani?

⁹² Namwali wamng'ono, Maria, kumusi uko mzi—mzinda wa Nazareti (wankhanza monga Jeffersonville) ndipo kumene uchimo ndi zonse zinachuluka, koma iye anali atadzisunga yekha wangwiro chifukwa iye ankadziwa kuti tsiku lina kunali Mesiya wakudza. Mukuona?

⁹³ Yosefe, mpalamatabwa, anali atataya mkazi wake ndipo—ndipo anali paubwenzi ndi msungwana wamng'ono uyu. Ndipo izo zinali kudzera pamenepo Mzimu Woyera unadza kwa ameneyo. Ndiyeno dziko likubwera mozungulira ndi kudzazitcha izo dzina lakuda, monga “woyera wodzigudubuza, wachipentekoste.” Mwaona, kuzitcha izo dzina lakuda. “Bwanji, izo, iye...mwana ameneyo anabadwira kunja kwa chikwati choyera.” Mwaona, iwo ankakhulupirira zimenezo, ndipo izo zinkawoneka ngati zinali choncho. Koma Mulungu amachita zimenezo kuti achititse khungu maso a anzeru ndi aluntha, ndi kuziwulula Izo kwa makanda omwe ati adzaphunzire.

⁹⁴ Ine ndikukhulupirira kuti pali maziko okwanira pamene ine ndigunda chinachake pakapita kanthawi. Ine ndikuwonetsani inu. Inu mukuona mafuta awa? Tsopano, zimene ndakuwuzani, maziko, kuti muone kuti si munthu, ndi Mulungu, ine ndiloza kwa *izi*. Chabwino.

⁹⁵ Tsopano, “Kwera kuno,” linali Liwulo. Ndipo pamene iye anatsegula iye anamva kulira kwa lipenga, ndipo pomwepo Yohane anali mu Mzimu—anali mu Mzimu, ndipo mwamsanga pamene iye analowa mu Mzimu iye anayamba kuona zinthu. Inu mumayamba kuwona zinthu pamene inu mulowa mu Mzimu. Choyamba inu mumayenera kuti mulowe mu Mzimu. Ndi kulondola uko?

⁹⁶ Tsopano, bwanji ngati inu mutapita ku masewera a mpira, ndipo inu nkumati, “Ine ndithudi ndimakonda baseball.” Umhum. Ndipo inu mumadzipezera mpando wakutsogolo, pansu pomwe mu mpando wa bokosi ndipo mukuwonerwa ma Yankees kapena Bulldogs, alionse amene iwo ali, akusewera. Ndipo onse ali ndi masewera aakulu kunja uko.

⁹⁷ Ndipo mbali yanu yangotsala pang'ono kuti igonje, ndipo zonse mwakamodzi Babe Ruth wamakono nkudzapukusa ndodo yake monga *chonchi* ndi kunena, “Mwakuona kutali uko?” Ndiri ndi amuna atatu pansu. “Whammy!” Ndipo nkumumenyera iye kutali kosawoneka; navula chipewa chake ndi kuzikupiza yekha; nayenda pansu pa bwalo loyamba ndi kuyang'ana pozungulira, anyamata onse awo; napita ku bwalo lachiwiri, kukagwirana chanza ndi munthu wa pabwalo lachiwiri;

kuyenda, kuyenda mwakachetechete kubwerera kunyumba komwe, kuweramitsa wake...Bwanji, mai! Mai! Kukuwa, kulumpha, kukuwa, kufuula kwa, “Chikondwerero!” Bwanji, iwo akanati... .

⁹⁸ Ine kwenikweni ndawawonapo iwo akutenga izi...Inu mukukumbukira chipewa chakale cha udzu choluka? Ine ndinapita ku masewera a baseball tsiku lina ndipo ndinawona munthu atagoletsa. Ndipo munthu ameneyu atakhala patsogolo panga ali ndi chipewa cha udzu, iye anali wosangalala; anatenga chipewa chake ndipo anangochikokera icho pansi pomwe, anangomuyika iye kolala mozungulira monga *chonchi* pamene pamwamba pake panatuluka kunja. Bwanji, iye ankakhala nayo nthawi yopambana! Iye—iye anali atasokonezeka kwambiri iye samadziwa zomwe anali kuchita. Kumangokankha ndi kukuwa ndi kufuula ndi kudumpha. Chabwino, tsopano, inu mukudziwa zomwe ine ndikuganiza, iye ndithudi anali...iye anali wa ba-...iye anali a...iye anakonda baseball. Iye anali wokonda baseball, monga ngati wokonda ndudu kapena wokonda kachasu.

⁹⁹ Ndine wokonda Yesu. Eya. Ine ndimangozikonda zimenezo. Ine...Ngati inu mufika pokhala wokonda Yesu, inu mukuona, wokonda chinachake.

¹⁰⁰ Ndiye inu mukhoza kulingalira munthu ameneyo anati, “Oh, ndithudi, ndine wokonda baseball.” Ndipo mbali yake yatsala pang’ono kuti igonje, ndipo iwo anamuwona iye akubwerapo ndi kupambana masewerawo monga choncho, iye anayang’ana pozungulira ndipo, “Eya, mwina izo zinali zabwino.” Uh-huh. Kunena, iye “amakonda baseball.”

“Oh, iye ndi chinachake!”

¹⁰¹ Inu mungati, “Bwanji, inu simumayikonda, inu mumatero? Pali chinachake cholakwika ndi inu!” Wokonda baseball wabwino aliyense anganene kuti, “Chalakhwika ndi chiyani ndi munthu ameneyo? Chinachake chalakhwika ndi iye. Tamuonani iye wakhala pamenepo.” Huh! Ndizo basi zotero... .

¹⁰² Ikani awiri kwa awiri palimodzi tsopano, mwaona. Oh, iwe ukakhala wokonda Yesu, ndipo iwe umamverera Mzimu Woyera ukuwamiza Mawu amenewo, ndiye chinachake chimafuula! Oh, inu mumapita kutali ndi inueni!

¹⁰³ Ine ndikukhulupirira kuti bambo uyu andikhulukukira ine, iye wakhala pafupi apa. Munthu wamkulu, wamtali wamutu wakuda wakhala apa, yemwe anayima kunja uko usiku wina mu holo, ndipo winawake ananena chinachake chonga... thandizo, inu mukudziwa, kukhala ngati zinamudalitsa iye monga choncho. Ndipo mnyamata wosaukayo wakhala nayo nthawi yoyipa, ine ndikudziwa wake—mkazi wake anamusiya iye ndipo anamusumila iye kwa chilekano chifukwa iye ankawakonda Ambuye Yesu. Uko nkulondola. Ndipo winawake

ananena chinachake chokhudza Yesu, inu mukudziwa, iye anali ngati mmodzi wa otengeka amenewo. Ndipo iye anali atakhala mu nkondo ndipo anali wowomberedwa paliponse, ndi chirichonse, mnyamatayo anali; anamumvera iye chisoni. Anabwera kunyumba ndi a...ana ake ndi mkazi wake. Ndiye iye—iye anamulonjeza Ambuye kuti adzamutumikira Iye, ndipo mwamsanga pamene Ambuye anayamba kumudalitsa iye ndipo anali molondola ndi Mulungu, mkazi wake anangotembenuka, kumusumira iye chilekano ndipo anamusiya iye. Anamusiya iye atakhala kunja kozizira. Koma iye anali wotengekabe.

¹⁰⁴ Ndipo pamene iye anayima pamenepo usiku wina ndipo wina ananena chinachake zokhudza Yesu, chinachake, momwe Iye analiri wamkulu, monga choncho, iye anati, “Oh, Ulemerero!” Anaponyera mikono yake kunja ndipo apa chibakera chake chinali chitakakamila mu khoma monga chonchi. Iye sankadziwa kuti anachita zimenezo. Chibakera chake chinakakamira pakhoma. Anati, “M’bale Bill, ine ndidzalipira pa zimenezo.” Ine ndikuganiza M’bale Wood anabwera ndi kudzayika chidutswacho, kudzayika chidutswa china. Ife sitinasamale zimenezo, M’bale Ben, ife basi—ife tinangokondwa kuti inu munali wotengeka. Mwaona?

¹⁰⁵ Pamene Mzimu Woyera uchita chinachake kwa iwe, sungakhoze basi kukhala chete, pali chinachake chimatumphukira kunja. Ameni. Fyuu! Eya, chinachake chimagwira, wotengeka wa Khristu. Pamene iwe umukonda Ambuye, chinachake mwa iwe chikufikira, chikugwira, chikuchitira njala ndi kuchitira ludzu, Yesu anati, “Odala ali iwo, chifukwa iwo adzadzazidwa. Odala ali iwo amene ngakhale amachitira ludzu, kaya inu muli nawo Iwo kapena ayi.” Ndi ngati akufuna zochuluka za Mulungu? Chabwino. Chabwino, chifukwa chimene inu mukufunira zochuluka za Mulungu, ndinu odala kungokhala chimenecho. Ngati inu mulibe Iwo, inu mukadali odala. “Ndipo odala ali iwo akumva njala ndi ludzu.” Ndinu odalitsidwa chifukwa chongokhala ndi njala ndi ludzu. Chifukwa inu mukuwufuna Iwo, ndinu odala. Chifukwa pali anthu ambiri omwe sakuwufuna Iwo.

¹⁰⁶ Mukukumbukira ulaliki wanga usiku wina? Mwaona, monga wopusa, iye anasunga bokosilo ndi kutayira mphatsoyo kutali. Mukuona? Musatenge bokosi, mutenge Mphatsoyo. Chabwino.

Tsopano, nthawi yomweyo...mu mzimu: ndipo, taonani, mpandowachifumu...unakhazikitsidwa kumwamba, ndipo mmodzi anakhala pa mpandowachifumuwo.

¹⁰⁷ Tsopano, zindikirani, kanthawi kena pang’ono, kapena, ife tinazipeza izo usiku wathawu, ine ndikukhulupirira, kuti pa Mpandowachifumu uwu...Ife tikupeza kuti poyamba panalibe kanthu pa Mpandowachifumu, ndipo tsopano pali

Winawake pa Mpandowachifumu kotero izo zinasonyeza kuti Yesu anabwera ndi Mpingo Wake mpaka mu Ulemerero ndipo anadzakhala pa Mpandowachifumu Wake Womwe. “Atakhala pa Mpandowachifumu,” zimenezo ndi utatha m’badwo wa Mpingo. Tsopano, tsopano, ife tikufuna kuti tifike ku zimenezo pakapita kanthawi.

108 Tsopano, inu mukuti, “Chabwino, mpandowachifumu Wake uli kuti lero?” Tsopano, M’bale Neville, ngati ine ndingadutse pa zimenezo, inu mundifunse ine pakapita kanthawi, “Uli kuti mpandowachifumu Wake lero.” Ine ndikuganiza kuti ndifika ku zimenezo mpaka kumeneko. “Mpandowachifumu Wake uli kuti tsopano ngati Iye siali pa Mpandowachifumu Wake tsopano?”

Iye siali pa Mpandowachifumu Wake tsopano. Ayi, bwana.

109 Chabwino, tsopano:

*Ndipo iye wokhalapo anali wowoneka monga...
yaspi ndi...mwala wa sardiyo: ndipo panali utawaleza
wozinga mpando wachifumuwo, wofanana...m’maso
mwake ngati mwala wa emarodi.*

110 Tsopano, tiyeni titenge tsopano ndime ya 3, kuti tiyambe. Ndipo kotero “yaspi,” Mmodzi uyu amene anakhala pa Mpandowachifumu anali wowoneka...Mwa kuyankhula kwina, pamene inu muyang’ana pa Iye, Iye anali mbambande, kukongola kotero! Oh, ine ndikufuna kuti ndimuwone Iye. Sichoncho inu?

111 Tsiku lina...Ine ndikukumbukira Mlango Cadle, Mlango Howard Cadle, ine ndikuganiza ambiri a inu mukumukumbukira iye. Ine ndinali kutsidya kwa msewu kumeneko, ndipo mkazi wanga atakhala pamenepo tsopano akukumbukira kuti iye anali wozizidwa, mu chipinda. Ndipo ine ndinali nditadzuka, ndipo ndinali ndi yaying’ono, yakale... inali mbaula ya utsi kunja uko ndi...ife tinaphika mkate wathu mu uvuni, mu paipi. Ndipo ine...kunkazizira kwenikweni ndipo mphepo inali ikuwomba, nthawi yachisanu, chipale chili pansu, ndipo mphepo pansu potulukira utsi, ndipo ine sindinathe kuchiwotha chinthu chimenecho, kuti ndipulumutse moyo wanga. Ndipo ine ndinangokhala wotopa kwambiri ndi zimenezo. Ndipo ine ndinayikamo ina, imaphulitsa iyo kachiwiri. Billy anazizidwa ndipo mkazanga anazizidwa, ine ndinkayesera kuti ndiyatse moto. Ndiyeno ine ndinapezeka kuti ndinatsegula wailesi ndipo (mphindi zochepa zisanachitike, ndipo nditangotenthedwa, ndinabwera), ndipo Mlango Cadle anali kuyimba, “Pamene ine ndidzafika ku Dziko limenero, pa njira yakutaliyo, ine ndikufuna kuti ndidzamuwone Yesu. Sichoncho inu?” Oh, mai!

112 Ine ndinangokhala pansu pompo pakati ndipo ndinangokhala pamenepo ndi kuyamba kulira. Inu mukudziwa momwe iye ankayimbira, pansu, kuchokera mu liwu lake lokoma

kwenikweni la mbalame. Ine ndikufuna kuti ndidzamumve iye pamene ine ndidzawolokera kutsidya linalo; anati, “Ine ndikufuna kumuwona Yesu. Sichoncho inu?”

¹¹³ Ine ndinaganiza, “O Mulungu, inde, ine ndikufuna kudzamuwona Iye tsiku lina. Pamene maluwa onse ayandama, ine ndikufuna kudzamuwona Yesu.” Bwanji... Kudzamuwona Iye pa Mpandowachifumu Wake, kukongola Kwake, kunyezimira Kwake! Ndipo ngati ine... Oh, ine ndikufuna kudzayima pamene Yohane anayima, kotero ine ndikhoza kudzangoyima ndi kumayang’ana pa Iye.

¹¹⁴ Kuno nthawi ina kalelo, kumusi... nthawi ya ukapolo. Ine ndikunena izi mmalo mwa abwenzi anga achikuda omwe ali pano mmawa uno. Uko kunali munthu wachikulire, wachikuda ndipo iye anali... kupita ku malo aang’ono, iwo ankakonda kutero.

¹¹⁵ Ndipo ndinkakonda kuchita izi uko mu Kentucky, kukakhala ndi kuyimba. Mwinamwake Amayi Cox ndi iwo akhoza kukumbukira pamene tinkapita ndi kukakhala ndi zoyimba, inu mukudziwa, kupita ku nyumba ndipo iwo ankayimba limba, ana aang’ono ndi onse nkumayimba. Ankachitira izo kuno ku Utica, ndi kozungulira kumadera akumidzi. Tsopano iwo ali ndi nkunda umodzi wa kachasu, kunja kwinakwake ku phwando la gwedemula.

¹¹⁶ Koma, nthawi imeneyo, iwo ankayimba nyimbo. Amodzi mwa mayimbidwe a nyimbo zachikale izi, panali m’bale wachikulire, wachikuda yemwe anapulumutsidwa. Ndipo Ambuye anamuyitana iye kuti akalalikire, ndipo tsiku lotsatira iye anapita mozungulira akuwauza akapolo pa munda. Iye anati, “Ambuye wandipulumutsa ine usiku wathawu ndipo wandiyitana ine kuti ndilalikire kwa abale anga.”

¹¹⁷ Ndipo potsirizira pake izo zinakafika kwa mwini malo odyetserawo kapena mwini mundayo. Anamuyitanira iye mkati, anati, “Sambo, ine ndikukufuna iwe, bwera mkati muno.” Anati, “Bwera mu ofesi yanga.”

Iye anati, “Inde, bwana,” anapita ku ofesiko.

¹¹⁸ Iye anati, “Ndi chiyani chomwe ine ndikumva kuti iwe ukufalitsa pakati pa akapolo, pakati pa anthu amenewo kunja uko, manja anga, akapolo anga, kuti Ambuye anakumasula iwe?”

¹¹⁹ Anati, “Inde, bwana.” Iye anati, “Bwana, ndine kapolo wanu.” Iye anati, “Ine ndinagulidwa ndi ndalama zanu, koma...” Iye anati, “Koma momwe Mulungu ameneyo anandimasulira ine usiku wathawu, Yesu anandimasula kuchoka ku moyo wauchimo ndi manyazi, ndi moyo wa imfa. Iye anandipanga ine womasuka.”

Iye anati, “Sambo, kodi iwe ukutanthauzadi zimenezo?”

Iye anati, “Ine ndikutanthauza izo.”

¹²⁰ Iye anati, “Ndinawamva iwo akunena kuti iwe uyamba kulalikira kuno kwa ako—anthu ako pa minda ndi zinthu.”

¹²¹ Anati, “Eya, bwana!” Anati, “Ndicho chimene ine ndikulinga kuti ndichite, ndi kulalikira Uthenga uwu kwa anthu anga.”

Anati, “Iwe ukutanthauzadi zimenezo, Sambo?”

Iye anati, “Ine ndithudi ndikutanthauza izo.”

¹²² Anati, “Bwera, upite nane ku—ku bwalo lamilandu, ine ndikupatsanso ufulu wako. Ndiwe mfulu kwa ine, ndipo ndiwe womasuka ku ukapolo uliwonse. Ine ndinakugula iwe, ndiwe wanga, ndipo ine ndikukumasula iwe kuti ukakhoze kulalikira Uthenga kwa anthu ako.” Iye anapita uko ndipo anakasaina chimasulo, kapena kulengeza, ndipo iye anamasulidwa. Iye sakanagulitsidwanso ngati kapolo. Iye anali munthu womasulidwa kuti alalikire Uthenga.

¹²³ Iye analalikira pakati pa abale ake kwa zaka zambiri. Azungu ambiri anatembenezidwa pansu pa utumiki wake. Tsiku lina munthu wachikulireyo anabwera pansu kuti afe. Iye anali atalalikira kwa zaka sarte kapena forte, kapena kupitirira. Ndipo pamene iye anabwera kuti adzafe, iye anali atagona mu chipinda, ndipo ambiri a abale ake achizungu anali atasonkhana mozungulira mchipindacho ndipo iwo ankaganiza kuti iye anali atapita kwa pafupifupi maora awiri kapena atatu. Ndiye pamene iye potsiriza anadzuka nayang’ana mozungulira mchipindamo, iye anati . . .

“Iwe unali kuti, Sambo?”

Iye anati, “Oh, kodi ndabwereranso kuno kachiwiri? Kodi ine ndabwereranso kachiwiri?”

Iwo anati, “Chavuta ndi chiyani, Sambo?”

Anati, “Oh, ine ndinawolokera ku Dziko linalo.”

Iwo anati, “Tiuzeni ife za zimenezo.”

¹²⁴ Iye anati, “Chabwino, ine ndinangolowa mkati, mu Kukhalapo Kwake.” Ndipo anati, “Pamene ine nditayima pamene,” iye anati, “panali Mngelo anayenda apo, anati, ‘Kodi dzina lako ndi, Sambo *Wakuti ndi wakuti?*’”

Iye anati, “Eya, bwana, ndi choncho.”

Iye anati, “Lowa mkati.”

“Ndinalowa mkati, ndipo ine ndinayang’ana pa Iye atakhala pamene.”

¹²⁵ Iye anati, “Sambo, bwera kuno tsopano, utatha kumuwona Iye ndikufuna iwe, ubwere kuno, ife tikufuna kuti tikupatswe iwe mwinjiro wako, ife tikufuna kuti tikupatswe iwe zeze wako, tikufuna kuti tikupatswe iwe korona wako.”

Sambo anati, “Musandiyankhule ine za azeze, akorona, ndi miinjiro.”

Anati, “Koma iwe walandira mphotho, ife tikufuna kuti tikupatse iwe mphotho yako.”

¹²⁶ Anati, “Musandiyankhule kwa . . . za ine . . . za mphotho.” Anati, “Ingondilolani ine ndiyime ndi kumayang’ana pa Iye kwa zaka chikwi. Imeneyo ikhala mphotho yanga.”

¹²⁷ Ine ndikuganiza umo ndi momwe ife tonse tikanamverera, “Ingondilolani ine ndiyime ndi kumayang’ana pa Iye.” Oh, ine ndiyenera kuti ndikhale ndi thupi losiyana ndi lomwe ine ndiri nalo tsopano, mnyewa uliwonse wa umunthu wanu kuti muzingoyang’ana pa Iye.

¹²⁸ Pamenepo Yohane anayima ndipo anamuwona Iye atakhala pa Mpandowachifumu, ndipo Iye “anali kuoneka ngati mwala wa yaspi ndi sardiyo.” Tsopano, zinthu zonse ndi mawu aliwonse ali ndi tanthauzo mu Baibulo. Tsopano, “mwala wa yaspi ndi sardiyo.”

¹²⁹ Tsopano, ngati inu mungazindikire, izo zikufanana ndi Lemba lonselo. Kumbuyo kwa Lemba, Iye anali Alefa, Omega, Iye anali Woyamba ndi Wotsiriza, Iye anali Woyamba ndi Wotsiriza, Iye anali Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera. Iye anali “zonse mu zonse” anawunjikidwa mwa Iye. Mateyu 17 akusonyeza kuti Iye . . . pamwamba pa Phiri la Chiwalitsiro, izo zonse zinasonkhanitsidwa mwa Iye.

¹³⁰ Tsopano, “yaspi” unali—unali mwala, ndipo “sardiyo” unali mwala. (Tsopano, ife tifika ku mitundu yawo pakapita kanthawi.) Tsopano, ine ndikufuna inu muzindikire kuti aliyense wa mbadwazo pamene izo zinkabadwa, eya, munthu aliyense, ali ndi mwala wakubadwa. Ine, ine ndinabadwa mu Epulo, diamondi. Ndipo miyezi yosiyana imayimira miyala yosiyana. Chabwino, mbadwazo zinali chimodzimidzi. Nthawi iliyonse imene mbadwa, pamene iye ankabadwa, iye ana- . . . anali ndi mwala wakubadwa.

¹³¹ Ndipo kungoyima pomwe pano mphindi yokha. Pamene amayi Achihebri amenewo . . . Ndilole ine ndikusonyeze iwe Mawu Auzimu, mzanga, kuti chikhulupiriro chako chimangidwe motsimikizika mu Mawu a Mulungu. Nthawi iliyonse, amayi Achihebri amenewo, pamene iwo anali mu zowawa, akupereka ululu wa kubala, kuti abadwe . . . kubala ana awa, mawu omwewo amene iye ankayankhula mu kubala kwake ankamupatsa mwamunayo (mwana wobadwa mwa iye) dzina lake, ndipo mwapamalo ake ankamuyika iye mu Palestina kumene iye ati adzakhale pa kudza kwa Ambuye. Ululu wakubala mwa mayi yuu! Monga, *Efremu* amatanthauza “pafupi ndi nyanja.” Mukuona? Ndipo *Efremu* anapatsidwa gawo lake mphepete mwa nyanja. Ndipo, kunena, *Yuda* ankatanthauza . . . Ine sindikudziwa chimene mawuwo amatanthauza, koma ine

ndikhoza kuwapeza iwo. Tsopano, taonani, ndi pamene ine ndiribe nthawi, zinthu zazifupi izi, kuti ndizitolere zinthu zimenezo. Koma ndiye bwererani m'mbuyo, ndipo Yuda, kulikonse kumene Yuda amathanthauza, amathanthauza malo ake ayikidwa pakati pa ana a Israyeli.

¹³² Ndipo tengani pa Genesis 48 ndi 49, inu mudzapeza pamene po kuti Yakobo, pamene iye ankafa, atatsamira pa ndodo yake, atachititsidwa khungu, iye mwapamalo anawauza ana amenewo kumene iwo akanati adzakhale pa mapeto a dziko. Ndipo mwapamalo akhazikitsidwa pomwe apo tsopano chibwererani ku dziko lakwawo. Anamuwaza Yosefe, “Ndiwe mpesa wobala pa linga,” mwaona, “pa chitsime,” madzi. Iye anapita kumeneko. Iye anati, “Inu mwadalira mwa Ambuye Mulungu. Munawupanga wanu—uta wanu kukhala wamphamvu” (United States. Mukuona?) “mwa Ambuye, koma tsiku lina mpesa umenewo unali kubwerera pamwamba pa khoma.” Ndipo apo iye ali, pomwepo tsopano. Ndendende basi zomwe iye ananena pafupifupi zaka firii sauzande zapitazo, kubwerera m'mbuyo momwe. Anamuwaza Efremu kuti iye anali ataviika mapazi ake m'mafuta, ndipo Efremu anakhazikika kumeneko kumene kuli zitsime zazikulu zamafuta. Ndendende basi.

¹³³ Kuyankhula kwa anthu amenewo, nchiyani chinali pa anthu achivundi amenewo? Mulungu akutenga minyewa yawo ndi kusuntha mwa iwo!

¹³⁴ Zinkawoneka ngati pamene Ufumu wa Chiroma unawabalalitsa iwo, pamene ena anawabalalitsa iwo, pamene iwo ankadedwa ndi Hitler, mateni a zikwi kuchulukitsa zikwi, iye anabayira thovu mmitsempha yawo ndipo iwo anafa, inu mumakhoza kuwawona matupi awo atapachikidwa pa mipanda ndi ana awo ndi china chirichonse, ndi mafupa... ndipo anatenga ndikupanga feteleza kuchokera ku mafupa awo. Amangowatenga iwo kunja uko ndi kuwabaya, nkuwayika iwo mu ngolo. Kenako amatuluka, nthawi yomwe iwo amatuluka, ngakhale poyamba, iwo anali kuyimba, “Mesiya adzabwera ndipo ife tidzamwanso magazi a mphesa kachiwiri.” Pamene iwo anapita uko, akufa, Ayuda amenewo, akuyenda kunja uko, podziwa kuti kugunda pang'ono kwinsano ndipo mtima wawo ukhala utapita. Ndipo iwo amagwera pansu, akuyimba, “Ife tidzamuona Mesiya posachedwa.” Oh, mai! Kupangira feteleza kuchokera ku mafupa awo.

¹³⁵ Ambiri a inu asilikari muno mukudziwa zimenezo ndipo munaziwona izo. Ine ndinayima pa malo pamene iwo ankawawotchera iwo ndi china chirichonse, pamene po, Hitler ndi iwo. Ndi kuyang'ana m'mwamba kwa Stalin ndi Russia ndi onse awo, anachita chinthu chomwecho. Uko nkulondola. Koma Myuda uja, vuto linali chiyani? Iye anakakamizika kubwerera ku dziko lakwawo. Apo ndi pamene iwo ayima.

¹³⁶ Tsopano, ine ndiri naye kanema wapamwamba ameneyo, *Maminiti Atatu Pasanafike Pakati pa usiku*. Pamene Ayuda amenewo analowa mkati, anali kuwafunsa iwo, anati, “Inu mukubwerera chifukwa chiyani, kuti mudzafere ku dziko lakwanu?”

¹³⁷ Anati, “Ife tabwera kuti tidzamuwone Mesiya.” Ameni. Hmm! Ife tiri pa nthawi yotsiriza.

¹³⁸ Aliyense wa ana amenewo pamene iwo ankabadwa, iwo anali nawo mwala wakubadwa. Ndipo pamene Aaroni, wansembe wamkulu pa aliyense wa ana amenewo, anali nacho chapachifuwa pa iye, chovala chake. Ndicho chimene ine ndikufuna kuti ndichisiye motalikitsa pang’ono, kuti ndilowe mu ndime iyi ya 6, chifukwa chimenecho chikubweretsamo choyimira chirichonse cha Chipangano Chakale mmenemo. Chirichonse. . . mipando yonse ndi chirichonse mu Chipangano Chakale chinali chitsanzo cha zomwe zinkawoneka Kumwamba, kutengeranso kwa munthu kachiwiri.

¹³⁹ Ndipo apa pali chapachifuwa cha Aaroni, iye anali wansembe wamkulu. Zindikirani, mwala wakubadwa wa fuko lililonse unali kuyimiliridwa mmenemo. Umodzi, mwala wakubadwa, anayika mwala wake mmenemo; fuko la Efremu, fuko la Manasse, fuko la Gadi, fuko la Benjamini, onse anayimiliridwa muno. Ndipo ndi momwe. . . Ndiye iwo amatenga miyala yakubadwa imeneyo, ngale zokongola izo, ndi kuzipachika izo pa mtengo monga chonchi. Ndipo ngati mneneri anenera, ndipo ngati izo zimveka zolondola kapena ayi, iwo ankamutengera iye ku Urimu Tumimu uyu ndi kumulola iye kuti anene ulosi wake; ngati pali Kuwala kopatulika kukubwera pamenepo ndi kuyamba kuwalitsira miyala iyi pamodzi, anali Mulungu akuyankhula moyankhira. Izo zinali za fuko lonse, onse a iwo, fuko lililonse.

¹⁴⁰ Tsopano, pa awa, mwala woyamba. Woyamba, ndi angati akudziwa yemwe mwana woyamba anali? Dzina lake anali ndani? Rubeni. Chabwino. Kodi womaliza anali ndani? Benjamin. Uko nkulondola. Mwala wakubadwa wa Rubeni unali “yaspi,” mwala wakubadwa wa Benjamini unali “sardiyo.” Iye anali woti adzawoneke ngati “Rubeni ndi Benjamini,” Woyamba ndi Wotsiriza, Iye amene Anali, Amene Ali, ndi Amene Ali mkudza, Iye anali Alefa (A) mu zilembo za Chigriki, Omega (Z) mu zilembo za Chigriki. Iye anali Woyamba, Wotsiriza, Iye anali kuyambira kwa Benjamini mpaka kwa Rubeni, kuchokera kwa Rubeni mpaka kwa Benjamini. Oh, mai! Apo Iye anali, “Wowoneka ngati mwala wa sardiyo ndi mwala wa yaspi.” Iye anali atakhala pa Mpandowachifumu uwu!

¹⁴¹ Kodi inu nonse mungafune kumuona motani Iye atakhala pa Ulemerero Wake? Tiyeni titembenezire mu Chivumbulutso

21:10, mwamsanga ndithu, ndipo tingoyang'ana pa Iye apa. Chabwino, 21:10 mpaka 11.

Ndipo iye ananditengera ine kutali mu mzimu ku phiri lalikulu ndi lalitali, ndipo anandiwonetsa ine mzinda wawukulu, Yerusalemu woyera, akutsika kuchokera kumwamba kwa Mulungu,

Ali ndi ulemerero wa Mulungu: . . . Ali ndi ulemerero wa Mulungu: ndipo kuwala kwake kunali monga mwala wa mtengo wake wapatali, ngakhale ngati . . . yaspi . . . , wonyezimira ngati krustalo;

142 “Kuwala Kwake.” Kuwala! Kodi Kuwala ndi ndani? “Ndipo Mzindawo sunkasowekera dzuwa, chifukwa Mwanawankhosa ndiye Kuwala kwake.”

143 “Yaspi, sardiyo” mwala. Ulemerero wa Mulungu ndi Yesu Khristu, Ulemerero wa Yesu Khristu ndi Mpingo Wake. Ndipo Iye anali Woyamba. Iye anali chiyani? Iye anali Chiyambi cha nthawi, Iye ali Mapeto a nthawi. Iye anali Woyamba wa mbadwa, Iye ali Wotsiriza wa mbadwazo. Iye anali Mpingo umene unali mu . . . Iye anali Mzi—Mzimu umene unali mu Mpingo wa Efeso, Iye ndi Mzimu wa Mpingo wa mu Laodikaya. Iye ndiye Woyamba ndi Wotsiriza, A mpaka Z, Woyamba, Wotsiriza, Iye amene Anali, ndi Amene Adzabwera, Muzu ndi Mphukira ya Davide, Nyenyezi ya Mmawa, Kakombo wa Mchigwa, Rozi la Sharoni! Oh, muli maudio foro handiredi ndi chinachake mu Baibulo okhudza Iye. Tangoganizani za izo, chimene Iye anali! Ndipo komabe Iye anali Ambuye Yesu wonyozeka yemwe anabadwira mu khola kwa matamando a Mulungu.

144 Chirichonse chimene chiri chodzichepetsa, penyani izo chifukwa ndizo zolondola. Chirichonse chomwe chiri chachikulu ndi chodzikuza, kotero inu musapereke tcheru ku chimenecho; mwaona, ndi mphepo yambiri, ndipo palibe kanthu kwa iyo. Chabwino.

145 Tsopano, “Iye anayenera kuwoneka ngati mwala wa yaspi ndi sardiyo.” Tiyeni tibwerere. Inu mwatero . . . ? Ife tiri ndi nthawi yochepe, sichoncho ife? Ife tiri ndi pafupifupi maminiti forte panobe. Tiyeni tizindikire, tiyeni tibwererenso ku Ezekieli 1. Bwererani mu Baibulo ku Chipangano Chakale, kwa Ezekieli, ndipo tiyeni tiwerenge apa pamene Ezekieli anamuwona Iye, nayenso. Ndipo tifanizitse Malemba awa tsopano ndi kuwona pamene ife tiri. Ezekieli mutu wa 1, chabwino, tsopano tiyeni tiwerenge kwa mphindi. Tsopano ine ndiwerenga ndime zisanu zoyambirira, ndiyeno ife tiwerenga, ine ndazilemba apa, kuyambira 26 mpaka 28. Koma tiyeni tiwerenge ndime zoyambirira tsopano za mutu 1 wa Ezekieli, mneneri. Chabwino:

Ndipo zinachitika kuti mu chaka cha sarte, ndi mu mwezi wachinayi, mu tsiku lachisanu la mwezi, . . . Ine ndinali pakati pa ansinga—pakati pa ansinga

m'mbali mwa mtsinje wa Chebar, . . . (Ndi kulondola uko, Chebar? C-h-e-b-b-r, Chebar.) . . . ndipo miyamba inatseguka, ndipo ndinaona masomphenya a Mulungu.

Ndipo mu. . . (Tsopano, penyani.) . . . Mu tsiku lachisanu la mweziwo, womwe ndi mwezi umene mfumu Yehoyakini inagwidwa,

Mawu a AMBUYE anadza momveka bwino kwa Ezekieli wansembe, mwana wa Buzi, m'dziko la . . . Akasidi m'mbali mwa mtsinje wa Chebar; ndipo dzanja la AMBUYE linali . . . pa iye.

Ndipo ine ndinayang'ana, ndipo, taonani, kamvuluvulu anatulukira kumpoto, . . .

¹⁴⁶ Penyani mneneri uyu apa, zaka faivi handiredi ndi nainte-faivi kusanachitike kudza kwa Khristu, onani momwe masomphenya ake akufananira ndi Yohane:

. . . kamvuluvulu anatulukira kumpoto, mtambo wawukulu, . . . moto ukudzitambasula wokha, ndipo kuwala kozungulira pamenepo, ndipo kuchokera mkati mwake munali mtundu wa ambara, kuchokera mkati mwa motowo.

Ndiponso kuchokera mkati mwake munatuluka mawonekedwe a zamoyo zinayi. Ndipo awa anali maonekedwe awo; iwo anali ndi mawonekedwe a . . . munthu.

¹⁴⁷ Zindikirani, mtundu wa Mzimu wa Mulungu umene unali pamwamba pa chifaniziro cha Zorengedwa zinayi izi, unali ambara. Ambara ndi chikasu-chobiriwira. Tsopano, penyani, "chikasu-chobiriwira," ambara, oh, Iye ali yemweyo dzulo . . . Iye anadziwulula Yekha kwa Ezekieli; mkati mwa masomphenya a Ezekieli, Kuwala uku kumene iye anakuona kukubwera pamwamba pa Zorengedwa zamoyo zinayi kunali kobiriwira mwachikasu. Pamene Iye anadza kwa Yohane, Iye anawonekera mu emarodi amene alinso "chikasu-chobiriwira." Iye akubwera tsopano kwa m'bvumbulutsi mu chikasu-chobiriwira. Iye amabwera kwa ife mu chikasu-chobiriwira, Kuwala! Yendani mu Kuwala, Iye ndiye Kuwala.

¹⁴⁸ Tiyeni tipite ku ndime ya 26 tsopano, kotero ife tikhoze kuweringa mpaka ya 28. Ndime ya 26:

Ndipo pamwamba pa mo- . . .

Oh, inu mukakafika kunyumba, ine ndikufuna kuti inu mulembe izo ndi kuweringa chidutswa chirichonse cha izo. Ndikusunga nthawi:

Ndipo pamwamba pa thambo limene linali pamwamba pa mitu yawo panali chifaniziro cha mwala, chowoneka ngati mwala wa sardiyo: ndipo pa

*chifaniziro cha mpandowachifumu panali chifaniziro
cha mawonekedwe a munthu pamwamba . . . pake.*

149 Ameneyo anali Mwana wa munthu, mwaona, Khristu. Tsopano penyani momwe Iye analiri, momwe Iye anavalira apa:

*Ndipo ine ndinawona mitundu ya ambara,
(penyani, mozungulira Mwana wa munthu uyu) ngati
mawonekedwe a moto mozungulira mkati mwake—
mkati mwake, kuyambira mawonekedwe a mchiuno
mwake . . .*

150 Mvetserani! Khalani auzimu, khalani omvetsetsa, ndi m'mitima yanu yomwe pano. Ine ndikukulumulirani inu mu Dzina la Yesu, zisungeni izi kwa inu nokha! Koma ingokumbukirani mmene zinaliri zodalitsira!

151 “Ine s- . . .” Tiyeni tiyambirenso mu ndime ya 27. Mvetserani, aliyense! Khalani omvetsetsa kwenikweni tsopano!

*Ndipo ndinawona ngati mtundu wa ambara
(chimenecho ndi chikasu chobiriwira), monga
mawonekedwe a moto pozungulira . . . izo, . . .*

Moto mozungulira chikasu-chobiriwira cha ambara. Tsopano:

*. . . kuyambira mawonekedwe a mchiuno mwake
mpaka kukwera m'mwamba, (Kuyambira mchiuno
mwake kupita m'mwamba.) ndipo kuyambira
mawonekedwe a mchiuno mwake . . . pansi, ndinawona
ngati mawonekedwe a moto, ndipo unali ndi
kunyezimira pozungulira. (Moto mozungulira ponse.)*

*Monga mawonekedwe a uta ndi mu mtundu mu
masiku a mvula, momwemonso anali mawonekedwe
a kunyezimirako pozungulira pake. Awa anali
mawonekedwe ndi chifaniziro ndi ulemereero wa
AMBUYE. Ndipo pamene ine ndinawona iko, ndinagwa
pa nkhope yanga, ndipo ndinamva mawu a amene
anayankhulayo.*

152 Penyani! Inu mwakonzeka? Mvetserani! Sungani izi tsopano, tangokumbukirani, kuti ndikudziwitseni. (Gene, iwe ukhoza kuyimitsa tepi iyi.) Mvetserani! (Ayi, ine sindikuyenera kuti ndiziyimitse izo pamenepo, izo ziri bwino. Ine ndikutanthauza ungoyisunga tepiyo; uyiloleze iyo kwa Mpingo.) Zindikirani izi! Tsopano, kuti inu mukhoze kudziwa kuti mtundu wa Kuwala umene uli ndi Ambuye, ndi Kuwala kwa Ambuye kumene kumawatsatira Ambuye, ndipo kuli ngati Ambuye, ndi ambara, chikasu-chobiriwira. Ndiwo mtundu womwewo wa Kuwala umene uli nafe lero, monga asayansi ajambula chithunzi Chake, chikasu-chobiriwira, ambara.

153 Ndiri mnyamata wamng'ono, ndipo ndakuwonapo Iko kwa nthawi yanga yoyamba, inu mukukumbukira, akale kuno.

Ine nthawi zonse ndinkakuwuzani inu chithunzi chenicheni chisanajambulidwe, “Chinali chikasu-chobiriwira, komwe ndi ambara.” Tsopano, kuti ndikudziwitseni inu kuti Mzimu wa Ambuye. . .

¹⁵⁴ Iye anati, pamene iye anakuwona iko kuchokera mchiuno cha Cholengedwa chamoyo chimene chinayima pamaso pake, “Kuchokera mchiuno mwake kupita m’mwamba munali monga moto, Kuwala kochokera mchiuno mwake kupita pansu, anali wozingidwa ndi Kuwala. Ndipo pozungulirapo panali mitundu yambiri ngati utawaleza.” Ndi kulondola uko?

¹⁵⁵ Ndikufuna kuti inu mukumbukire, Mulungu akadapezekabe m’mitundu yomweyi, “kuyambira mchiuno kupita mmwamba, moto, mtundu wa ambara,” kujambulidwa ndi kamera ya kanema kapena ndi kamera ya mtundu, “ambara kuchokera mchiuno kupita mmwamba, kuchokera mchiuno kupita pansu, ndi pozungulira konse, mitundu yambiri monga iliri mu utawaleza m’mwamba ikatha mvula.” Yesu Khristu yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse! Mzimu Woyera ukadali mu mphamvu Yake, ukadali mu Mpingo Wake m’masiku otsiriza ano. Ndi zimenezotu. Osati ine, ine ndinangoyima pamenepo, koma chinali chithunzi chomwe chinajambulidwa. Ine ndikufuna kuti inu muyang’ane pa zimenezo, ndendende basi zomwe Ezekieli anaziwona. Mitundu yofanana, mwanjira yomweyo, ndipo inkachita mwanjira yomweyo, ndipo kunyezimira mwanjira yomweyo, kwa Zolengedwa zamoyo. Ndi chiyani icho? Zolengedwa zamoyo zikuyimira Mpingo wamoyo, Mpingo umene ukukhala moyo ndi mphamvu ndi chiwukitsiro cha Khristu. Mitundu ya ambara yomweyo yachiphimba icho kuyambira mchiuno kupita mmwamba, kuchokera mchiuno kupita pansu.

¹⁵⁶ Palibenso zongopeka, sayansi yajambula zithunzizo! Tayang’anani pa mitundu yawo, tangoyang’anani pa mitundu ya motowo mmenemo. Mukuona? Utawaleza. Yang’anani mtundu uwu wa emerodi wachikasu. Tsopano, pa kamera *iyi*, inali kamera chabe ya wojambula wowongoka. Pa kamera *iyi* panali mtundu, zithunzi zamitundu, mtundu wa Kodachrome. Tayang’anani pa mitundu ya emarodi mmenemo. Ngati ine ndikanakhoza kuyiyika iyo powala penapake pamene inu mukanakhoza kuziwona izo kumbuyoko. Mukukhoza kuwona tsopano? “Monga utawaleza,” tayang’anani pa mizereyo ikubwera m’mbuyo ndi mtsogolo monga utawaleza, uliwonse mtundu wosiyana. Tilowa mu zimenezo m’amaminiti ochepe, ndi mitundu yanji imeneyo ndipo iyo ikuwonetsera chiyani?

¹⁵⁷ Oh! Izo zimangopangitsa mtima wanga wosauka kudumphu ndi chisangalalo. Ndipo kudziwa kuti mu tsiku lino limene ife tikukhalamo, Khristu ameneyo. . .pamene maziko ena onse ali mchenga wotitimira, maziko ena onse. Ine ndikuganiza, “Chifukwa chiyani ine sindingathe kunena zimenezo? Chifukwa

chiyani ine sindingathe kulipangitsa dziko kuti liziwone Izo?" Dziko silinapangidwe kuti liziwone Izo. Dziko silidzaziwona Izo, iwo sadzaziwona Izo! Koma Mpingo ukulandira kugwedezeka kwamphamvu kumene Iwo unayamba wakhalapo nako!

158 M'masiku amenewo iwo sakanakhoza kujambula chithunzi cha Izo. Iwo akhoza tsopano chifukwa iwo ali ndi zipangizo za makina. Iwo amene amayesera kutenga zimango kuti azimukana Mulungu, amabwerera mozungulira ndi kudzatsimikizira kuti kuli Mulungu. Uko nkulondola, "Emerodi." Tsopano, inu mukukumbukira, ine sindinazipeke izo, ine ndikuwerenga zimenezwa kwa inu kuchokera mu Baibulo momwemo. Penyani pamene ine ndikuwerenga, ndi kuyang'ana, ndipo onani kuti Iye ali Ambuye Mulungu yemweyo, palibe kusiyana. Penyani ndime ya 27:

Ndipo ine ndinawona . . . mtundu wa ambara, ngati mu mawonekedwe a moto . . .

159 Mwaona, ngati malawi akuyaka. Mwaona? Mitundu ya ambara ikuchokera mu moto. Inu mukuziwona izo tsopano? Ambara, *iyi* ndi mitundu ya ambara ikubwera kuchokera mu moto. Pansi apa ikuti:

Ndi mawonekedwe ngati uta, kapena utawaleza, mu masiku itatha mvula, . . . utawaleza, mu masiku itatha mvula, . . .

160 Ndipo panali a—a "Cholengedwa chamoyo." Chimene Yohane ankayimira, Mpingo wonse, unatengedwera m'mwamba. Ine ndinakuwuzani. Munthu mmodzi pano m'masomphenya akhoza kuyimira Thupi lonse la Khristu, lophimbidwa! Tsopano, penyani:

Ndipo ine ndinawona . . . mtundu wa ambara, ngati mawonekedwe a moto . . . pafupi ndi izo, ndipo mawonekedwe . . . kuyambira mawonekedwe a mchiuno mwake kufikira m'mwamba, ndipo kuyambira mawonekedwe a mchiuno mwake kufikira pansu, ine ndinawona ngati mawonekedwe a moto, . . .

161 Penyani, *taonani* pa kupopera moto. Kuchokera ku chiyani? Utawaleza, mitundu seveni. Tsopano, penyani, pali ndendende mitundu seveni *pamene*, ndipo utawaleza uli ndi mitundu seveni.

. . . Ine ndinawona ngati mawonekedwe a moto, ndipo unali ndi kuwala pozungulira pafupi.

Monga mawonekedwe a utawaleza umene uli m'mitambo mu tsiku la mvula, momwemonso mawonekedwe a kunyezimirako pozungulira pafupi. (Kuzungulira Mpandowachifumu wa Mulungu, mwaona.) Awa anali mawonekedwe a chifaniziro cha ulemere wa AMBUE.

¹⁶² Osati *Ambuye*, tsopano, *ulemerero wa Ambuye*. Ulemelero wa *Ambuye* ukuphimba Mpingo Wake chifukwa Iye ali mu Mpingo Wake! Ameni! Oh, izo zikumveka zopusa kwa opanda nzeru, koma momwe Izo ziliri zazikulu kwa iwo amene amakhulupirira. Uh-huh.

...Awa anali mawonekedwe ndi chifaniziro cha ulemerero wa AMBUYE. Ndipo pamene ine ndinawona izo, ndinagwa pa nkhope yanga, ndipo ine ndinamva liwu likuyankhula...

¹⁶³ Tsopano iye akupita patsogolo ndi kunena chimene masomphenyawo amatanthauza, chimene ife tiribe nthawi yoti tilowemo mmawa uno.

¹⁶⁴ Tsopano zindikirani momwe *Ambuye* mu chifundo Chake chachikulu amatipatsira ife zinthu izi.

¹⁶⁵ Tsopano tiyeni timutenge wina. Onse awiri Ezekieli ndi Yohane anamuwona Iye mu chinsinsi cha mitundu Yake ndi Kuwala, ndipo anawutcha Iwo “mtundu wa ambara.” Yohane pambuyo pake... Inu amene mukuyika... mukulemba Malembawa, Yohane Woyamba 1:5 mpaka 7. Yohane, pambuyo pake (ndipo iye anali pa chisumbu cha Patmo pafupifupi zaka zitatu pamene iye ankalemba Bukhu), pamene iye anabwerera, bambo wachikulire mu zaka zake za mma nainte, mu Yohane Woyamba 1:5 ndi 7, iye anati, “Mulungu ndi Kuwala.” Yohane anali nacho chomuchitikira, anali atamuwona Iye ndipo anadziwa kuti Iye anali Kuwala, Kuwala, Kuwala Kwamuyaya; osati kuwala kwa dziko, osati kuwala kwa nyali, kuwala kwa magetsi, kuwala kwa dzuwa, koma Kuwala Kwamuyaya! Oh, momwe ine ndimamukondera Iye. “Mulungu ndi Kuwala.”

¹⁶⁶ Zindikirani, ife tiyambira m’mbuyo tsopano ndi kuwona pamene ife tiri. Pa ndime ya 3 panobe, sichoncho ife? Kodi ife tizipeza Izo? Ine ndikuyembekeza. Chabwino:

...iye...anali kuoneka ngati mwala wa yaspi ndi sardiyo: ndipo panali utawaleza...pafupi ndi mpandowachifumu, mu mawonekedwe ake monga emerodi. (Chikasu-chobiriwira.)

¹⁶⁷ Tsopano, “utawaleza,” inu mukuzindikira kuti iwo unali utawaleza. Tiyeni tibwerere m’mbuyo mu Genesis 9 ndi kupeza, mu Genesis 9:13. Ndipo ife tikupeza kubwerera apa “utawaleza,” pamene utawaleza unawonekera koyamba. Genesis mutu wa 9, ndipo ife tiyambira pa ndime ya 13, Genesis 9:13. Nonse inu mukuzifuna Izo? Oh, ine ndimazikonda Izo! Ine sindimangozifuna Izo, Ine ndimazikonda Izo! Tayang’anani:

Ine ndayika utawaleza wanga mu mitambo, ndipo icho chidzakhala chizindikiro (Penyani!), chizindikiro cha pangano pakati pa ine ndi dziko lapansi.

168 Chiyani? “Pakati pa Ine ndi Nowa”? Ayi. “Pakati pa Ine ndi dziko lapansi.”

Ndipo zidzachitika kuti, pamene Ine ndidzabweretsa mtambo padziko lapansi, kuti utawalezawo udzawonedwe mu mtambo:

Ndipo ine ndidzakumbukira pangano langa, limene—limene liri pakati pa ine ndi inu . . .

169 Tsopano Iye wabwerera ku pangano Lake pakati pawo, koma pangano la utawaleza . . . Mwaona, pangano linali moyo kwa Nowa, kuti Iye anamupulumutsa iye, koma pangano limene Mulungu anapanga ndi Iyemwini linali utawaleza, kuti Iye sakanatero . . . Tsopano, ine ndikusonyezani inu chimene pangano la Nowa linali ndi Mulungu, mu miniti. Koma ili apa linali pangano Lake lomwe la Mulungu ndi Iyemwini, ameni, utawaleza.

170 Tsopano, ife tikupeza kuti pangano nthawi imeneyo ndi “chizindikiro,” chizindikiro. Mulungu anati chinali “chizindikiro” apa, sichoncho Iye? Mukuona?

Ine . . . ndayika wanga . . . Ine ndikuyika utawaleza wanga mu mitambo, (Ndizo pambuyo pa chiwonongeka cha dziko, kuwonongeka ndi madzi; mnofu wonse, kupatula Nowa—Nowa, unawonongedwa.) ndipo icho chidzakhala chizindikiro cha pangano pakati pa ine ndi dziko lapansi.

171 Osati “Ine ndi dziko lapansi.” Dziko ndi “kosmos.” Mwaona? Koma izi ziri “pakati pa Ine ndi dziko.” Mulungu anati, “Ine ndinapanga dziko limenero. Ndipo ine ndinalichonderera ilo moyipa kwambiri, mwakuti ine ndinangolitembenuza ilo mozondoka ndi kulimiza ilo mzidutswa. Ndipo—ndipo ine—ine—ine—ine—sindinkayenera kuchita izo, mwinamwake.” Iye anati, “Ine—ine ndinamva chisoni kwambiri, chinali chinthu choyipa kwambiri.”

172 Kodi mukuganiza kuti chidzakhala chiyani pamene Iye adzabwera mu mkwiyo Wake tsopano? Khala molondola, mzanga wochimwa.

Oh, khalani oyang’anira ndi kudikirira kuti muwone;

Iye akubweranso kachiwiri.

Inu mukukhulupirira zimenezo?

Iye akubweranso kachiwiri.

Ine ndimazikonda zimenezo, sichoncho inu?

Oh, kodi inu mungawerengedwe ngati mmodzi wa mdani Wake?

Ine sindikanafuna kuti ndikhale chimenecho. Mungatero inu? Ayi, bwana. Kukhala mdani kachi- . . . kapena, kukhalani

mdani wa Iye, kukhala ndi Iye zikanakhala bwino. Koma kutsutsana Naye!

Khalani opanda banga mkati, khalani
ong'anira ndi kudikirira kuti muwone,
Iye akubweranso kachiwiri. (Hmm!)

173 Tsopano, pangano, chizindikiro cha chiyani? Chizindikiro cha chiyani? Cha nsembe imene yalandiridwa. Tsopano pezani Genesis 8:20 ndi 22. Tsopano, Genesis 8:20 ndi 22, chabwino, kudutsa tsamba lomwe izo ziri.

Ndipo Nowa anamangira AMBUYE guwa la nsembe; ndipo anatenga...nyama iliyonse yodyedwa, ndi... mbalame yodyedwa iliyonse, ndipo anapereka nsembe zopsereza pa guwa la nsembe.

Ndipo AMBUYE ananunkhiza fungo lokoma; ndipo AMBUYE anati mu mtima mwawo, Ine sindizatembereranso nthaka (kutemberera nthaka) konse chifukwa cha munthu; pakuti lingaliro la mu mtima wake liri loyipa kuyambira ubwana wake; ngakhalenso Ine sindizakanthanso konse chinthu chirichonse chamoyo, monga Ine ndachitira.

174 Ndipo tsopano ife tikhoza kuwerenga ndime yotsiriza:

Ndipo...Pakukhala dziko lapansi, nthawi yodzala ndi yokolola, . . . kuzizira ndi kutantha, . . . chilimwe ndi chisanu, . . . usana ndi usiku sizidzatha. (Pangano.)

175 Chinthu chomwecho chimene Yohane anawona: Yesu, pangano lovomerezedwa ndi Mulungu litazungulira miyamba. Ndipo pomuzungulira Iye panali utawaleza mozungulira Mpandowachifumu, pamaso pake monga emarodi, Kuwala kobiriwira kwa ambara mozungulira Mpandowachifumu. Matamando akhale kwa Mulungu!

176 Penyani! Wa Nowa unapangidwa makamaka . . . Utawaleza wa Nowa unapangidwa makamaka ndi mitundu seveni. Aliyense amadziwa kuti utawaleza uli ndi mitundu seveni. Tsopano, kodi mitundu yake ndi yotani? Kufiira, oranje, vayoleti, ayi, kufiira—kufiira, oranje . . . wobiriwira, buluu, indigo, ndi vayoleti. Ndiyo mitundu ya utawaleza. Tsopano, ife tiri ndi chinthu chakuya apa, ndipo ine ndikungoyenera kuti ndikhudze malo ofunikira a icho chifukwa tikufika pochedwa kwambiri. Tsopano, kumbukirani, oranje, kapena, kufiira, oranje, chikasu, kubiriwira, buluu, indigo, ndi violet.

177 Tsopano, ngati inu mungazindikire, seveni. Penyani. Mautawaleza seveni . . . mitundu seveni, ine ndikutanthauza, utawaleza wa mitundu seveni. Izo zinkatanthauza mauta seveni! Mauta seveni, mipingo seveni ikunyezimiritsa nyali seveni, kuwala kulikonse kumakutidwa mu umzake. Zinayamba ndi kufiira, kufiira. Pambuyo pa kufiira panabwera oranje,

chomwe ndi chinyezimiritso cha kufiira. Pambuyo pa oranje . . . pambuyo—pambuyo pa oranje panabwera chikasu, chomwe ndi kufiira ndi oranje zosakanizidwa pamodzi, zimapanga chikasu. Kenako kubiriwira. Kubiriwira ndi buluu zimapanga kuda. Kenako panabwera indigo. Ndipo kenako kuchokera ku indigo panabwera violet, womwe ndi gawo la buluu. Aleluya! Kodi inu simukuwona? Mulungu, mu utawaleza Wake wa mitundu seveni, pangano Lake limene Iye analipanga, pangano kuti kudzera mu Mibadwo Seveni ya Mpingo, mitundu seveni, Iye akanati adzapulumutse dziko lapansi.

¹⁷⁸ Kodi Iye akanachita chiyani? Kumbukirani, Iye anawupanga iwo ndi dziko lapansi, mtundu Wake. Koma tsopano penyani. Utawaleza uwu wokha, mopingasa, umangokuta (mu uta) theka limodzi la dziko lapansi. Ndizo zonse za mitundu ya utawaleza wa Nowa, basi . . . unakuta, theka chabe la dziko lapansi. Unali mu ngowe, ndizo zonse zomwe inu mukhoza kuwona. Koma pamene Yohane anamuwona *Iye* mu mtundu Wake wa emerodi, Iye anazinga Mpandowachifumu wonse wa Mulungu. Theka linali lisanauzidwebe konse. Iye anaphimba . . . Iye basi . . . dziko lapansi limangopanga ngowe, ndi theka chabe la ilo; ndiyo mibadwo ya mpingo.

¹⁷⁹ Koma pamene Yohane anamuwona Iye mu mtundu uwu wa ambara, mtundu wa ambara, Iye anazungulira ndi kuphimba mozungulira ngati lawi. Lawi! Lawi la mtundu wa ambara, Linazungulira umunthu Wake! Mukuona? Mtundu umodzi, Mulungu mmodzi pamwamba pa onse, kudzera mwa onse, ndi mwa zonse, koma pali Mibadwo Isanu ndi iwiri ya Mpingo.

¹⁸⁰ Penyani diamondi wamkulu. Ankakonda kumawapeza iwo . . . inu mukhoza kuwapeza iwo mu Africa ali mmisewu. Inu simungayerekeze kusunga mmodzi, chifukwa sanadulidwe. Inu mukapezeka naye mmodzi yemwe siwodulidwa, iwo akutsekerani inu chifukwa cha izo pakali pano, ndi kukupatsani inu chigamulo cha moyo wanu wonse chifukwa chosunga izo. Inu mukuyenera, muperekeni iye mwamsanga pamene mwangomupeza iye.

¹⁸¹ Tsopano, iwo amatenga daimondi uyu . . . Oh, ndi chinthu cholimba. Ine ndawonapo chigayo chachikulu cha matani forte chikuyimirira monga *chonchi*, iwo amatsanulira mwala wabululuwo mmenemo, kuwugaya iwo mozungulira, icho chimaphwanya mwala umenewo nkungokhala ngati phulusa, koma icho sichimaphwanya diamondi. Cha matani forte chimenecho chitapachikidwa pa chozungulira, pamwamba *apa*, chikugudubuzika ndi zingwe zazikulu zimenezo monga choncho, chikungophwanya mwala umenewo kukhala zidutswa; koma daimondi amadutsa momwemo, iye amasuntha mataniwo forte apo. Oh! Pamene iye waphwanyidwa ndi kutsika pansu kudzera mu sefa, amasefekera pansu ku zosefera zina, amatsukika ndipo kenako potsiriza amapita panjira yayitali.

182 Woyang'anira wamkulu wa Kimberley Diamond Mines anali mmodzi wa ondithandizira anga kumusi uko mu mzere, wodzichepetsa kwenikweni, m'bale wokoma.

183 Ndiyeno kwa pafupifupi mapazi atatu pamwamba pa madzi amenewo, kumene iwo amayenda, ndi, Cosmoline amayikidwa pamenepo. (Inu mukudziwa, chiyani—chinthu ichi inu mumachitcha chiyani? A... Meda, ndi chiyani chomwe ife tiri nacho mu chigubu mu kabati mmenemo? Vaseline!) Ndipo ife timayika Vaseline ameneyo, pafupifupi inchi kuya kwake, pamwamba apa pa choyendetsa. Ndipo iwo umabwera pansi, ndipo zindikirani, nthawi iliyonse yomwe mwala umenewo ubwera pamenepo, iwo umagudubuzika kuchokera pa Vaseline ameneyo; koma pamene daimondi abwera pamwamba pake, amamatirira. Daimondi ndi wowuma ndipo amamatirira pamenepo. Ine ndawonapo iwo akumutola iye, ngakhale tizidutswa tating'ono timeneto, ndi kutilekanitsa ito ndi magalasi a maso. Ndipo ine ndinawafunsa iwo chimene iwo amachitira zimenezo, iwo anati amazigulitsa izo ku Amerika kwa mashingano a Victrola ndi zinthu; iwo samaperepeseka, mwaona.

184 Koma ma daimondi aakulu amenewo, tsopano, apo iwo ali, mpira umodzi wokha waukulu. Koma pamene... Iwo amawatenga iwo ndi kutenga makina amagetsi ndi kuwadula iwo, ndi kupanga daimondi wodulidwa. Ndiye akamudula iye, iye ndi woti azinyezimiritsa mitundu yamoto ya m'bulu wake, ndipo iye amanyezimiritsa mitundu seveni, nayenso.

Oh, momwe kuti Yesu. . .

185 Oh, inu mukhoza kukhala ndi ndalama zambiri, inu mukhoza kukhala ndi ma Cadillac ambiri, inu mukhoza kukhala m'busa wa nyumba ina yayikulu yosungiramo mitembo kapena tchalitchi chachikulu cha chinachake, inu mukhoza kukhala bishopu kapena akibishopu, koma, oh, m'bale, pamene inu muyipeza Ngale imeneyo, Daimondi ameneyo, munthu amagulitsa chuma chake chonse chimene iye ali nacho, amachipereka icho, china chirichonsecho.

186 Tayang'anani pa namwali wogonayo. Oh, kodi iye anachita chiyani? Iye anayenera kugulitsa chinachake kuti agulire Mafuta ake. Kodi iye ankayenera kugulitsa chiyani? Zikhulupiriro zake zakale ndi zipembedzo ndi zinthu. Iye anagulitsa zonse zomwe iye anali nazo kuti amupeze Khristu, Khristu, Ngale yopambana imeneyo. Yesu, thupi limenero... [Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi]. . .? . . . Ine ndiri ndi tikiti yopitira Kumwamba pamene sitimayo ibwera, umodzi wa mmawa wamdima uwu. Oh, dalitso lakelo!

Oh, kofunika ndi kuyendererako
Komwe kumandiyeretsa ine monga chipale;
Palibe kasupe wina yemwe ndimdziwa,

Si china koma Magazi a Yesu.

¹⁸⁷ Palibe kutchuka, palibe zinthu zazikulu, palibe kanthu, palibe chuma, osati—osati kalikonse, ingondipatsani ine Kuyenderera kofunikako. Ndizo zonse!

Palibe chomwe ndikubweretsa mmanja
mwanga,
Mophweka ku Mtanda Wanu ine
ndikukangamira.

¹⁸⁸ Ngale yopambana ija! Chinali chiyani Icho? Chinali changwiwo. Zinali pa usinkhu wa zaka sarte-firii ndi theka pamene Mulungu anayiyika Iyo kudzera mu makina opunthira aakulu, pamene Iye anayitengera Iyo pamenepo ndi kuyamba kuyiwumba Iyo. Iye anayidula Iyo, Iye anayiphwanya Iyo, Iye anayivulaza Iyo.

*. . . iye anavulazidwa chifukwa cha zolakwa zathu, . . .
anatunduzidwa chifukwa cha kusaeruzika kwathu:
chilango chotitengera ife mtendere chinali pa iye; ndipo
ndi mikwingwirima yake ife tinachiritsidwa.*

¹⁸⁹ Kodi Mulungu anachita chiyani kwa Munthu wangwiwo ameneyo? Alipo m'modzi yekha wa iwo mu dziko, m'modzi yekha mu dziko, ndipo ameneyo anali Iye! Ndipo Mulungu anamusema Iye apa, "Iye anavulazidwa chifukwa cha zolakwa zathu." Chifukwa ine ndinali wochimwa, Iye analola Kuwala kwa utawaleza kwa Mibadwo Yake Seveni ya Mpingo kuwalire pa ine, kudziwa kuti Iye anavulazidwa chifukwa cha zolakwa zanga.

¹⁹⁰ Apo pali utawaleza wanu wa mitundu seveni. "Iye anatunduzidwa chifukwa cha kusaeruzika kwathu, chilango cha mtendere wathu chinali pa Iye, ndi mikwingwirima Yake ife tinachiritsidwa." Mulungu anamudula Iye, ndipo anamutunduzira Iye, ndi kumuphwanya Iye, ndi kumudula Iye, kuti Iye akhoze kunyezimiritsa kudzera mu zilonda Zake zakufa, chikhululukiro cha tchimo, chimwemwe, mtendere, kuleza mtima, ubwino, chifatsa, unjonda. Mizimu seveni ya Mulungu ili zipatso seveni za Mzimu zomwe zikanadzanyezimiritsa kubwerera kwa anthu Ake. Iye anatunduzidwa, kuwumbidwa ndi kupangidwa, kuti Kuwala kwa Mulungu kowalira kudzera mu thupi la Munthu mmodzi ameneyo kukhoze kuwombola dziko lonse lapansi; "Ine ndidzakwezedwa kuchoka pa dziko lapansi, Ine ndidzakokera anthu onse kwa Ine." Penyani mitundu ya utawaleza imeneyo pamene ikunyezimira.

¹⁹¹ Koma pamene Yohane anamuwona Iye apa, chinali chiyani icho? Tsiku la kuwombola linali litatha. Izo zonse zinali zitatha, kotero anamuwona Iye atabwerera mu chikhalidwe Chake chapachiyambi, mtundu wa ambara. Osati theka chabe la dziko lapansi, lingakhoze basi . . .dzuwa, limangokhoza kuwalira pa theka la dziko pa nthawi, mwaona, pamene ilo likuzungulira.

Koma pamene Yohane anamuwona Iye, Iye anali atakhala akuwoneka ngati mwala wa yaspi ndi sardiyo, mitundu ya ambara; mukasakaniza ziwirizo pamodzi, inu muli ndi ambara. “Ndi mtundu wa ambara kuzungulira Mpandowachifumu!” Oh, mai! Oh, ine—ine ndikukuuzani inu, izo basi...ife tikhoza kumangopitirira ndi kupitirira.

¹⁹² Mizimu seveni, mitundu seveni, mibadwo seveni ya mpingo, atumiki seveni, zowunikira seveni, chirichonse chiri mu seveni. Mulungu ndi wangwiro mwa “seveni.” Mulungu anagwira ntchito masiku sikisi; tsiku lachiseveni, Iye anapumula. Dziko lidzakhalapo zaka sikisi sauzande, ndipo lachi seveni sauzande ndi Zakachikwi.

¹⁹³ Zindikirani, *mu theka la mkombero*, “theka silinadziwikebe.” Tsopano, ndithudi zinthu izi zikuyimira chinachake.

¹⁹⁴ Tsopano, mu Eksodo 23:13 ndi mu Aheberi 6:12, Mulungu anapanga pangano ndi Iyemwini ndipo analumbira pa Iyemwini. Aheberi :13 amatiuza kuti, kapena 9, :13, kuti “Iye analumbira pa Iyemwini.” Panalibe wamkulu woti nkulumbirirapo pamene Iye anamuwuzira Abrahamu ndi Isake, pamenepo Iye anamuwuzira Abrahamu kuti adzachita naye pangano, pangano losatha. Mulungu . . .

¹⁹⁵ Pangano limapangidwa nthawi zonse ndi lumbiro, kotero palibe aliyense . . .Iwe umatenga lumbiro pa winawake wamkulu kuposa iwe; kutenga lumbiro pa amayi ako, kutenga lumbiro pa fuko lako, kutenga lumbiro pa chinachake, kutenga lumbiro pa Mulungu. Koma inu simungakhoze kutenga lumbiro pokhapokha ali winawake wamkulu kuposa inu.

¹⁹⁶ Ndipo panalibe wina wamkulu kuposa Mulungu, kotero Iye anadzilumbirira Iyemwini, pa Iyemwini. Amen! Kulumbira pa Iyemwini kuti Iye adzatsimikizira pangano ili. Amen. Oh! Fyuu! Analumbira pa ilo, Iye akanadza “sunga Mbewu ya Abrahamu.” Kodi Mbewu ya Abrahamu ndi chiyani kwa Amitundu? Ubatizo wa Mzimu Woyera, Mbewu ya Abrahamu. Analumbira pa Iyemwini, “Ine ndidzawakweza iwo, aliyense, m’mwamba. Ine ndidzawapatsa iwo Moyo Wamuyaya ndi kumwayika iwo kumbuyo kuno pa dziko lapansi.” Zomwe ife tiyenera kuchita - . . .kuti tiganizirepo?

¹⁹⁷ Kotero ife tikumuwona Iye mu uta wozungulira wobiriwira, mtundu wa ambara. Wobiriwira uwu, kubiriwira kumayimira chiyani? Moyo. Chobiriwira ndi chobiriwira nthawi zonse, chimakhala chobiriwira nthawi zonse, ndi moyo. Zikutanthauza chiyani? Kuti Mulungu analonjeza, monga Iye anatenga lumbiro kumbuyo uko mu Genesis, kuti Iye “sakanati . . .” (Anayika utawaleza m’mwamba.) kuti Iye “sadzawononganso dziko ili ndi madzi.” Iye akutenganso lumbiro Lake nalumbira pa Iyemwini kuti Mbewu yonse ya Abrahamu Iye adzayiwickitsa, ndipo

dziko lapansi ili lidzayima pa ziweruzo zake zonse zogwedeza. Ziweruzo zomwe tikudutsamo m'maphunziro amtsogolo omwe tiri nawo akubwera, ndidzakusonyezani inu kumene dziko ili lidzageya ndi kusanduka ziphala zamoto, ndi kuphulika mzdutswa, ndi kutembenezika ndi chirichonse. Koma Iye walumbirira pa Iyemwini kuti Iye sadzaliwononga ilo, koma Iye adzalisalaza ilo kachiwiri ndi kuyikapo ana Ake pa dziko lapansi kwa Zakachikwi zimenezo. Oh, mai!

Ine ndikuyang'anira kudza kwa tsiku
lokondwa la Zakachikwi limenero,
Pamene Ambuye wathu wodala adzabwera
ndi kudzamutengera Mkwatibwi Wake
woyembekezera kupita;
Oh! Mtima wanga ukulakalaka, kulirira tsiku
lomasulidwa lokomalo,
Pamene Mpulumutsi wathu adzabweranso
padziko lapansi kachiwiri.

¹⁹⁸ Oh, momwe ife tikufunira kuliwona Tsiku limenero, Iye analonjeza kuti Zakachikwi zazikulu zidzabwera. Ndipo chinthu china, chifukwa chimene Iye anazunguliridwa, Iye ndi Mulungu wosunga pangano. Iye adzasunga pangano Lake!

¹⁹⁹ Tsopano tiyeni titenge ndime yotsatira, mulimonse. Mai, ife tikufuna kuti titenge imodzi inanso, ndipo ife tiri nawo pafupifupi maminiti teni, fifitini kuti tichite zimenezo. Kodi inu mwatopa kwambiri? Inu mukufuna kupitirira patsogolo? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi.] Chabwino, tiyeni titenge ndime ya 4:

*Ndipo pozungulira pafupi ndi mpandowachifumuwo
panali mipando foro ndi twente: ndipo pa mipandopo
ndinaona akulu foro ndi twente atakhala, ovekedwa
ndi zobvala zoyera; ndipo anali nawo pa mutu pawo
akorona agolide.*

²⁰⁰ Ife mwina sitingathe kuwerenga ndime yonseyo. Chabwino, tiyeni tiyambe. Ndime ya 4, penyani tsopano, pamene Yohane anamuwona Iye, mtundu wa emerodi umenewo pomuzungulira Iye, ife tiri nayo mitundu yonse, utawaleza, ndi zina zotero, ndi zimene izo zonse zinali. Tsopano, pa ndime ya 4, chinthu choyamba iye akuchiyankhula apa, pa ndime ya 4 ind- . . .

Ndi kuzungulira mpandowachifumu . . .

²⁰¹ Penyani! Ndi chithunzi chokongola apa, musaphonye icho, "Mpandowachifumu."

²⁰² Inu mukudziwa, tiyeni tibwerere kwa Mose. Mose . . . Ife tiribe nthawi yoti tizifukule izo, kotero inu mungotenga zomwe ine ndikunena. Mose, pamene iye anapatsidwa masomphenya pa Phiri la Sinai . . .

203 Ine ndikufuna inu muzindikire kuti uwu siunali Mpandowachifumu wachisomo aponso. Pamenepo, magazi anali atapita, ndipo nsembe inali itabwereranso ndipo iwo anali atalandiridwa, ndipo magazi anali atachoka pa mpando wachifundo. Ndipo tsopano unali mpando wachiweruzo chifukwa mabingu ndi mphezi zinatuluka mmenemo. Ndi kulondola uko?

204 Kumbukirani, zinali ngati Phiri la Sinai. Pamene Mose anakwera Phiri la Sinai, nchiyani chinachitika? Bingu, mphezi. Ndipo ngakhale ngati ng'ombe, kapena mwana wa ng'ombe, kapena nkhosa, kapena wina aliyense, angakhale kungokhudza phirilo, chinkayenera kufa. Baibulo linati, "Chivomerezicho chinali chachikulu kwambiri kufikira Mose anachiwopa icho." Ndipo Mos-. . .Iye anati, "Vula nsapato zako pano, uli pa malo Oyera." Yoswa wankhondo wamkulu, anali woti awatengere anawo kumeneko ndi kukawagawira cholowa chawo, amangokhoza kukwera theka la phirilo.

205 Apa panayimirira Mose pamwamba apo ndi mitundu ya kuwala kwa Mulungu ndi mphezi ndi ma emarodi pomuzungulira iye, kupenyereka malamulo amenewo akulembedwa. Akuyima mu Kukhalapo kwa Mulungu, Liwu limenero likuyankhula momveka, "Mose, iwe uli kuti? Vula nsapato zako, uli pa malo Oyera."

206 Mpando wachiweruzo, iwo unali tsopano, palibe chimene chikanakhoza kuyima pamenepo koma owomboledwa. Wochimwa sakanakhoza kuziyandikira izo nkomwe (izo zatha), mpando wachiweruzo. Chabwino.

207 Tsopano, Mose anapanga zinthu pa dziko lapansi, anapanga kachisi, monga zinthu zimene iye anaziwona Kumwamba. Ife tikudziwa zimenezo, sichoncho ife? Ife tikupeza kuti Paulo anachita chinthu chomwecho. Tiyenera kutero. . .Ahebri 9:23, kuti Mose anapanga zinthu monga mmene iye anachitira. Ndipo Paulo m'masomphenya ake pamene iye anapita Kumwamba (pamene iye anaphunzitsa Bukhu lalikulu lija la Ahebri), iye ayenera kuti anaona m'masomphenya ake chinthu chomwecho chimene Mose anachiwona, chifukwa iye ananena kuti (iye anaphunzitsa Bukhu lodabwitsa limenero la Ahebri), momwe kuti Chikhristu chinali choyimira cha Chipangano Chakale. Iye anali mphunzitsi wamkulu, Mo-. . .Paulo anali. Tsopano, umenewo unali Mpandowachifumu Wake *pamenepo*. Ndiye mu. . .

208 Tiyeni basi. . .Palibe ntchito, ine sindingathe. . .Ine ndikanati ndizidutse izi, koma ine sindingakhoze basi kuchita zimenezo. Bolodi lakuda liri kuti? Kodi munalipititsa kumbuyo? Ilo liri kumbuyo, Doc? Chabwino, mwinamwake ine ndikhoza kukuwonetsani inu kuchokera apa. Ine-ine. . .Tsopano, tengani mapensulo anu ndi pepala, pakuti ine ndikufuna kunena

chinachake apa. Ine—ine ndinali nditakhala mmawa uno pamene chinachake chinabwera kwa ine. Tsopano ine ndikuwuzani inu chimene ine ndinachita, ngati inu mungazindikire, ine ndazijambulira izo kumbuyo apa. Mukuona? Kungochijambula icho monga Mzimu unachiperekera icho kwa ine, mwaona, chojambula apa cha chomwe chiti chidzakhale. Koma ine—ine ndikufuna kunena chinachake pomwe pano.

²⁰⁹ Tsopano, Mulungu, pamene Iye adzadzodzedwa, Iye ndi Woweruza pamene. Ndi kulondola uko? Kodi woweruza amaweruza liti? Pamene iye afika pa mpando wake woweruzira, mpandowachifumu. Tsopano, ine ndikufuna inu muwone momwe Chipangano Chakale chinapangidwira, momwe mabwalo oyandikira ku Mpandowachifumu Wake anapangidwira, ndi momwe Yohane anawonera apa. Ife sitifika ku zimenezo mmawa uno, zonse za izo. Koma momwe Yohane anawonera mabwalo omwewo akuyandikira kwa Iye, ndi chomwe kuyandikira kwa mabwalo Ake kuli. Tsopano, oh, ine ndikuzikonda izi.

²¹⁰ Tsopano, mu Chipangano Chakale, munali chimene chimatchedwa “mpingo,” kumene anthu anasonkhana. Chinthu choyamba, iwo asanabwere mkati, osonkhana, kuti alowe mmenemo, iwo ankayenera kubwera pansa pa magari okhetsedwa, mabwalo akunja. Poyamba iwo ankabwera ku madzi a kulekanitsa, kumene ng’ombe yamphongo yofiira inkaphedwa ndi kupanga madzi a kulekanitsa. Ameneyo ndi wochimwa amene amabwera ndi kudzamvetsera pa Mawu.

²¹¹ Umo ndi momwe rabbi wamkulu wa Chiyuda uyu anangobweretsedwa kumene kwa Ambuye, munandimva ine ndikulalikirira pa zimenezo kumusi uko . . . ku Tulsa. Ku Tulsa, uko kunali. Ife tinali kumeneko ku Tulsa, Oklahoma. Ndipo iye anabwera kumeneko, wongowonerera. Ndipo iye anapita pambuyo pa utumiki, iye anati, “Ine ndikudziwa!” Anati . . . Iye ndi mmodzi mwa ma rabbi seveni odziwika bwino padziko lapansi. Ndipo iye anabwera kumeneko, anati, “Ine ndikufuna kuti ndiwone zomwe Amuna Amalonda Achikhristu awo . . . Iwo amawatcha iwo, ‘Apentekoste.’ Ine ndikufuna kuti ndipite kumeneko, ndikakhale pansa, nkumvetsera.”

²¹² Ndipo pamene Ambuye anandiuza ine kuti ndiyankhule pa nsembe ya ng’ombe yofiira ija, utatha utumiki iye anakumana ndi ena a abale kumbuyo uko, anati, “Ine ndikufuna kuti ndikumane ndi mwamunayo. Ine ndikudziwa kuti iye alibe maphunziro nkomwe koma . . .” Anati, “Ndine rabbi Wachiyuda amene ndimadziwa kafikidwe kosiyanasiyana ako ndi zinthu monga choncho,” anati, “Ine sindinayambe ndaziwonapo izo mu moyo wanga wonse.” Anati, “Ine sindinayambe ndaziwonapo izo.”

²¹³ Ndipo tsopano iye ndi rabbi wa Chipentekoste, wodzazidwa

ndi Mzimu Woyera, akupita kulikonse, kulalikira Uthenga. “Rabbi wa Chipentekoste,” iye amadzitcha yekha. Iye anapita ku Washington Youree Hotel, tsiku lina pamene ife tinakumana limodzi kumusi kwa M’bale Jack, ndipo donayo anamudziwa iye, anati, “Rabbi,” iye anati, “ife tiri ndi chipinda chabwino cha inu, koma” anati, “ife tiribe televizioni mmenemo.”

²¹⁴ Iye anati, “Zinthu zimenezo ziri ‘hellevizion,’ zitayireni kunja! Sindikuzifuna izo mmenemo, mulimonse; ziri mmenemo, ine ndingakupangitseni kuzitayira kunja.”

Iye anati, “Rabbi!”

Iye anati, “Ndine rabbi wa Chipentekoste.” Aleluya!

²¹⁵ Anati, “Tsopano, pamene inu mupita ku Israeli, M’bale Branham, ine ndikufuna kuti ndidzapite nanu.” Anati, “Ife tikhoza kuzitengera izo kwa anthu athu.”

²¹⁶ Ine ndinati, “Osati tsopano, Rabbi, osati tsopano. Osati tsopano, ora lake silinafikebe, dikirani pang’ono pokha.”

²¹⁷ Tsopano, zindikirani malo oyera awa. Tsopano, pamene inu mubwera m’mabwalo amilandu, oyamba anali mabwalo, mabwalo akunja. Chotsatira chinali guwa, kumene nsembe zinkaperekedwa, guwa lamkuwa. Ndiye kunja kwa guwa lamkuwa, kunali chophimba apa chomwe chinkapita mu malo Oyeretsetsa; mmenemo munali mpando wachifundo, mmenemo munali Akerubi. Ndicho chimene ine ndikufuna kuti ndifikeko mu phunziro lathu lotsatira, Akerubi amenewo akuphimba mpando wachifundo. Oh, mai! Ine... Ife tikhoza kungokhala mwezi wonse pa zimenezo, mwaona, pa Akerubi amenewo.

²¹⁸ Tsopano, tsopano zindikirani pamene iwo ankalowa mmenemo. Osonkhana ankakhoza kubwera *kumeneko*; ansembe ankakhoza kuyima *apa*; koma wansembe wamkulu yekha amakhoza kulowa *mmenemo*, kamodzi pa chaka, atatenga magazi limodzi naye.

²¹⁹ Ndipo iye ankayenera kuti avekedwe mwanjira inayake, chovala chinachake; ankayenera kukhala ndi belu ndi makangaza, wina kwa mzake. Ndipo pamene iye ankayenda, iye ankayenera kuyenda mwanjira inayake. Pamene iye ankayenda ankayimba, “Woyera, woyera, woyera, kwa Ambuye. Woyera, woyera, woyera, kwa Ambuye” mabelu amenewo ndi makangaza akulira pamodzi, “Woyera, woyera, woyera!” Chifukwa chiyani? Iye anali kuyandikira kwa Mulungu, ali nawo magazi a pangano mu dzanja lake, akupita patsogolo Pake, atanyamula magazi.

²²⁰ Atadzedwa (Oh, mai!) ndi zonunkhiritisa zina. Zovala zake zinkayenera kupangidwa ndi dzanja lodzazidwa ndi Mzimu Woyera, manja olembetsedwa amapanga zovala zake. Rozi la Sharoni, mafuta odzozera, atatsanulidwira pamutu pake, iwo amayenderera mpaka ku ndevu zake zonse ndiyeno mmusi pa malo ake ndi zonunkhiritisa zachifumu; mkangaza ndi

belu; atatenga magari a mwanawankhosa wosalakwa; ndipo iye sangayerekeze kuyandikira chophimba chimenecho kunja, iye akhoza kufera pomwepo, pamene iye ankayima. Kotero iye ankayenera kupita, akuyenda mwanjira inayake, “Woyera, woyera, woyera, kwa Ambuye. Woyera, woyera, woyera,” (akuyandikira kwa Mulungu) “kwa Ambuye. Woyera, woyera, woyera!”

²²¹ Ndipo iye ankapita kumeneko ndipo anakapereka magari pa mpando wachifundo, kamodzi pa chaka. Ndipo pamene iye anali mmenemo, iye anali ndi mwayi kuwona Ulemerero wa Shekinah; pamene Lawi la Moto, Kuwala kwa ambara komwe kunkatsika, komwe kunkawatsogolera ana kutuluka mu Israeli. Iye ankafukiza ngakhale kachisiyo kuti pasakhale wina yemwe angaliwone Ilo. Ulemerero wa Ambuye unkagwa mpakaponse panali pamafukizidwa. Ndipo Iye anadza Iyemwini, napita kuseri kwa chophimba ndipo anakakhala pansi pa mpando wachifundo mu Malo Oyeretsetsa a oyera. “Malo Oyera Kwambiri,” iwo amatchedwa, Oyeretsetsa a oyera. Ndipo iye ankayenera kuti avekedwe mwanjira inayake, kuyenda mwanjira inayake, kudzozedwa mwanjira inayake. Iye anali munthu wapadera kuti azilowa mmenemo. Momwe mpingo uyenera kuti unkamuchitira iye nsanje!

²²² Koma pamene Yesu anafa, chophimba cha m’kachisi chinang’ambika. Osati wansembe wamkulu yekha, koma “iye amene afuna” akhoza kukhala nako kudzoza komweko kwa Ulemerero wa Shekina ndi kuyenda moyo woyera, “Woyera, woyera, woyera, kwa Ambuye,” ndi kuyandikira mu Kukhalapo komwe kwa Mulungu, kudzera mu Magazi a Yesu Khristu patsogolo pake. Mutengeni iye ndi: “Ambuye Yesu, apa pagona munthu wodwala, iye ndi m’bale wanga. Iye ali pa kama waimfa pakali pano, kuti afe. Ine ndikukuyandikirani Inu, ‘Woyera, woyera, woyera, kwa Ambuye.’”

“Zachiyani?”

“Monga wansembe wamkulu.”

“Zachiyani?”

“M’ malo mwa m’bale wanga. ‘Woyera, woyera, woyera, kwa Ambuye.’”

²²³ Ndi zimenezotu! Kuyenda kwanu kwa tsiku ndi tsiku, zoyankhula zanu za tsiku ndi tsiku, makhaliidwe anu a tsiku ndi tsiku, mtima wanu, moyo wanu, ndi zonse, “Woyera, woyera, woyera, kwa Ambuye.” Popanda mizu yowawa, popanda china chirichonse, “Woyera, woyera, woyera, kwa Ambuye. Woyera, woyera, woyera, kwa Ambuye,” pamene ife tikuyamba kuyandikira m’ malo mwa m’bale wathu. Aliyense amene afuna abwere, wodzozedwa, Magazi patsogolo pake, Magazi akupita patsogolo pake, akuyimba “Woyera, woyera, woyera, kwa Ambuye.”

224 Tsopano, amenewo anali mabwalo akunja, malo opatulika. Ndipo Oyeretsetsa a oyera, amenewo anali malo opatulika a Mulungu pa dziko lapansi. Penyani, ilo linayimiridwa ndi la Kumwamba. Tsopano, ife tibwereranso ku Lemba lomweli. Oh, tonse pamene tikudutsa mu Chibvumbulutso, ife tikhoza kubwera molunjika kumene kubwerera ku izi kachiwiri. Mukuona?

225 Tsopano iye. . . Yohane, Yohane wayima kuti? Ku mabwalo. Tiyeni tingowerenga patsogolo pang'ono apa kuti inu mumvetse chithunzicho:

Ndipo kuchokera ku mpandowachifumuwo munatuluka mphezi. . . mabingu. . . maliwu: ndipo panali nyali seveni za moto (Dikirani mpaka ife itafika ku zimenezo!) zikuyaka kutsogolo kwa mpandowachifumu, imene ili Mizimu seveni ya Mulungu.

226 Ikunyezimiritsa Kuwala kwa Mulungu mu Mpingo, molunjika kumene kuchokera ku Mpandowachifumu wa Mulungu, osati kudzera mu seminare, osati kudzera mwa bishopu wina, koma kuchokera ku Mpandowachifumu wa Mulungu, mwa vumbulutso la mphamvu ya chiwukitsiro Chake, kumupanga Iye kukhala yemweyo dzulo ndi nthawizonse; nyenyezi seveni zimenezo zitayima pamenepo zikunyezimiritsa Kuwala kumeneko, Kuwala kwa Shekina, kuchokera ku Ulemelero wa Shekina wochokera ku Oyeretsetsa a oyera. Nyali seveni zoyaka moto, zokhala pamwamba pa zoyikapo nyali izi, zikunyezimiritsa Kuwala Kwake, mitundu Yake, ya mphamvu Yake ya chiwukitsiro Chake, kulowa mpaka mu Mpingo. Amenii! Hmm!

Ndipo patsogolo pa mpandowachifumu. . . panali nyanja yamandala yofanana ndi mwala: ndipo pakati pa mpandowachifumu, ndi pozungulira mpandowachifumuwo, panali zamoyo zinayi zodzala ndi maso kutsogolo ndi kumbuyo.

227 Ndipo iye amapitirira ndipo iye amayamba kupereka izi. . . zamoyo izi, chinthu chomwecho Ezekieli anachiwona; alonda amenewo. . . wina ngati munthu, wina ngati mkango, ndi wina ngati mphungu. Chinali chiyani icho? Tsopano, penyani, pamene ife tikuwabweretsa iwo mkati ndi kuwasonyeza Mkango wa Fuko la Yuda umenewo ndi onse osiyanasiyana amenewo ochokera mu mafuko awo, amene anakhala pa makoma anayi, ndipo iwo anali kulondera mpando wachifundo uwu. Oh, ndi chithunzi chotani! Oh, ine basi. . . Pali masiku opambana patsogolo.

228 Monga ife tinawawona iwo, tsopano, umenewo unali Mpandowachifumu wa Mulungu Kumwamba, Mose anawufanizira Iwo pa dziko lapansi, unali Mpandowachifumu

wa Mulungu chifukwa mpando Wake wachiweruzo unayimiridwa pano pa dziko lapansi mu Malo oyeretsetsa. Mulungu . . . Israeli yense ankabwera ku malo amodzi amenewo kuti adzapeze chifundo, chifukwa Mulungu ankangokumana nawo pansa pa magazi okhetsedwa.

²²⁹ Tsopano, mvetserani mwacheru. Ndiye Ulemerero wa Shekina unawuka kuchokera ku mpando wachifundo umenewo tsiku lina, ndipo Iwo unakhazikika pa Kachisi wina (Ameni!), Umenewu, “Atate samaweruzo munthu aliyense koma Iye wapereka chiweruzo chonse kwa Mwana.” Mpando Wachiweruzo wa Mulungu. Fyuu! “Inu mukayankhula motsutsana ndi Ine, izo zidzakhululukidwa kwa inu,” mukayankhula china—Umodzi wina ukubwera, Mpando Wachifundo wina. “Kuyankhula . . . inu mukayankhula motsutsana ndi Mwana wa munthu, Ine ndidzakhululukirani inu; koma tsiku lina Mzimu Woyera udzabwera kudzakhala mu mitima ya anthu, mawu amodzi owutsutsa Iwo sadzakhululukidwa konse.”

²³⁰ Izo zimapirira kukhala zovuta kwambiri ndi zovuta kwambiri nthawi zonse, chiweruzo, chifukwa Mulungu mosalekeza akuvula chipiriro Chake, kuyesera kuti awatengere ochimwa kuti abwere kwa Iye kuti adzayanjanitsidwe. Poyamba, Iye anali m’miyamba kumwamba ndi kumawala kudzera mu nyenyezi. Kachiwiri, Iye anali pa dziko lapansi akuwala kudzera mu Ulemelero wa Shekina. Kotsatira, Iye anabwera ndipo anapangidwa thupi ndipo anadzakhala pakati pathu, akuvalabe chipiriro Chake. Ndiye Iye anamuwombola munthu ndi Magazi Ake, anabwera mu Mpingo Wake mwa mawonekedwe a Mzimu Woyera, ndipo kuyankhula motsutsana ndi Chimenecho ndi chinthu chotsirizidwa, kuthedwa.

²³¹ Tsopano inu mukhoza kuwona kumene kugwedezekako kunabwera. Kumene nthawiyo, iwo samazindikira. Anthu sangamvetse zomwe Izo zikutanthauza.

²³² Tsopano, Mpandowachifumu woyamba unali Kumwamba, mpando wachiweruzo. Mpandowachifumu wachiwiri unali mwa Khristu. Mpandowachifumu wachitatu uli mwa munthu.

²³³ Tsopano, ndiloleni ine nditenge chinthu chaching’ono ichi chimene ndachijambula apa. Ife tipanga . . . Ine ndikanakonda ndikanakhala ndi bolodi, kuti ndizipange izo kuti mwinamwake zimveke bwino kwambiri kwa inu. Ife titenga ndi kujambula mabwalo, kungopanga izo mu chozungulira, kapena monga chonchi, limodzi lililonse. Tsopano ife titenga . . . Ine ndikukhulupirira, monga *izi* mwinamwake zingakhale zabwino kwambiri, ife titenga ndi kupanga mabwalowo.

²³⁴ Tsopano, munthu ndi chiyani? Iye ndi munthu wa patatu; thupi, solo, ndi mzimu. Ndi angati akudziwa zimenezo? Penyani mafikidwe a Mulungu. Kodi mtima wake ndi chiyani? Inu

mukukumbukira uthenga wanga, *Mulungu Anasankha Mtima wa Munthu Kukhala Nsanja Yake Yolamulira?* Mdierekezi anasankha mutu wake kukhala nsanja yake yolamulira; mwawona, iye amamupangitsa iye kuwona zinthu, kuyang'ana kudzera m'maso ake. Koma mmenemo. . . Mulungu mu mtima mwake amamupangitsa iye kukhulupirira zinthu zomwe iye sangakhoze kuziwona. Iye Anatero? Mwaona, Mulungu ali pa mtima wake, mu mtima wa munthu muli Mpandowachifumu wa Mulungu. Inu mukumvetsa zimenezo? Munthu! Mulungu anapanga Mpando Wake Wachifumu mu mtima wa munthu.

²³⁵ Tsopano, penyani. Kodi gawo loyamba la munthu ndi chiyani? Gawo loyamba la munthu ndi *thupi*. Gawo lotsatira ndi *solo* yake, imene ili chikhalidwe cha mzimu wake umene umamupanga iye chimene ali. Iye akufika tsopano. Tsopano, gawo lachitatu la munthu ndi *mzimu* wake, ndipo mzimu wake uli pakati pa mtima wake, ndipo pakatikati pa mtima ndi pamene Mulungu amabwera ngati Mpandowachifumu.

²³⁶ Inu mukukumbukira, posachedwapa, a—mapepala anapereka mu Chicago pafupifupi zaka zinayi zapitazo, pamene wokhulupirira wakale. . . wosakhulupirira wakale, kani, anakonda kunena kuti Mulungu analakwitsa kudzera mwa Solomoni pamene Iye anati, “Monga munthu amaganizira muntima mwake.” Anati, “Mulibe mphamvu zamaganizo mu mtima zoganizira nazo. Kodi iye akanaganiza bwanji ndi mtima wake? Iye akuyenera kutero. . . Iye ankanthauza mutu wake.”

²³⁷ Ngati Mulungu akananthauza mutu wake, Iye akanati, “mutu wake.”

²³⁸ Monga Mose, bwanji ngati Mose. . . Mulungu akanati, “Mose, vula nsapato zako, uli pa malo Oyera”; iye nkuti, “Chabwino, bwanji ine ndingovula chipewa changa, ndizo zabwino basi”? Iye anati, “nsapato.” Iye sanati, “chipewa,” iye anati, “nsapato.”

²³⁹ Ndipo pamene Iye anati, “Lapani, ndipo batizidwani mu Dzina la Yesu Khristu,” Iye sankanthauza “Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera.” Iye ankananthauza basi zomwe Iye ananena.

²⁴⁰ Pamene Iye anati, “Inu *muyenera* kubadwanso mwatsopano,” Iye sanati, “Inu *muyenera* kukhala.”

²⁴¹ Iye anati, “Zizindikiro izi *zidzawatsata* iwo akukhulupirira,” Iye sananene kuti, “*Mwina* izo zidzatero.”

²⁴² Iye amanena zomwe Iye akutanthauza! Ndipo Iye ndi Mulungu ndipo Iye sangathe kuzibwezanso Izo. Iye amadziwa chimene chiri changwiro koteru Iye amachipanga Icho mwanjira imeneyo, ndipo umo ndi momwe Iye—Iye akulinga kuti Izo zikhalire. Ndipo inu mumayenera kukwera kukafika ku Chimenecho. Osati Iye kutsika pansu ku lingaliro lanu, inu mukuyenera kubwera ku Lingaliro Lake. Ndiko kusiyana kwake.

²⁴³ Tsopano, tsopano, pa kachitidwe aka ka thupi, solo... Tsopano, ngati inu mutenga mawu akuti *solo* ndi kuwayang'ana iwo, iwo adzakuwuzani inu mu—mu dikishonale ya Baibulo kapena Webster, chirichonse cha izo, ndi “chikhalidwe cha mzimu.”

²⁴⁴ Tsopano, pano pali mwamuna, ife timati, *apa pali* John Doe. Chabwino, John Doe. Ndipo *apa pali* Sam Doe. Chabwino. Tsopano, John Doe ndi mwamuna, thupi, iye ndi m'bale wake wa Sam Doe. Tsopano, John ndi mzimu, solo, thupi; ndipo Sam Doe ali chinthu chomwecho (thupi, moyo, mzimu) monga iye aliri, thupi, moyo, mzimu. Tsopano, munthu *uyu* ndi woyipa, wankhanza, wachinyengo, amaba, amanama, amachita chigololo, chinthu choyipa chirichonse chimene iye angakhoze kuchichita; koma munthu *uyu* ndi wodzala ndi chikondi, mtendere, chimwemwe. Iwo onse ali ndi solo, thupi, ndi mzimu. Chabwino, pali kusiñana kotani? Munthu *uyu* akhoza kubwerera m'mbuyo ndi kunena, “Ine ndikukumbukira amayi anga, Ine ndikukumbukira zinthu zimene ife tinkachita tiri anyamata”; onse awiri angathe. Iwo onse ali ndi mizimu, iwo onse ali ndi ma solo, iwo onse ali ndi thupi.

²⁴⁵ Koma chikhalidwe cha mzimu wa munthu *uyu* ndi choyipa; chikhalidwe cha mzimu wa munthu *uyu* ndi chabwino. Mukuona? Kotero chikhalidwe cha mzimu ndi solo ya munthu. Mukuona? Kotero, tsopano, Mulungu akuyesera kuti alowe mu chiyani? Mzimu ndi mtima wa munthu. Pomwe mzimu uli ndi mu mtima.

²⁴⁶ Inu mukudziwa, ndipo sayansi inanena (monga ine sindinamalizitse izo), kuti munthu sangaganize ndi mtima wake. Ndipo sayansi ikuyamba kuzindikira kuti mu mtima wa munthu muli kagawo kakang'ono (osati mu mtima wa nyama, koma mu mtima wa munthu), mulibe ngakhale khungu la magari, kapena kalikonse. Iwo anati, “Iwo ayenera kukhala malo amene solo imakhalapo, kapena mzimu.” Ingololani—ingowasiyani iwo okha, iwo amatenga zinthu zawo zopusa ndi kumamutsimikizira Mulungu. Uko nkulondola. Mulungu amangowapangitsa opusa kuti achitire umboni za Iye.

²⁴⁷ Tsopano, ndi izo pamene, mitu yayikulu mu pepala. Mtsikana wamng'ono wa M'bale Boze anati, “M'bale Branham, inu mukudziwa zomwe inu mumanena tsiku lina?” Anati, “Tayang'anani, penyani, sayansi yazipeza kale.”

²⁴⁸ Ndinati, “Chabwino, adalitsike Mulungu! Ine ndikufuna zimenezo, mlongo, ine ndikufuna—ine ndikufuna zimenezo.”

²⁴⁹ Solo ya munthu ndi chikhalidwe cha mzimu, ndipo mzimu umakhala mu mtima wa munthu.

²⁵⁰ Tsopano, tsopano, mabwalo akunja ndi chiyani? Ndiwo thupi. Mukuona? Ndicho chinthu choyamba chimene inu mumabwerako, thupi. Inu mukuyenera muthane nalo ilo

poyamba. Inu mukuyenera, kudutsa kupyola thupi. “Ine—ine sindikumverera ngati ndidzuke ndi kupita kutchalitchi, misewu ndi yoterera kwambiri. Ine—ine... Kwatentha kwambiri. Oh, tchalitchi, ine sindikudziwa.” Limenero ndi thupi. Chabwino. Tsopano, inu mukuyenera kuthana ndi kuyenda kudutsa limenero, Mulungu akuyenera kudutsa pa limenero.

²⁵¹ Nthawi yotsatira Iye abwera, Iye akuyenera kubwera mu solo, ndicho chikhalidwecho. “Oh, kodi a Jones ati chiyani za ine? Oh, mai! Inu mukudziwa, mpingo wanga udzandithamangitsa ine ngati ine—ngati ine ndichita chinachake chonga icho. Mukuona?” Koma inu mukuyenera kudutsa pamenepe.

²⁵² Ndipo pamene inu muyenda kudutsa ilo, ndiye Iye amapita mu mtima ndipo kumeneko ndi kumene Iye amakhala. Uwo ndi Mzimu Woyera mwa inu. Yesu anati, “Zingakhale bwino kuti mwala wamphero upachikidwe pakhosi pako ndipo inu nkukamizidwa pa kuya kwa nyanja, koposa kukhumudwitsa m’modzi wa aang’ono awa amene akukhulupirira mwa Ine.” Musawachitire iwo choyipa chirichonse; basi ngakhale kubweretsa chokhumudwitsa kwa iwo, kungowakhumudwitsa iwo pa chinachake. Zikanakhala bwino kuti inu mukanamizidwa, kapena mukanapanda kubadwa padziko lapansi, kuposa ngakhale kukhumudwitsa munthu mmodzi. Kodi Iye ankatanthauza izo? Kodi Iye akanakhoza kunama? Kodi atumwi ananena zimenezo? Ayi, ayi. Yesu ananena Izo! Yesu anati, “Ngati inu mungabweretse chokhumudwitsa kwa mmodzi wa iwo, aang’ono awa amene akukhulupirira mwa Ine.”

“Zizindikiro izi zidzawatsata iwo amene akhulupirira!”

²⁵³ Munthu wina wopambana, wamkulu anati, “Oh, ine ndimakhulupirira mwa Iye! Aleluya!”

²⁵⁴ “Kodi inu munayamba mwayankhulapo ndi malirime, kutanthauzira malirime, kutulutsa ziwanda, masomphenya, ndi zina zotero, monga Iye analonjezera?”

“Ayi, tsiku limenero linapita.” Iye si wokhulupirira, iye ndi wodzipangitsa kukhulupirira.

²⁵⁵ Yesu anati, mawu otsiriza amene Iye ananena, “Zizindikiro izi zidzawatsata iwo amene akukhulupirira, ku dziko lonse lapansi ndi ku cholengedwa chirichonse.” Uko nkulondola. “Izo zidzamutsata wokhulupirira mpaka ine ndidzabwerere.” Ndiwo Mawu otsiriza amene Iye ananena. Ndi angati akudziwa zimenezo? Baibulo, Marko 16.

Tsopano, taonani, iye ndi wodzipangitsa kukhulupirira.

²⁵⁶ Koma mukampeza wokhulupirira amene amakhulupirira kwenikweni, ali ndi zizindikiro zikumutsatira, ndipo mumaona kudzichepetsa kwa moyo wawo, osati wotsanzira, amadziwa kuti iwo ndi Akhristu, enieni, chipangizo chenicheni,

ingokhazikikani. Chinthu chimene inu mukuyenera kuchita, ndicho kujowinana nawo iwo, kuyamba kusuntha motsatira, chifukwa inu mukuyenda mumsewu waukulu wa Mfumu.

257 Tsopano, chimachitika ndi chiyani? Penyani izi. Mabwalo akunja: unali m'badwo wa Luther, pamene ife tikuyamba mu Thupi la Mpingo wa Amitundu.

258 Inu mukukumbukira, iwo anali Achiyuda mpaka pafupifupi nthawi ya—ya A.D. 606 pamene iwo unafika mu Tiyatira, pafupifupi onse anali otembenuka mtima Achiyuda. Koma atatha Achiyuda, izo zinagwera mkati umu kwa onse Ayuda ndi Amitundu (koma makamaka Achiyuda). Koma pamene zinafika kwenikweni mu m'badwo wa Amitundu, anabwera mbali iyi, mwaona, kunabwera Martin Luther, John Wesley, ndi ena otero. Mukuona?

259 Tsopano, penyani atatu otsiriza awa utatha M'badwo wa Mdimba uwo, akubwera mpaka ku M'badwo Wapakati ndi kudutsa. Zikafika, taonani mabwalo akunja awa. Mukuona: thupi, solo, mzimu. Mwaona? Mabwalo akunja amenewo, thupi. Malo oyera: Anazarene, Pilgrim Holiness, Free Methodist. Mukuona? Ndipo kenako Oyeretsetsa a oyera: kubwerera mu Chipentekoste, kumene iwo unayambira pachiyambi, mwaona, kubwerera ku chiyambi.

260 Tsopano, ngati inu mukuzijambula izo, ine ndikufuna kuzilemba. Tsopano, pali zipata faivi zomwe zimapita mu thupi, zomwe zimalamulira thupi. Inu mukudziwa zimenezo. Kodi palibepo? Ndizo zokhudzira faivi. Ndi zokhudzira zingati zomwe zimalamulira thupi? Faivi: kuwona, kulawa, kukhudza, kununkhiza, kumva. Ndi kulondola uko? Ndilo thupi, mabwalo akunja, ndizo zinthu zomwe inu simungazidalire chifukwa ndi zathupi.

261 Mabwalo amkati ndiye, ife tiri ndi mabwalo amkati, lomwe liri guwa lotsatira. Ndipo guwa lotsatira limalowamo, ndipo ilo limalowamo ndi—ndi chikumbumtima, malingaliro, zikumbutso, zilakolako, ndi zokonda. Ndizo zokhudzira faivi zomwe zimalamulira mabwalo amkati. Ndiyo solo. Zokhudzira za zachikondi, ndiyo solo, chikondi, ndi zina zotero. Ndiyeno chotsatira mu chokhudzira ichi umu, mumakhalanso zikumbutso, ndi chikumbumtima, ndi chifundo, ndi zina zotero, ndi—ndi—ndi malingaliro. Inu mumakhala pansu ndi kumalingalira zinthu, inu mukuchita chiyani? Inu simumachita izo mu thupi lanu, zokhudzira zanu sizimalingalira. Ndi bwalo lamkati mkati mwanu.

262 Ilo liri ndi zipata zitanu. Kodi ife tikuchita chiyani? Ife tikuziphwanya tsopano, musaziphonye Izi. Kuchokera ku thupi, zokhudzira zisanu; kupita ku chotsatira, solo, mabwalo amkati; koma tsopano inu mwalowa mu mtima. Mukuona?

263 Tsopano, apo ndi pamene inu a Pilgrim Holiness abwino ndi Amethodisti munakhala pa guwa limenero kunjira *uko*. Mwaona, inu muli m'mabwalo. Inu Achilutera ndi ena otero m'mbuyo mu thupi, kumbuyo uko ndi zokhudzira zisanu, zomwe diso lingakhoze kuziwona ndi kuzipanga. Mukuona?

264 Apa panabwera a Pilgrim Holiness amene anali chabe a Free Methodist, kubwera ku mabwalo otsatirawa ndi kukhulupirira mu chiyero, chifukwa iwo ankatchedwa malo oyera kumene nsembe inkayikidwa.

265 Koma kamodzi pa chaka mkulu wa ansembe ankapita ku Malo oyeretsetsa amene anatsutsidwa. Uko kunali m'badwo wa Chilutera; kenako m'badwo wa Methodisti; kenako m'badwo *uno*, kuwala kwa Mpingo kukubwera, zomwe ziri monga mu kachitidwe ka munthu.

266 Ndiye bwanji—ife timalowa bwanji *umu*? Tsopano, kumbukirani, panali chophimba, chophimba chimene chapachikidwa pakati pa oyera ndi Malo oyeretsetsa. Mu Malo oyeretsetsa ndi kumene Khristu amabwera kudzakhala pa mpandowachifumu wa mtima wanu, Khristu amapatsidwa ulamuliro. Iye amabwera kudzera mu kulungamitsidwa (Ndi kulondola uko?); kuyeretsedwa; “Ndipo kenako mwa umodzi...” (madzi...mwa mpingo umodzi...mwa chikhulupiriro chimodzi...Ayi!) “mwa Mzimu umodzi,” kuchokera pano ife tonse timabatizidwa kulowa mu Thupi limodzi lomwe liri Thupi la Khristu. Ndi chiyani? Mzimu Woyera.

267 Ndani amalowamo? Amethodisti, Abaptisti, Apresbateria, Achipentekoste, aliyense amene angafune. Chophimba chimenecho, inu mukudziwa chomwe chophimba chimenecho chiri chimene chimaphimba mtima wanu kwa Icho? Mwakonzeka? Chophimbacho chimatchedwa “chifuniro chawekha.” Kodi inu mwachipeza chithunzicho tsopano? Zokhudzira kunjira *uko*, zokhudzira pa thupi ndi zokhudzira ku solo, ndipo chophimba pakati pa izo ndi malo oyera, Malo oyeretsetsa. Ndipo njira yokhayo yomwe inu mungalowere mmenemo ndi kukhala ndi chifuniro chawekha! “Kwa aliyense...” Chiyani? Aliyense amene agwirana chanza? Aliyense amene amizidwa? Aliyense amene ajowina mpingo? Aliyense amene apereka kalata yake? Aliyense amene amachita...? Ayi! “Aliyense amene *afuna* abwere kudutsa chophimbacho.”

268 Lolani Khristu abwere ku zokhudzira; kunena “Chabwino, ine ndiyenera kutero. ine sindikufuna kuti ndipite ku gehena, ndicho chinthu chimodzi. Ine ndidzajowina mpingo.” Chabwino, Achilutera.

269 “Chabwino, ine ndikuwuzani inu chiyani, ine ndikukhulupirira kuti ine ndiyenera kukhala moyo wosiyana,

zomwe ine ndingathe,” kuyeretsedwa pa guwa. Chabwino, Amethodisti.

²⁷⁰ Chabwino, ndiyeno aliyense amene *afuna*, muloleni iye adutse chophimba chong’ambikacho. Oh, ulemerero ukhale kwa Mulungu! Ine ndiri mbali inayo. Aleluya kwa Dzina Lake! Oh, mai! Aliyense amene afuna, muloleni iye aching’ambe icho, makatani a chifuniro chake chomwe, ndipo mulole Mulungu abwere mu mtima mwake. Pali Khristu pa mpando Wake wachiweruzo mu mtima wa munthu! Kodi choti chichitike nchiyani?

²⁷¹ Inu mukuti, “Ine ndiyenera kutero . . . Oh, ine—ine ndikhoza kunena nthabwala zonyansa, izo sizimanditsutsa ine.” Chifukwa chiyani? Iwo alibe Ichu chimene chingawatsutse. Palibe Amene ali pamenepo kuti—kuti achichotse icho. Palibe Amene alipo kuti—kuti akutsutseni inu. “Chabwino, ine ndikuwuzani inu,” akazi anati, “Ine ndikhoza kukhala ndi tsitsi lalifupi, izo sizimanditsutsa ine.” Nzosadabwitsa! Mwaona? “Oh, ine ndikhoza kuvala zazifupi . . . Ine ndikhoza kuchita *izi*. Ine . . .” Amunawo anati, “Izo sizimandipweteka ine kusuta ndudu, ndipo izo sizimandipweteka ine kusewera ena—makhadi ena ndi kuponya madayisi,” ndi chirichonse chimene iwo amachita. “Izo sizimandipweteka ine.” Ndipo iwo akadali a mpingo, mwaona, “Sizimandipweteka ine kuchita *izi*.” Chifukwa chiyani? Chifukwa chiyani? Palibe chirichonse pamenepo choti chikuweruzeni inu.

²⁷² Koma Khristu akalowa mkati, inu mwapanga guwa pa mtima panu ndipo machimo anu amachotsedwa tsiku ndi tsiku. Paulo Woyera wamkulu, iye anati, “Ine ndimafa tsiku ndi tsiku. Komabe ine ndiri ndi moyo, koma si *ine* ndikukhala moyo, Khristu akukhala moyo mwa ine.” Pamenepo pali chophimba chamkati. Oh, m’bale, mlongo!

²⁷³ Fulumirani, ine ndikudziwa . . . Oh, ayi, ndine . . . Ine basi sindingathe kuzimaliza izo, ine ndadutsa nthawiyo. Tiyeni tione, ndiloleni ine basi . . . Ayi, kulibwino ndisatero. Mwaona, ine ndikufuna kuti nditenge akulu twente foro, ndipo ine ndikudziwa ine ndikukuchedwetsani inu nonse ku chakudya chanu chamadzulo. Ife basi . . . Tiyeni tione, izo . . . Ndi angati akuti tengani akulu twente foro? Basi . . . [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi.] Chabwino, miniti yokha. Chabwino, miniti yokha. “Akulu twente foro,” ndiye, tiyeni tiwatenge iwo mwachangu tsopano, “kuzungulira Mpandowachifumu, ndipo panali twente- . . . kuzungulira Mpandowachifumu.”

²⁷⁴ Tsopano inu mukuwona chiyani . . . Kodi Mpandowachifumu uli kuti tsopano? Mu mtima. Mu mtima mwa ndani? Mamembala a Mibadwo Seven ya Mpingo, Khristu! “Kuyankhula mawu motsutsa zochita zawo, ndinu wotsutsidwa,” inu mudzayankhira

ku zimenezo pa Tsiku la Chiweruzo. Ndipo ndani adzaweruzza dziko lapansi? Oyeramtima adzaweruzza dziko lapansi.

²⁷⁵ Kodi Danieli anaona ndani akubwera ndi ma teni a masauzande kuchulukitsa ma teni sauzande? Oyera. Mabuku anatsegulidwa, ochimwa. Bukhu lina linatsegulidwa, lomwe linali Bukhu la Moyo, namwali wogona. Oh, mai, kodi iwo sangakhoze kuziwona izo? Mpingo wogona, iwo amene anapita kuti akakumane ndi Mkwati, iwo analola Mafuta athe mu nyali zawo; sanalowe mu Izi, sanamulole konse Khristu kutenga ulamuliro kuti Iye akhoze kuchita zozizwitsa ndi kuyankhula ndi malirime ndi kuchita zodabwitsa ndi zinthu kuti zitsimikizire kuti Iye ankakhala mu Mpingo Wake.

²⁷⁶ Bwanji ngati Yesu akanabwera pa dziko lapansi ndi kunena “Ndine Yesu, Ndine Mwana wa Mulungu,” sanachite kalikonse, Iye akanangoti “Ine—Ine ndikupita uku ndi kukajowina mpingo”? Kodi ameneyo akanakhala Mwana wa Mulungu?

²⁷⁷ Kodi Iye ananena chiyani? “Ngati Ine sindichita ntchito za Atate Anga, ndiye musandikhulupirire Ine.”

²⁷⁸ Oh, mai! Kodi inu mukuona? Mulungu amadzifotokoza Yekha, Iye amakonda kutero. Iye ndi Yehova. Iye amakonda kudzidziwitsa Yekha. Oh, ndine wokondwa kwambiri nazo izo. Inde, bwana. Iye wadzidziwitsa Yekha kwa ine, ine ndikudziwa Iye wawero kwa inu. Ena a inu anthu achichepere mwangotembenuka kumene, komabe inu simutero...mwina simungamudziwe Iye mu mphamvu ndi zinthu zazikulu zimene Akhristu akale amachita, koma inu mukubwera kumene mu izo. Inu mukubwera kumene mumsewu waukulu wa Mfumu. Musatero...Muzingopitirirabe kuyang’ana ndi kukangamira molimba momwe inu mungathere. Thamangani, thamangani, thamangani molimba basi momwe inu mungathere. Musayime pachabe, muzingopitirirabe kumapita.

²⁷⁹ Monga wosauka wakale Mlongo Snelling anakonda kunena:

Ndikuthamanga, kuthamanga, kuthamanga,
ndangodutsa kumene;
Kuthamanga, kuthamanga, kuthamanga, ine
ndangodutsa kumene;
Kuthamanga, kuthamanga, kuthamanga,
ndipo inu simungathe kukhala pansu.

Moyo wokalamba wosauka, iye ali kumeneko lero.

²⁸⁰ Chabwino, tsopano, ndipo panali—panali mipando yachifumu ndipo pali, panali twen-...panali mipando foro ndi twente. Tsopano, ndi angati amene iwo angakhale, foro ndi twente? Twente foro. Chabwino:

...mipando foro ndi twente: ndipo pa mpandopo...
pa mipandopo ndinaona akulu foro ndi twente...

(mmodzi pa mpando), *wovekedwa* ndi *zovala zoyera*;
ndipo iwo anali nawo pa mitu pawo akorona agolide.

²⁸¹ Tsopano, “akulu twente ndi forowo.” Ine ndikufuna kuti inu muzindikire kuti iwo sanali Matupi a Angelo. Angelo samakhudzana, Matupi a Kumwamba samakhudzana ndi akorona ndi mipando yachifumu. Mwaona, iwo sizimawakhudza konse, iwo ndi Angelo, iwo sanagonjetse konse. Ngati inu mungazindikire kanthawi kena, nyimbo zomwe iwo ankayimba, ndi zinthu, zinatsimikizira kuti iwo sanali. Mwaona? Iwo ankayimba nyimbo ya chiwombolo; kotero, Angelo samasowa kuti awomboledwe. Mwaona? Chabwino. Koma iwo anali anthu owomboledwa.

²⁸² Sindine...anthu inu, ine sindikhala ndi nthawi yoti ndizigwire izi. Koma inu amene mukulemba, ngati inu mukufuna kudziwa kuti iwo anali anthu owomboledwa, tengani Mateyu 19:28, chabwino, 19:28, Mateyu, Chivumbulutso 3:21, ndiye zitengeni iwo, Chivumbulutso 20:4, Chivumbulutso 2:10, Petro Woyamba 5:2 ndi 4, Timoteo Wachiwiri 4:8. Izo zikudziwitsani inu kuti iwo ndi owomboledwa. Ine ndikufuna kuti ndidutse mu zimenezo mmawa uno, inu mukuona. Ndipo inu mukhoza kungozitambasula izo kwa masabata, inu mukuona. Iwo sanali—iwo sanali Matupi a Angelo, iwo sanali Matupi a Akumwamba, iwo anali anthu owomboledwa. Mukuona? Inu mukhoza kuganizira kavalidwe kawo, mmene iwo anavalira; inu mukhoza kuganizira malo awo, amene iwo anali nawo; inu muganizire nyimbo, zomwe iwo ankayimba; ndipo mudziwa kuti iwo sanali Matupi a Angelo. Hmm.

²⁸³ Ine ndikudana nazo kuti ndibwere ku izi, koma tiyeni tiwerenge Lemba limodzi lina. Kodi mungatero? Chabwino. Tiyeni tibwerere ku Danieli 7, mphindi yokha, kumbuyo kuno, Danieli 7, ndipo tingowerenga Lemba apa. Ndikufuna... kotero izi zikuthandizani inu mochuluka kwambiri mu uthenga wonsewo mmawa uno. Ndikutsimikiza kuti zitero—izo zikupangitsani inu kumverera bwino kwambiri mukatha kuwerenga izi ndi kuona izi, onani chimene Danieli, mutu wa 7 wa Danieli, ndipo tiyeni tiyambire tsopano kuchokera pa... Danieli 7, tiyeni titenge wa 9 mu-... ndime ya 9. Tsopano, mvetserani mwatheru tsopano kwa zinthu izi:

Ndipo...Ine ndinaona mpaka mipando yachifumu inagwetsedwa pansu, ndipo Wamakedzanayo anakhalapo, zovala zake zinali zoyera ngati chipale, ndipo amene tsitsi la pamutu pake linali ngati... ubweya woyera: ndi mpandowachifumu wake unali ngati lawi lamoto, (Inu mukuona kachiwiri, kubwerera ku moto wa emerodi uja.) ndi magudumu ake ngati moto woyaka.

Ndipo...mtinge wamoto unatuluka ndi kubwera

kuchokera pamaso pake: masauzande kuchulukitsa masauzande anatumikira kwa iye, ndi ma teni a masauzande kuchulukitsa ka teni sauzande (Apo pakubwera Owomboledwa anu.) anayima pamaso pake: ndipo chiweruzo chinakhazikitsidwa, ndipo mabuku (mabuku, ambiri) anatsegulidwa.

²⁸⁴ Tsopano, zindikirani, chiweruzo ichi chinakhazikitsidwa. Mwaona? Tsopano penyani. Danieli, pamene iye anawona mipando yachifumu pa chiweruzo, iyo inali yopanda kanthu, iye anawona “mipando yachifumu itagwetsedwa pansi, anatsika kuchokera Kumwamba, Wakale wa nthawi anatsika kuchokera Kumwamba.” Koma pamene Yohane anaona izo, Mpandowachifumu unali kale utakhalidwa ndi Yesu, ndipo mipando yachifumu ya ophunzira ndi mbadwa, owomboledwa, inali itakwaniritsidwa kale. Mukuona? Danieli anaziwona izo zaka faivi handiredi isanafike nthawi ya Khristu. Ndiyeno pambuyo pa Khristu, zikupanga zaka twente faivi handiredi, ndipo Yohane anali kukhala moyo mu m’badwo umene uli nkudza, ndipo iye anali ataziwona zonsezi zikuchitika. Pamene, Danieli sanaziwone izo, (Mukuona?) iye anangowona Wamakedzanayo akubwera; iye anamuwona Iye akubwera. Koma pamene Yohane anamuwona Iye, Mpandowachifumu unali utakhalidwa, mwaona, mipando yachifumu inagwetsedwa pansi ndi Wamakedzanayo, ndipo Chiweruzo chinakhazikitsidwa. Koma pamene Yohane anamuwona Iye, akulu anali asanasankhidwebe mu nthawi ya Yohane...kapena nthawi ya Danieli, koma iwo anali atawomboledwa kale pa nthawi yotsiriza...?... Oh mai! Oh, si choncho... Kodi Iye si wodabwitsa?

²⁸⁵ Kotero, Danieli 7, iye... kodi Danieli anachita chiyani? Iye anawoneratu Chiweruzo, anawona mipando yachifumu inali yopanda kanthu. Mwaona, iyo imayenera kukhala yopanda kanthu. Monga Yohane mu nthawi yake, pambuyo pa Mpingo wokwatulidwa, iyo inali itakhalidwa ndi akulu owomboledwa. Hmm.

²⁸⁶ Kodi *mkulu* amatanthauza chiyani? Ngati inu mutenga mawu akuti *mkulu*, ine ndiri ndi pafupifupi... matanthauzo onse awa atalembedwa apa, ine ndikungozidumpha. *Mkulu* amatanthauza “mutu wa mzinda” kapena “mutu wa fuko.” *Mkulu*, “mutu wa chinachake.” Monga ine—ine ndingakhale a... M’bale Neville pakali pano ndi mkulu waku mpingo uno. Iye ndi chiyani? Iye ndiye mutu wa thupi la kuno. Mukuona? Ndipo meya wa mzindawu akhoza kukhala mkulu wa mzinda uno; mwaona, mkulu wa mzinda. Inu mukukumbukira m’mbuyo mu nthawi za Baibulo, akulu a mzinda? *Mkulu* amatanthauza “mutu wa mzinda” kapena “mutu wa fuko.”

²⁸⁷ Tsopano, anali angati iwo? Twente ndi foro, akulu twente foro. Ndi kulondola uko? Tsopano... Oh, mai! Anali ndani?

Atumwi thwelovu ndi mafuko thwelovu a Israeli, mbadwa thwelovu. A. . . Tsopano, ife tizitenga izo mopitirira mpaka ife titafika mu maphunziro ena, ndi kutsimikizira kuti izo ndi zolondola, kotero inu, ndine wokondwa kuti inu mukuzilemba izo tsopano. Mukuona? Mbadwa thwelovu ndi mafuko thwelovu a Israeli! Tsopano, penyani. Yesu ananena kuti. . .

²⁸⁸ Petro anafunsa tsiku lina, anati, “Kodi ife tidzalandira chiyani? Ife tasiya abambo, amayi, mwamuna, mkazi, ana, china chirichonse, ife tasiya chirichonse.” Petro anati, “Ife tasiya akazi athu, ife tasiya ana athu, ife tasiya abambo athu ndi amayi athu, nyumba zathu ndi minda yathu, kuti tikutsatireni Inu.”

²⁸⁹ Iye anati, “Indetu, indetu ndinena kwa inu, kuti mudzakhala pa mipando yachifumu thwelovu kuweruza mafuko thwelovu.” Ndizimenezotu, amenewo ndi owomboledwa, akulu owomboledwa.

²⁹⁰ Yang’anani—yang’anani pa Davide akuwonetsera Khristu. Mukuona? Pamene Davide ankabwera mu ulamuliro, chinthu choyamba, iye anali nayo nthawi yoyipa iye asanalowe mu ulamuliro. Komabe iye anali nako kudzoza pa iye, eya, kudzoza kunali pa iye. Ndipo anthu ambiri ankaganiza “Iye anali wopanduka pang’ono, mnyamata wamng’ono yemwe anali wosiyana, akuyesera kung’amba chinachake.” Koma panali amuna ena omwe ankadziwa kuti iye anali mfumu yakudzayo, iwo anakhala ndi iye kumene. M’bale, ine ndikutanthauza kuti inu simukanakhoza kuwachotsa iwo kwa iye, pamene iwo ankayendabe.

²⁹¹ Tsiku lina iye anayimirira pamwamba pa phiri, anayang’ana pansi ndipo anawona wake womwe waung’ono, mzinda wokonededwa utazingidwa ndi mdani. Ndipo iye anayima pamenepo ndipo anakumbukira pamene iye anali mnyamata wamng’ono, iye anakakonda kutengera nkhosa kudutsa kumeneko ndi kumwa madzi amenewo, awo anali madzi enieni. (Ife tinayankhulapo za zimenezo kuno osati kale kwambiri, *Madzi a Moyo*.) Ndipo apo iye ali, “Taganizani, ine ndinamwa kuchokera mmenemo.”

²⁹² Ndipo chokhumba chake chaching’ono chinali lamulo kwa munthu aliyense yemwe anali naye. M’bale, awiri mwa amuna amenewo anatenga malupanga awo ndipo anamenyana ndi Afilisti mamailosi fifitini, kuwasadza iwo kuchokera kumanja kupita kumanzere, kuti akamutengere iye madzi akumwa pa chitsime chimenecho. Iwo ankadziwa kuti iye akubwera mu ulamuliro. Inde, bwana. Nthawi ina, m’modzi wa iwo, kuti amupulumutse iye, analumphira m’dzenje ndi kupha mkango, ndi dzanja limodzi. Iwo anali ankhondo. Ndipo pamene—pamene iye anabwera mu ulamuliro, inu mukudziwa zomwe iye anachita? Iye anamupanga aliyense wa iwo kukhala wolamulira wa mzinda winawake.

293 Mukumuwona Khristu pamenepo? “Iye amene agonjetsa adzalamulira pa mzinda.” Ogonjetsa! Lero pamene ife tikuwona kuti Iye akubwera mu ulamuliro, Khristu adzalamulira dziko lapansi lino. Germany, ndi United States, ndi onse akuyenera kugwa, fuko lirilonse likuyenera kugwa. Maufumu a dziko lapansi asanduka maufumu a Mulungu wathu ndi a Kristu Wake, ndipo Iye adzalamulira ndi kulumulira pa iwo. Uko nkulondola.

294 Ife tikudziwa kuti Iye akubwera mu ulamuliro, kotero chokhumba Chake chaching’ono ndi lamulo kwa ife! “Iye akufuna ine kuti ndimuyimire Iye mu Timbuktu wamng’ono kumene kulibe ndalama zokwana masenti fifite, kumene kulibe kalikonse, kapena gulu losauka la anthu,” ndicho chokhumba. Amenii!

295 “Inu simumasowa kuti muzipeza zambiri, inu simukuyenera kuti muzichita *izi*, ingondidziwitsani kuti Iye akufuna kupita.” Amenii. Ndizo zonse.

296 “Ngati Iye akufuna kuti ine ndichite mosiyana, ndichite mosiyana,” monga alongo awa ndi zinthu, “ngati Iye akufuna kuti ine ndichite chinthu chinachake, Mulungu adalitsike, ndi mwayi kwa ine kuti ndichichite icho.” Ndi inu apo! Ife tikudziwa kuti Iye akubwera mu ulamuliro, ziribe kanthu zomwe dziko likunena. “Ngati ine ndikuyenera kutaya cholemetsa chirichonse ndipo machimo amangondisokoneza ine mophweka, ndiloleni ine ndithamange ndi chipiriro mpikisano umene wayikidwa patsogolo panga. Ndiloleni ine ndiyang’ane kwa Woyambitsa ndi Wotsirizitsa wa Chikhulupiriro chathu, Yesu Khristu.” Akubwera mu ulamuliro!

297 Kutu “akulu,” akulu twente ndi foro. Chabwino. Thwelovu... Uko mu Chibvumbulutso, ife tikupeza *izi*. Mu Bukhu la Chibvumbulutso, pa mutu wa 21, ife tikupeza kuti mzinda wa Yerusalemu unali ndi maziko thwelovu. Kulondola uko? Ndipo iye anali nazo zipata thwelovu, zomwe zinali zitatu mbali iliyonse, ma foro atatu ndi thwelovu. Ndendende basi momwe kachisi anakhalira mu chipululu, pakuti Yohane ananena ndendende ndipo anawona ndendende chinthu chomwecho chimene Mose anachiwona pamene iye anali kumtunda uko, chinthu chomwecho chimene Paulo anachiwona.

298 Ndipo tsopano ife tikuzindikira kuti maziko thwelovu anali mayina a atumwi. Ndipo zipata thwelovu zinali ndi dzina la fuko lirilonse pa chipata. Momwe ife tikuziyang’anira izo ndi kuona akulu thwelovu amenewo, mafuko thwelovu, atumwi thwelovu, maziko thwelovu, zipata thwelovu! Oh, mai! Tengani mawerengero awo a Mulungu ndipo inu simungakhoze kuziphonya izo paliponse, iye athamanga molunjika kulikonse nthawi iliyonse.

299 Ndi chifukwa chake, inu mukuona, ife tiri nawo masiku sikisi awa amene dziko lagwiramo ntchito, ndipo ife tiri pafupi

kwambiri ndi tsiku la seveni ili tsopano. Zaka thuu sauzande zoyambirira, Mulungu anawononga madzi. . . dziko ndi madzi. Zaka thuu sauzande zachiwiri, Khristu anabwera. Ino ndi 1961, pakhomu pomwe, kanthawi pang'ono. Ndipo tayang'anani, Yesu anati, "Tsopano, izo sizidzapita mtunda wautali," Iye anati, "chifukwa ndikuyenera kuyifupikitsa ntchitoyo. Ngati ine sinditero, bomba la atomiki lidzawononga mnofu wonse. Uh-huh. Chifukwa cha Osankhidwawo, ine ndidzayifupikitsa ntchitoyo mwa chilungamo. Kulidulapo ilo, gawo la nthawiyo." Mwaona, ndiye zaka sauzande za Zakachikwi, Tsiku lalikulu.

³⁰⁰ Pamene Mpingo wakhala ukugwira ntchito motsutsana ndi tchimo kwa zaka sikisi sauzande, ndipo la seveni sauzande ndi Zakachikwi. Monga Mulungu anapanga zaka sikisi sauzande kuti amange dziko, ndipo la seveni sauzande Iye anapuma ku ntchito Zake zonse. Ndipo Mpingo ukugwira ntchito motsutsana ndi tchimo kwa zaka sikisi sauzande, ndipo la seveni sauzande Mpingo ukupuma.

³⁰¹ Miinjiro yoyera yomwe inali pa akulu ndi chilungamo cha Oyeramtima. *Choyera* chimatanthauza "chilungamo." Ndipo chifukwa iwo anali *atavala miinjiro* zinasonyeza kuti iwo anali "ansembe kapena oweruza," ovala mwinjiro woyera, ansembe, oweruza, aneneri, ena otero; mwaona, chimene iwo anali. Iwo anali ovala miinjiro yoyera, akulu twente ndi foro. Padzakhala akulu twente ndi foro. Padzakhala thwelovu a iwo kwa mafuko thwelovu a Israyeli; atumwi thwelovu kwa Mpingo.

³⁰² Ndipo iwo anakhala m'mabwalo a Mfumu yayikulu. Kumbukirani, iwo akhala kunjira uko, *awa* ali. Ndipo *apa* pali Mkwatibwi ndi Khristu atakhala pa Mpandowachifumu Wake, ndipo Mkazi Wake atakhala pafupi ndi Iye, Mpingo. Akulu twente ndi foro. . . Adindo handiredi forte foro sauzande a kachisi, akumtumikira Iye. Kumene Iye adzadzuka, Mkazi Wake adzapita ndi Iye. Oh, oh mai! Kudzera mu M'badwo waukulu uwo umene ukubwera, pamene tchimo lonse ndi mawonekedwe a machimo. . .

³⁰³ Nyumba zazikulu zonse, zabwino zomwe anthu amazikonda kwambiri lero, ndalama zonse ndi kusilira ndi tchimo lonse ndi akazi okongola ndi amuna, ndi chirichonse chimene iwo amayesera kulipanga thupi lawo, chinachake kapena chinzake, kuti likhale msampha wa mdierekezi kuti atumize miyoyo yawo ku gehena, lidzawonongeka ndi kuwola, ndipo mphutsi za pakhungu zidzalidya ilo. Ndipo chinthu choyamba, mphutsi za pakhungu. . . zonse zomwe iwo anali zidzangopita mu chiphala chamoto kuti chidzabwererense osati ku chirichonse koma kugwa ndi—ndi phulusa lonse la chiphalacho.

³⁰⁴ Koma umodzi wa mmawa uwu, mzanga, umodzi wa mmawa uwu, pamene izo zonse zidzatha, iye adzaphukanso kachiwiri. Minda yokhala ndi maluwa ake oyera ndipo—ndipo

kununkhira kwa rozi kudzagwirizana ndi kuphukira kuchokera pa Mtengo wa Moyo, ndipo Khristu adzabwerera mmawa wina. Pamene mbalame zazikulu, nkhunda, zidzakakhala mu mitengo ndi kumalira, ndipo sikudzakhalanso imfa komanso chisoni. Khristu ndi Owomboledwa Ake adzabwerera ku dziko lapansi; osati anthu okalamba, koma achinyamata kwamuyaya. Achisavundi, ife tidzayima mu chifaniziro Chake, ife tidzawala kuposa dzuwa ndi nyenyezi.

Ndikupita ku Mzinda wokongolawo
 Ambuye wanga wawakonzera Ake Omwe;
 Kumene onse owomboledwa a mibadwo yonse
 Adzayimba “Ulemerero!” kuzungulira
 Mpandowachifumu Woyera.
 Nthawi zina ndimalakalaka kwathu
 Kumwamba
 Ndi ulemerero kukawona:
 Chidzakhala chimwemwe chotani pamene
 Mpulumutsi wanga ndidzawuwona,
 Mu Mzinda wokongola uja wagolide!

Momwe ine ndikukhumbira kumuwona Iye! Oh, ine ndikufuna kumuwona Iye!

Ndikupita ku Mzinda wokongola uja.

³⁰⁵ Yohane anawuwona iwo, pa chisumbu cha Patmo, ukutsika pansi ngati Mkwatibwi wokongoletsedwa kwa mwamuna wake. Ulemerero wake ine ndikufuna kuti ndidzawuwone, tsiku lina.

Ine ndikufuna kuti ndidzawuwone Iye, ndi kudzayang’ana pa nkhope Yake,
 Uko kuti ndidzayimbe za chisomo Chake chopulumutsa;
 M’misewu ya Ulemerero ndikweze liwu langa;
 Nkhawa zonse zatha, kwathu pomaliza, kuti ndikakondwere nthawi zonse.

³⁰⁶ Kuterera kwakung’ono ndi kutsetsereka mu chipale, kutentha pang’ono ndi zovutikira za tsiku; Ine ndikanakonda mkazi wanga ndi Mabel akanabwera ndi kudzandiyimbira ine nyimbo imeneyo, ngati ine—ine ndingathe, “Zovuta za paulendowu sizidzawoneka ngati kanthu, pamene ine ndidzafika kumapeto kwa njira.” Uko nkulondola.

³⁰⁷ Ine ndikukumbukira usiku pamene ndinachoka ku mpingo kuti ndikayambe ntchito yolalikira, pamene inu nonse munkalira; palibe mmodzi wa iwo amene watsalira, nkomwe, mwina wake ochepa a inu muli pano. Mlongo ndi M’bale Spencer, ndi mwina wake o—ochepa mwa akale atsalira, pamene iwo analira kuno. Koma pamene Mzimu Woyera unatero, “Iwe ukuyenera kupita!”

³⁰⁸ Ndipo ine ndikukumbukira msonkhano wanga woyamba ine nditapita kwa miyezi, Meda anabwera ku Jonesboro, Becky

anali mwana wamng'ono kwambiri, anabwera pa sitima yakale ya Cottonbelt, zinawatengera masiku kuti akafike kumeneko. Ndipo ine ndinali nditayima kunja uko pamene iye anabwera usiku umenewo. Ife tinayesetsa kuti tikafike ku holo, mtunda wa midadada itatu, apolisi anali akugwira misewu monga choncho. M'misewu munalinso anthu ambiri. Ndinali, zinanditengera ine kudutsa m'misewu ndi kukhotakhota mozungulira kuti ndikafike pa malopo. Meda anati, "Kodi iwo anabwera kudzakumva iwe ukulalikira, Bill?"

³⁰⁹ Ine ndinati, "Ayi." Kenako ife tinayimba:

Iwo amabwera kuchokera Kummawa ndi
Kumadzulo,
Iwo amabwera kuchokera ku dziko lakutali,
Kudzachita phwando ndi Mfumu yathu,
kudzadya monga mlendo Wake;
Ndi odala bwanji amyendamnjira awa!
Kuona nkhope Yake yoyera
Yowala ndi chikondi cha Umulungu;
Odala ogawana nawo chisomo Chake,
Monga ngale mu korona Wake kuti awale.
Oh, Yesu akubwera posachedwa,
Mayesero athu adzatha pamenepo.
Oh, bwanji ngati Ambuye wathu atabwera
mphindi ino
Kwa iwo ali afulu ku tchimo?
Oh, ndiye zingakubweretsereni inu
chimwemwe,
Kapena chisoni ndi kukhumudwa kwakuya?
Pamene Ambuye wathu mu ulemerero
adzadza,
Tidzakumana Naye mu mlengalenga.

³¹⁰ Ameni! Oh, ine ndimamukonda Iye! Kodi zingakubweretsereni chisoni ndi kupsinjika kwakukulu, kapena zingakubweretsereni chimwemwe? Pamene Ambuye wathu mu ulemerero abwera, tidzakumana Naye mu mlengalenga. Ndi maganizo amenewo m'malingaliro athu, tiyeni tiweramitse mitu yathu. Ambuye akalola, ine ndidzamalizitsa ulaliki uwu nthawi ina.

³¹¹ Atate Athu Akumwamba, oh, iwo adzabwera kuchokera Kummawa ndi Kumadzulo, iwo adzabwera kuchokera ku mayiko akutali. Ine ndikuganiza za Mkwatulo waukulu umenewo. Anthu amene ndawalalikira ku Afrika, India, ndi padziko lonse lapansi, mmene ine ndidzawone nkhope zawo kachiwiri. Ambiri a iwo akulira, akupita kunja ku ndege, ndi kutsamira mipanda ndi kukuwa ndi kulira. Ine ndikuganiza pamene iwo anatuluka ndi Paulo nthawi ina, anagwada pansu ndipo anapemphera. Iye anati, "Ine ndikutsimikiza palibe

aliyense wa inu. . . ambiri a inu pano simudzawonanso nkhope yanga.”

Koma iwo adzachokera Kummawa ndi
Kumadzulo,
Iwo adzachokera kumayiko akutali,
Kudzachita phwando ndi Mfumu yathu,
kudzadya monga alendo Ake;
Ndi odala bwanji amyendamnjira awa!
Kuwona nkhope Yake yoyera (mu ulemerero
wa emerodi,)
Kuwala ndi Kuwala kwa Umulungu;

Osati kuwala kwa nyali chabe kapena kuwala kwa kandulo,
koma—koma Kuwala kwa Umulungu.

kuwala ndi Kuwala kwa Umulungu;
Odala ogawana nawo chisomo Chake,
Monga ngale mu korona Wake kuti awale.

O Mulungu!

Pamene khala la Moto linamukhudza mneneri,
Kumupanga iye wangwiro monga wangwiro
akanakhalira,
Pamene Liwu la Mulungu linati, “Adzatipitira
ife ndani?”
Ndiye iye anayankha, “Ndine pano, nditumeni
ine.”

³¹² Oh, tumizani Mngelo mmawa uno, Akerubi okhala ndi mapiko sikisi, monga Yesaya anawawonera iwo, akuwuluka kudutsa mnyumbamo, akufuula, “Woyera, woyera, woyera, kwa Ambuye.” Ndipo Yesaya mneneri wamng’onooyo anati, “Ndine wamilomo yosayera, ndi pakati pa anthu osayera, ndipo maso anga awona Ulemerero wa Ambuye.” Ziundo zinasuntha kuchoka mkachisi. Ndipo Mngelo anatenga chopanira pa guwa, ndipo anatenga khala la moto naliyika ilo pa milomo yake, nati, “Ndikuyeretsa milomo yako. Tsopano nenera, mwana wa munthu.” Tumizani Mngelo mmawa uno, Ambuye, yeretsani milomo yathu ku choyipa chirichonse. Yeretsani mitima yathu, ndipo bwerani mkati, Ambuye. Phwanyani chifuniro cha inemwini. Kuti. . . lolani chifuniro changa (mwa Inu) chikhale Chifuniro Chanu, Ambuye. Oh, funani Chifuniro Chanu mwa ine, O Mulungu. Ndipo mulole ine ndi mpingo wanga ndi anthu anga tikhale anu, O Ambuye. Ife tikudzipereka tokha kwa Inu.

³¹³ Ndipo monga wolemba ndakatulo anapitiriza kunena, Atate:

Mamiliyoni tsopano mu tchimo ndi m’manyazi
akufa,

Uko mu Afrika, kumusi mu India, kuzungulira dziko, masauzande pa ora, ndi kukumana Nanu popanda kukudziwani Inu.

Mamiliyoni tsopano ali mu tchimo ndi
m'manyazi akufa,

Komabe, Mulungu, zimang'amba moyo wanga ku zidutswa
kuganizira za izo.

Mvetserani ku kulira kwawo kwachisoni ndi
kowawa;
Fulumizitsani, m'bale, afulumizitseni kuti
mukawapululumutse;
Mwamsanga yankhani, "Ambuye, ndine pano."

³¹⁴ Perekani izi, Ambuye, perekani izo kachiwiri. Ine ndapanga
mitundu yonse ya kulakwitsa, Atate, kudutsa chaka chathachi,
ndikupemphera Inu mundikhululukire ine chifukwa cha izo.
Ndipo mu Chaka Chatsopano ichi, Ambuye, ndidzozeni ine
mwatsopano. Ndiloleni ine ndipite kwa mamiliyoni awo
akukhala kutali mu tchimo ndi m'manyazi, akufa, abweretsereni
iwo vumbulutso lalikulu ili la Choonadi Chanu, kubweretsa
kwa iwo kudzoza kwa Mzimu Woyera; kuti pa tsiku limenero
iwo adzabwere kuchokera Kummawa ndi Kumadzulo, akuwala
ngati ngale mu Korona Wanu. Ndithandizeni ine, Ambuye,
kuti nditsike ndi kuwafufuza ndi kuwafukula iwo kuchoka mu
nthaka, fumbi la dziko lapansi, litsiro ndi nyansi zomwe iwo
akukhalamo. Ndipo mulole iwo awone Mulungu Woyera amene
amawayeretsa iwo ndi kukhala monga Akhristu, oyeretsedwa
ndi angwirowo pamaso Panu; kupatuka ku zoyipa, kuchoka ku
mitundu yonse ya zosangalatsa za mdziko, ndi kutembenukira
kwa Mulungu wamoyo, ndi kuwapanga iwo nthumwi za Ufumu
Wanu kwa tsiku lalikulu ilo.

³¹⁵ Muyeretse mpingo wawung'ono uwu mmawa uno, Ambuye.
Muyeretseni munthu aliyense muno ndi Mzimu Wanu, ndipo
mulole Mzimu Woyera ubwere m'mitima yawo, aliyense wa
ife. Tsitsimutsani Mzimu mwa iwo amene. . . anatsigula mitima
yawo mwa chifuniro cha iwoeni, akana chifuniro chawo chomwe
ndipo abwera kudzadziwa Chifuniro Chanu.

³¹⁶ Ana aang'ono awo, Ambuye, ambiri a iwo ana aang'ono
chabe. Momwe Inu mumawasamalirira iwo mmanja Mwanu!
Momwe mayi amasamalirira mwana wake wamng'ono,
akupukuta misozi m'maso mwawo ndi—ndi kuwapatsa iwo
zinthu zapadera chifukwa iye amawakonda iwo. Umo ndi
momwe Inu mumawakondera makanda Anu aang'ono obadwa
kumene, Ambuye. Iwo sangathe kuyenda apobe, iwo sangathe
ngakhale kuyankhula. Chinthu chokha chimene iwo angakhoze
kuchita ndi kulira ndi kuyang'ana kwa Amayi. O Mulungu,
agwireni iwo mmanja Mwanu, mosamalitsa, ngati ana ankhusa,
ndipo atsogolereni iwo mpaka iwo atakula kuti athe kumayenda.
Ndiye atsogolereni iwo, Ambuye, kudutsa mu njira za utumiki.
Perekani izi.

³¹⁷ Mutikhululukire ife machimo athu, monga ifenso tiwakhululukira iwo amene amatichimwira. Musatitengere kokatiyesa, koma mutipulumutse kwa woyipayo. Pakuti Wanu ndi Ufumu, ndi mphamvu, ndi ulemerero, kwanthawizonse, kudzera mu Dzina la Yesu Khristu. Amen.

³¹⁸ Mulungu akudalitseni! Ine ndikudalira kuti Ambuye akuchitirani inu chinachake mmawa uno kuti akupangitseni inu kuyamba Chaka Chatsopano pa chinthu chimodzi ichi, kuti inu mumamukonda Yesu Khristu, ndipo tsiku lina inu mukufuna kudzamuona Iye ndi kudzamukonda Iye ndi kudzakhala Naye kwanthawizonse. Ndi chokhumba changa kuti pasakhale mmodzi wa inu amene adzatayike, kuti aliyense wa inu apulumutsidwe ndi kudzazidwa ndi Mzimu Woyera, ndi kusungidwa mpaka tsiku limenero la Kudza Kwake, chifukwa ine ndikukhulupirira ziri posachedwapa.

Tsopano ine ndikupereka msonkhanowu kwa M'bale Neville.



61-0101 Chibvumbulutso, Mutu Foro Gawo II
Branham Tabernacle
Jeffersonville, Indiana U.S.A.

CHICHEWA

©2024 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. Box 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.

www.branham.org